

# **KAYENDETSEDWE**

## **KA**

### **ZINTHU MALINGANA NDI BAIBULO**

#### **HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE**

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a **Harvest International Institute** ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinasandulitsa anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

## ZAMKATI MWA BUKULI

Kagwiritsidwe ntchito Ka bukuli.....	3
Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira limodzi Pagulu.....	4
Mau oyamba.....	5
Zolinga za Maphunzirowa.....	6
1. Utumiki wa kuyendetsa Zinthu.....	7
2. Mipando Yautsogoleri.....	18
3. Kudzodza kwa utsogoleri.....	30
4. Zoyenera Atsogoleri.....	42
5. Kutsogolera Monga Kapolo.....	58
6. Kutsogolera ngati m'busa.....	67
7. Ntchito za Atsogoleri.....	79
8. Kupanga zisankho.....	90
9. Mikangano komanso mwambo.....	100
10. Kuphuzitsa atsogoleri komanso aphuzitsi.....	111
11. Kukumana ndi kulephera.....	126
12. Mfundo zopambanira.....	140
13. Kuwerenga Malipiro.....	153
Zoonjezera Zapadera.....	161
Mayankho amafunso odziyesa Nokha.....	166

## **KAGWIRITSIDWE NTHCITO KA BUKULI**

### **KAKONZEDWE KA BUKULI**

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

**Zolinga:** Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Welengani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

**Vesi Yotsogololera:** Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

**Zopezeka mu Magawo:** Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

**Mayeso Odziyesa Nokha:** Osathamangira kulemamba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

**Zophunzira Zowonjezera:** Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mau Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

**Mayeso Omaliza:** Ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

### **ZOWELENGA ZINA ZOFUNIKA POHUNZIRA PHUNZIROLI**

Mudzafunikira Buku Lopatulika

## NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU

### MKUMANO WOYAMBA

**Kutsekulira:** Yambani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

**Khazikitsani Ndongomeko Zapagulu:** Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene muzikumana.

**Mayamiko ndi Matamando:** Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

**Gawani Mabuku Kwa Ophunzira:** Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

**Perekani Ntchito Yoyamba.** Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene aziphunzitsidwa pa mkumano uli wonse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

### MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO

**Kutsekulira:** Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina a ophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a ophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

**Kukumbutsira:** Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

**Phunziro:** Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphanzira komanso m'mene angagwiritsire ntchito zimene aphanzira pamoyo wawo ndi utumiki.

**Mayeso Odziyesa Nokha:** Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankho kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adzipezere okha mayankho.

**Mayeso omaliza:** Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphanzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina aliyense ali ndi buku laphunziroli.

## MAU OYAMBA

Phunziro lino likubvumbulutsa mfundo za kayendetsedwe ka zinthu molingana ndi Baibulo likufotokozero. “Kuyendetsa chinthu” ndi chimodzi modzi “kukhala mdindo.” Adindo kapena “oyang’anira” amakhala ndi ntchito yosamalira zinthu zimene zapatsidwa kwa iwo kuonesetsa kuti zikuyenda bwino. Ngati okhulupirira, ife tonse ndi adindo a zauzimu zimene Mulungu watipatsa.

Bvuto lalikulu lagona pakuti atsogoleri ambiri a Chikristu satha kuyendetsa bwino zinthu zauzimu zimenezi. Ngati ogwira ntchito m’ munda ndi ochepa ndiye kuti ochepawo akuyenera kugwira ntchito mwa dongosolo motsogozedwa ndi atsogoleri awo.

Kukula pa thupi la munthu kumachitika pamene mafupa ake akukula kuti athandize kunyamula minofu imene imakhala ikukula nthawi ndi nthawi. Chomwechonso mpingo. Kuti thupi la Khristu likakule bwino, nkofunika kukhala ndi dongosolo loyenera la kachitidwe ka zinthu. Moyo wauzimu umabweretsa kukula kwa mpingo ndipo atsogoleri akuyenera kukhala ndi kuthekera kogwirizitsa kukulako.

Phunziro lino ndi loyamba pa maphunziro atatu amene tili nawo mu gawo lotchedwa “Kukonza Zinthu” lomwe ndi gawo limodzi la maphuziro a Harvestime International. Maphunziro awiri enawo ndi “Kafukufuku wa Dera” ndi “Kuyendetsa Zinthu mwa Zolinga.” Maphunzirowa akonzedwa kuti akuthandizeni kukhala mdindo wokhulupirika pa zinthu zauzimu zimene Mulungu watipatsa. Pempho lathu ndi lakuti maphunziro atatuwa aphunziridwe motsatana ndi cholinga chakuti mumvetse bwino za utsogoleri, kukonza zilinganizo, ndi kuika zinthu m’ malo zomwe ndi zofunika kwambiri mu utumiki.

Phunziro lino likubweretsani ku mutu wa kayendetsedwe ka zinthu, kuzindikira mipando ya utsogoleri komanso kutsindika za kufunika kwa kudzodza pa utsogoleri. Tionanso za mfundo za Baibulo pa za utsogoleri wotumikira komanso tikambirana za zowayenereza atsogoleri.

Tikhala tikuona ntchito zikulu-zikulu za utsogoleri makamaka potsindika mfundo ya kupanga chiganizo ndi kuthana ndi kusiyana maganizo. Tikupatsani mndandanda wa mfundo zophunzitsira atsogoleri ndi otsatira, mfundo za kuchita bwino pautsogoleri komanso tiunguzaunguza zifukwa zimene zimabweretsa kulephera pautsogoleri.

Chigawo cha “Zowonjezera” kumapeto kwenikweni chikupatsani mwayi wophunzira mfundo zina poyang’ ana za atsogoleri otchuka m’ Baibulo, kuti mukazame m’ chidziwitso chanu pa mutu wa utsogoleri.

## ZOLINGA ZA PHUNZIRO LINO

Pamene mwamaliza phunziro lino muzitha kuchita zinthu izi:

- Kufotokozero mau oti kayendetsedwe ka zinthu
- Kuzindikira chuma chazimu chimene okhulupirira apatsidwa kuti achiyendetse ndi kuyang'anira.
- Kudziwa zomwe oyang'anira akuyenera kuchita
- Kudziwa chitsanzo chachikulu cha utsogoleri wauzimu
- Kulemba mwachidule zomwe utumiki woyendetsa zinthu umayenera kukhala nazo
- Kudziwa maudindo a utsogoleri molingana ndi Baibulo
- Kufotokozero momwe mphatso zauzimu zimayenera kugwiritsidwira ntchito.
- Kufotokozero momwe atsogoleri ayenera kugwirira ntchito limodzi
- Kudziwa kufunika kwa kudzodza pa utsogoleri wauzimu
- Kulemba mndandanda wa zowayenereza atsogoleri
- Kufotokozero momwe munthu angatsogolere anthu ngati mtumiki
- Kufotokozero momwe munthu angatsogolere anthu ngati m'busa
- Kulemba mwachidule ntchito ya atsogoleri
- Kugwiritsa ntchito mfundo za Baibulo popanga chiganizo.
- Kugwiritsa ntchito mfundo za Baibulo pothana ndi kusiyana maganizo ndi kusungitsa mwambo mu mpingo.
- Kusula atsogoleri ndi otsatira
- Kusanthutsa zolephera kukhala zopambana
- Kugwiritsa ntchito mfundo za Baibulo pa kupambana
- Kudziwa dipo lautsogoleri
- Kufotokozero yeso lenileni la utsogoleri wauzimu.

## CHAPUTALA 1 UTUMIKI WA KUYENDETSZA ZINTHU

### ZOLINGA:

Mukamaliza phunziro lino mukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kupereka tanthauzo la “kuyendetsa zinthu.”
- Kudziwa chuma chauzimu chimene okhulupirira apatsidwa kuti achiyang'anire
- Kudziwa zofunikira zenizeni za oyang'anira
- Kuzindikira chitsanzo chenicheni cha utsogoleri
- Kulemba mwachidule zinthu zomwe zimafunika mu utumiki woyendetsa zinthu.

### VESI LOTSOGOLERA

**Mauwa ali okhulupirika, ngati munthu akhumba udindo wa woyang'anira, aifuna nchito yabwino. (1 Timoteyo 3:1).**

### MAU OYAMBA

Chaputala chino chikutibweretsa ku nkhani ya utumiki wa kayendetsedwe ka zinthu. Tikakamba za kayendetsedwe ka zinthu si monga momwe dziko limayendetsera mabizinesi ake ayi. Koma tikulankhula za kuyendetsa bwino chuma chauzimu mu ntchito ya utumiki.

Mukaphunzira za utumiki wa kayendetsedwe ka zinthu, mukhala mdindo wabwino wa Uthenga Wabwino komanso utumiki umene Mulungu wakupatsani. Mutha kugwira ntchito limodzi ndi Mulungu kukwaniritsa zolinga zake.

### TANTHAUZO LA KAYENDETSSEDWE KA ZINTHU

Mau oti “kuyendetsa zinthu” amafanana ndi mau oti “kukhala mdindo.” “Adindo” kapena “oyendetsa zinthu” ndi anthu amene adaliridwa ndi zinthu zina zake ndi munthu wina. Ndipo kuyendetsa zinthu ndi ntchito yokwaniritsa zolinga ndi madongosolo a Mulungu pogwiritsa bwino ntchito anthu, katundu, ndi chuma chauzimu. Ndipo kuchita bwino pa kayendetsedwe ka zinthu kumaonekera pamene zolingazi zakwaniritsidwa. Baibulo limati:

**Tonse tasocera ngati nkhosa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa Iye mphulupulu ya ife tonse. (Yesaya 53:6).**

Monga nkhosa zimasoweka kuzitsogolera panjira yake, anthunso amasoweka utsogoleri kuti ntchito ndi mphamvu zawo zikakwaniritse zolinga ndi madongosolo a Mulungu.

## **CHUMA CHAUZIMU**

Okhulupirira onse ndi adindo a chuma chauzimu chimene Mulungu adawapatsa. Izi ziri m'chigawo cha “Kupitiriza Kuphunzira” kumapeto kwa chaputala chino. Kuonjezera pa chuma chimenechi, atsogoleri ndi adindo a chuma chapaderadera monga:

**Uthenga Wabwino:** Tikuyenera kugawana ndi ena Uthenga Wabwino.

**Ndalama:** Wokhulupirira wina aliyense ndi mdindo wa ndalama zake, ndipo iwo amene akuyang'anira mpingo kapena mabungwe a Chikhristu ndi adindonso a chuma cha magulu amenewa.

**Katundu wogwiritsa ntchito mu utumiki:** Izi ndi monga malo, nyumba kapena zipangizo za mpingo.

**Mphatso zauzimu:** Wokhulupirira wina aliyense ali ndi mphatso ina yake imene Mulungu anampatsa ndipo amakhala mdindo wa mphatso imeneyo. Mtsogoleri amakhalanso ndi udindo wothandizira okhupulupirira kukula m'mphatso zawo zauzimu.

**Okhulupirira ena:** Ngati ndinu mtsogoleri, muli ndi udindo pa anthu ena. Mukuyenera kuwathandiza kuti akule muuzimu ndipo kuti azitenga nawo mbali mu ntchito ya utumiki. Mulungu amagwiritsa ntchito anthu kumanga Ufumu wake osati zilinganizo. Ndipo kuyendetsa zinthu tikunenaku ndiko kuchita zinthu mu Ufumu wa Mulungu kudzera mwa anthu.

## **UTHENGA WOYAMBA WA KAYENDETSSEDWE KA ZINTHU**

Uthenga woyamba wa Mulungu kwa munthuu unali wokhuza kuyendetsa bwino zinthu.

Mulungu anauza Adamu ndi Hava kuti:

**Mulungu ndipo anadalitsa iwo, ndipo adati kwa iwo, Mubalane, mucuruke, mudzaze dziko lapansi, muligonjetse: mulamulire pa nsomba za m'nyanja, ndi pa mbalame za m'mlengalenga, ndi pa zamoyo zonse zakukwawa pa dziko lapansi.**

**(Genesisi 1:28)**

Ntchito zitatu zikuluzikulu za oyang'anira zikuoneka mu vesi imeneyi:

1. Kuchulukitsa zinthu kuti zikakwaniritse zolinga za Mulungu
2. Kuchepetsa chisokonezo pakugonjetsa
3. Kukhazikitsa bata polamulira



## **CHITSANZO CHACHIKULU**

Chitsanzo chachikulu cha utsogoleri ndi Ambuye Yesu Khristu. Atsogoleri onse a Chikristu akuyenera kutsanzira Iye. Muphunzira za momwe anaonetsera chitsanzo chotsogolera ngati mtumiki komanso ngati m'busa.

Mfundo zonse zomwe ziri m'phunziro lino zinaonetseredwa kudzera mu zimene Yesu anaphunzitsa komanso kuchita. Chiri chonse chomwe munthu angayembekezere kuchipeza mwa mtsogoleri chinaonekera mwa Khristu Yesu. Ntchito iri yonse yomwe mtsogoleri amayenera kuchita inaonekera mwa Yesu. Anaonetseranso chitsanzo cha kusula atsogoleri ndi kuphunzitsa otsatira.

## **CHOFUNIKIRA CHACHIKULU**

Pamaso pa Mulungu, mdindo sakhala wopambana chifukwa cha maphunziro, luso, kapena makhalidwe okoma. Amakhala wopambana chifukwa cha kukhulupirika kwao. Chofunikira chachikulu pa mtsogoleri ndicho kuti akhale wokhulupirika:

**Komatu pano pafunika za adindo, kuti munthu akhale wokhulupirika. (1 Akorinto 4:2)**

Yesu ananena fanizo mu Mateyu 25:14-30 la antchito omwe mbuye wao anawapatsa chuma chotchedwa “matalente” ndipo zinali ndalama. Anayembekezera kuti akhale adindo okhulupirika ndi kugwiritsa ntchito chumacho moyenera. Iwo amene anachita bwino anatchedwa “okhulupirika” ndipo anapatsa mphoto. Koma amene sanachite bwino anaweruzidwa nalandira chilango.

## **UTUMIKI WOYENDETSA BWINO ZINTHU**

Mu utumikiwu muli kutsogolera ena kuti akachitire Mulungu zinthu zodabwitsa. Pali zinthu zingapo zimene muphunziro zomwe zimapezeka m'kuyendetsa bwino zinthu. Zinthuzo nazi: **Kudzindikira kufunika kwa kudzodza kwa utsogoleri:** Kudzodza kwa Mulungu pa utsogoleri ndi kofunika kwambiri kuposa maphunziro, luso, kapena kudziwa zinthu.

**Kukwaniritsa zowayenera za utsogoleri:** Utumiki woyendetsa bwino zinthu umayamba ndi kukwanitsa kudzitsogolera wekha munthu.

Kuphunzira kutsogolera ngati mtumiki: Utsogoleri wauzimu siwongofuna kukopa anthu kapena kutchuka ayi. Ndi utumiki wotumikira anthu modzichepetsa. Kutumikiraku ndi komwe kumasiyanitsa utsogoleri wauzimu ndi utsogoleri wa kudziko.

Kuphunzira kutsogolera ngati m'busa: Zinthu zomwe m'busa wa nkhusa amachita ndi zomwe Yesu akugwiritsa ntchito pofuna kufotokozera za ubusa wauzimu.

Kumvetsa ntchito za atsogoleri: Izi ndi monga kupanga ziganizo, kuthetsa kusemphana maganizo ndi kukonza zinthu.

Kuphunzitsa atsogoleri ndi otsatira: Tonse timatsogolera m'magawo osiyanasiyana, koma wina aliyense ndi wotsatira penapake. Atsogoleri akuyenera kukhala ndi otsatira. Atsogoleri ndi otsatira omwe akuyenera kuphunzitsidwa.

Kugwiritsa ntchito mfundo za kupambana zomwe ziri m'Baibulo: Mfundo izi zikuthandizani kupambana pakuyendetsa bwino chuma chazimu.

Kupewa zinthu zopunthwitsa pa utsogoleri: Kulephera pa utsogoleri kapena pakutsatira kumachitika chifukwa cha kuphwanya mfundo za m'Mau a Mulungu.

Kumvetsa mfundo za kukonza zinthu molingana ndi Mau a Mulungu: Izi zikuphatikizapo maudindo omwe anakhazikitsidwa ndi Mulungu komanso amene anakhazikitsidwa powona zosowa za mu mpingo.

### **TSINDE LA KUKONZA ZINTHU MOLINGANA NDI BAIBULO**

Kukonza zinthu mu utumiki si nkhusi yomwe inangokhazikitsidwa mwa mfundo za dziko lapansi kapena yosasinthika. Kukonza zinthu mu utumiki ndi komasuka kupereka danga kwa Mzimu Woyera kuti atenge gawo lalikuru. Ndipo cholinga chake ndi kukwaniritsa zolinga ndi madongosolo a Mulungu, osati kumanga maufumu a dziko lapansi. Kukonza zinthu mu utumiki kuli ngati chinthu chamoyo pakokha. Baibulo limayerekeza mpingo ndi thupi la munthu lomwe liri ndi magawo osiyanasiyana koma ogwira ntchito limodzi.

Mu dongosolo ili munthu sachita kusankhidwa pa udindo. Mutha kusankhidwa ndi anthu kuti mukhale pa mpando, koma sizingakupangeni kukhala mtsogoleri. Mukuyenera kuchita kuitanidwa ndi kuphunzitsika ndi Mulungu kuti mukagwire ntchito ya mu Ufumu wa Mulungu. Utsogoleri umayenera kukhala ndi udindo, mwachitsanzo, udindo ngati mtumwi, mneneri, mlaliki, m'busa, ndi mphunzitsi. Utsogoleri umayeneranso kukhala ndi ntchito. Ndipo ntchito yake yaikulu ndiyo kukonzekeretsa ena ku ntchito ya utumiki. Utsogoleri umakhuzanso ubale wa pakati pa atsogoleri ndi anthu owatsatira.

Kusankhidwa ndi kukwezedwa ngati mtsogoleri kumachokera kwa Mulungu:

**Pakuti kukuzaku sikucokera kum'mawa, Kapena kumadzulo, kapena kucipululu,  
Pakuti Mulungu ndiye woweruza; Acepsa wina, nakuza wina. (Masalimo 75:6-7)**

## **MAGAWO ENA A KAYENDETSEDWE KA ZINTHU**

Kuyendetsa bwino zinthu kumakhuzanso kauniuni wa utumiki wa munthu kuti mukhazikitse zolinga ndi madongosolo. Mutha kuphunzira luso limeneli mu phunziro la Harvestime International lotchedwa, “*Kauniuni wa Dera.*” Mu kuyendetsa bwino zinthu mumapezekanso zinthu ziri m’musizi zomwensho zimapezekanso mu phunziro la Harvestime International lotchedwa, “*Kuyendetsa Zinthu mwa Zolinga*”:

**Kukonza cholinga cha utumiki mogwirizana ndi cholinga cha Mulungu:** Ngati mulibe cholinga kapena masomphenya, simungatsogolere ena.

**Kukonza madongosolo okwaniritsira cholingacho:** Simungathe kukwaniritsa cholinga chanu ngati mulibe dongosolo loti mulitsate.

**Kuika anthu ndi zinthu zina m’ malo mwake ndi cholinga kuti mukakwaniritse cholingacho:** Kuyendetsa bwino zinthu kumakhuzanso kulimbikitsa ndi kuyang’anira anthu pamene akukwaniritsa cholinga chomwensho chikugwirizana ndi zolinga za Mulungu. Kuunika dongosolo lanu ngati likuthandiza: Ntchito ya Mulungu ikuyenera kuchitika mwapamwamba.

## **UBWINO WOYENDETSZA ZINTHU MOYENERA**

Izi ndi zina mwa zifukwa zomwe kuyendetsa bwino zinthu mu utumiki nkofunika:

### **MUMAPEREKA CHOLINGA NDI KUDZIWA KOMWE MUKUPITA**

Ngati mukufuna kupambana mu utumiki, mukuyenera kukhala ndi cholinga komanso madongosolo omwe ndi ogwirizana ndi a Mulungu ndipo kuti muwafotokozere anthu omwe mukugwira nawo ntchito. Mukadziwa cholinga chanu mu utumiki ndi kuika zinthu m’ malo kuti muwakwaniritse, mutha kutsogolera anthu. Atsogoleri amayenera kudziwa komwe akupita kuti akwanitse kutsogolera ena. Kutsogolera anthu mu umodzi pa utumiki kumakhala kosavuta ngati mtsogolori ali ndi cholinga komanso akudziwa komwe akupita.

### **KUMATHETSA CHISOKONEZO**

Pamene pali masomphenya, chimpwirikiti sichikhalapo:

**pakuti Mulungu sali Mulungu wa cisokonezo koma wa mtendere; monga mwa Mipingo yonse ya oyera mtima. (1 Akorinto 14:33)**

**Cifukwa cace khalani akutsanza a Mulungu, monga ana okonedwa; (Aefeso 5:1)**

Monga taonera mu ndimezi, ngati Mulungu siwachisokonezo, ntchito yake sikuyenera kuchitika mwa chisokonezo.

## **KUMATHANDIZA PA KAPANGIDWE KA ZIGANIZO ZOYENERA**

Ziganizo zimakhala ndi mphamvu pa tsogolo la munthu. Izi ziri chimodzimodzi ngakhale pa chipulumutso. Mumapanga chiganizo cholandira kapena kukana Uthenga Wabwino ndipo zimenezi zimanena momwe tsogolo lanu lidzakhalire kumwamba.

M'mene moyo kapena utumiki wanu uliri lero, ukuonetsera ziganizo zimene mumapanga m'mbuyomu. Mwina mumatenga nthawi kukhala pansi ndi kuganiza mozama kapena ayi mumangodzukapo basi nkupanga chiganizo pompopompo. Kuyendetsa bwino zinthu kumapangitsa kuti munthu azipanga ziganizo ndi chitsogozo cha Ambuye.

## **KUMAKHAZIKITSA ZINTHU ZOFUNIKIRA KWAMBIRI KUCHITIKA MU UTUMIKI**

Pali zinthu zina zomwe ndi zofunika kwambiri kuposa zina. Zofunika kwambiri zimayenera kutenga nthawi yanu yambiri komanso chidwi chanu chachikukulu. Munthu aliyense amakhala nazo zinthu zofunika kwambirizi. Mukuyenera kudziwa zinthu zofunika kwambiri pa moyo wanu. Kaya muchita kukhala pansi ndikuzikonza, kaya mukakamizika ndi zochitika kapena anthu okuzungulirani, kaya mupanga motsogozedwa ndi zolinga za Mulungu, koma mukuyenera kukhala nazo.

## **KUMAKUPATSANI CHOCHITA OSATI KUMACHITA ZINTHU POPEZA PALI VUTO**

Ma utumiki ambiri atanganidwa ndi kuthana ndi mavuto omwe adzuka m'malo mokhala pansi ndikuika zinthu m'malo mwake kuti ngakhale mavutowo asabwere nkomwe. Mukatero mugwira ntchito mwa nzeru komanso motsata zolinga zomwe ziripo.

Popanda dongosolo, simungathe kudziwa choyenera kuchita mu utumiki ndi momwe mungachitire. Popeza kuti mulibe dongosolo la kachitidwe ka zinthu, mumasowa chochita, simungathe kuunika kachitidwe kanu mu utumiki, komanso mumatha kutengeka ndi zinthu wamba, komanso simuchedwa kukweza manja pamene mwakumana ndi zovuta.

Kuyendetsa bwino zinthu kumasandutsa zokhumba kukhala zochitika komanso masomphenya kukhala zooneka ndi maso. Kumakuthandizani kudziwa choyenera kuchita ndi momwe mungachitire kuti mukakwaniritse zolinga za Mulungu.

## **KUMATHANDIZA KUTI MUZICHITA ZINTHU MOWONEKERA**

Mu fanizo la matalente pa Mateyu 25:14-30 akapolo aja amayenera kufotokoza bwino momwe agwiritsira ntchito zinthu zomwe anapatsidwa. Mbuye wao anali dongosolo, nawafotokoza

antchito ake ndipo amayenera kukwaniritsa cholingacho pochita malonda ndi chuma chomwe anapatsidwa.

Mulungu adzafuna kuti mukafotokoze momwe munagwiritsira ntchito chifuniro cha Mulungu pa moyo ndi pa utumiki wanu.

**Ndipo 4 kapolo uyo, wodziwa cifuniro ca mbuye wace, ndipo sanakonza, ndi kusacita zonga za cifuniro caceco, adzakwapulidwa mikwapulo yambiri. (Luka 12:47)**

Ngati simuchita mwa nzeru pa utumiki womwe munapatsidwa, mudzayankha pamaso pa Mulungu.

#### **KUMAKULOLANI KUTI MUUNIKE ZOMWE MUKUCHITA**

Kayendetsedwe kabwino kazinthu kamafunikanso kukhala panso ndi kuunika zomwe mukuchita kuti muone ngati mukukwaniritsa zolinga ndi zilanganizo za Mulungu. Kumvetsa bwino mfundo za kupambana kapena zifukwa zolepherera mu utsogoleri kumakulolani kuti muchite kauniuni ameneyu.

#### **KUMAKULOLANI KUTI MUGWIRITSE NTCHITO CHUMA CHA UZIMU**

##### **MWANZERU**

Kuyendetsa bwino zinthu kumathandiza kuti mugwiritse bwino ntchito chuma chauzimu zomwe zimudzakuonetsa kukhala mdindo wabwino wa ndalama, katundu, anthu, komanso mphatso zauzimu mu ntchito ya Mulungu.

#### **KUMAKUKONZEKERETSANI KULOWA ZIPATA ZOTSEGUKA**

**Pakuti panditsegukira pa khomo lalikuru ndi locititsa, ndipo oletsana nafe ndi ambiri. (1 Akorinto 16:9)**

Mulungu akatsegula makomo, mukuyenera kukhala wokonzeka kulowamo ndi kukumana ndi zotchinga zatsopano. Izi zimakhala zotsatheka ngati palibe kukonzekera koyenera. Werengani fanizo la anamwali khumi asanu ochenjera ndi asanu opusa pa Mateyu 25:1-13. Mulungu amatsegula zitseko, koma sizikhala zotseguka mpaka kalekale. Zikatseguka zimadikira kuti mulowe. Kenako zimatsekeka ndipo nthawi zambiri sizimatsegukanso.

#### **KUMAYANJANITSA UTUMIKI NDI CHIFUNIRO CHA MULUNGU**

Funso loyamba la Paulo Mtumwi atangotembenuka kumene mtima linali lakuti, “Mukufuna ndichite chiyani?” Munjira ina Paulo amafunsa kuti, “Dongosolo lanu pa moyo ndi utumiki

wanga ndi lotani?” Kukhala mdindo wanzeru ndiko kuika dongosolo la moyo ndi utumiki wako molingana ndi madongosolo a Mulungu ndi zolinga zake.

### **MULUNGU AKUFUNA ATSOGOLERI**

Mulungu anauza Mfumu Sauli:

**Koma tsopano ufumu wanu sudzakhala cikhalire; Yehova wadzifunira munthu wa pamtima pace; ndipo Yehova wamuika iye akhale mtsogoleri wa anthu ace, cifukwa inu simunasunga cimene Yehova anakulamulirani. (1 Samuel 13:14)**

Mulungu akufunafunabe anthu oti awagwiritse ntchito ngati atsogoleri:

**Ndipo ndinafunafuna munthu pakati pao wakumanganso linga, ndi kuimira dziko popasukira pamaso panga, kuti ndisaliononge; koma ndinapeza palibe. (Ezekiel 22:30).**

**maso a Yehova ayang'ana uko ndi uko m'dziko lonse lapansi, kudzionetsera wamphamvu kwa iwo amene mtima wao uli wangwiro ndi Iye. Mwacita copusa m'menemo; pakuti kuyambira tsopano mudzaona nkhondo. (2 Mbiri 16:9)**

Kuchita bwino mukayendetsedwe koyenera ka zinthu kumatenga nthawi yaitali komanso kumafunika khama:

**nchito ya yense idzaonetsedwa; pakuti tsikulo lidzaisonyeza, cifukwa kuti yabvumbuluka m'moto; ndipo mota wokha udzayesera nchito ya yense ikhala yotani. (1 Akorinto 3:13)**

Mitengo, maudzu ndi ziputu zimakhala pantunda. Zimapezeka mosavuta popeza zimakhala poyerayera koma sizichedwa kuonongeka. Golidi ndi siliva ndi miyala ya mtengo wapatali yomwe imapezeka pansu pa nthaka. Sizimapezeka kapena kuoneka wamba ndipo zimakhala nthawi yaitali. Utsogoleri wodzipopa ndi kukhumba kuchuka uli monga mitengo, udzu ndi ziputu. Ndi maluso ongoonekera poyera kwa anthu ndipo amapangidwa mosavuta kuchokera ku luso lachibadwa. Koma utsogoleri wa Umulungu uli monga golidi ndi siliva. Zimapangidwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera mwa obisika wamkatiyo. Ndi chuma chokoma komanso cha mtengo wapatali.

## MAFUNSO ODZIFUNSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osonera.

---

---

2. Perekani tanthauzo la mau oti, “kuyendetsa bwino zinthu”

---

---

3. Lembani mndandanda wa chuma chauzimu chomwe okhulupirira aikidwa kukhala adindo.

---

---

---

4. Kodi chofunika chachikulu kwa adindo ndi chotani?

---

---

5. Kodi chitsanzo chachikulu cha utsogoleri ndi ndani?

---

6. Molingana ndi kukambirana komwe kwachitika m’phunziro lino, lembani mwachidule zomwe ziri mu “utumiki woyendetsa bwino zinthu.”

---

---

7. Kodi kufunika kwa kuyendetsa bwino kwa zinthu nkotani?

---

---

## KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

1. Yesu anaphunzitsa zambiri za kukhala mdindo wabwino pa chuma kuposa zomwe anaphunzitsa pa kumwamba, ku gahena kapena chipulumutso. Pa mafanizo 40, 19 ndi zokhuza chuma.
2. Utsogoleri ndi udindo waukulu popeza ukukhuza kuyang'anira anthu ena. Mwa chitsanzo, m'mene Peturo anati, "Ndikupita kokasodza", anthu omwe anali naye mwamsanga anati, "Ifenso tipitana nawe limodzi." Utsogoleri ndi wofunikanso popeza mtsogoleri ndi mthenga wa Mulungu. Onani Malaki 2:7.
3. Yerekezani kufanana kwa utsogoleri woyendetsa zinthu bwino kwauzimu ndi kwadziko. Mkuyendetsa zinthu kwa kudziko, mphamvu zimagonera pa luso, kuthekera ndi chidziwitso. Koma kuyendetsa zinthu kwauzimu, kusankha atsogoleri kumagonera pa kudzodza, maitanidwe ndi bvumbulutso la chidziwitso cha Mulungu. Mkuyendetsa zinthu kwadziko, maphunziro amakhazikika pa luso ndi chidziwitso. Pamene kuuzimu maphunziro amakhazikika pa chikhalidwe molingana ndi Mau a Mulungu pamodzi ndi luso.
4. Mulungu amagwira ntchito limodzi ndi iwo amene amayendetsa utumiki. Paulo anati: (1 Akorinto 3:5-6)
5. Kusiyana zinthu zomwe utsogoleri wa dziko ndi wauzimu umatsindika:

Kuyendetsa zinthu kwa dziko	Kuyendetsa zinthu kwauzimu
Ndalama	Utumiki
Kuchita zinthu	Pemphero
Zooneka	Chikhulupiriro
Ukadaulo	Kudzodza
Malamulo	Chikondi
Luso	Mau a Mulungu
Machitidwe okopa	Chikhalidwe
Nzeru	Moyo wauzimu
Kulamulira anthu moipa	Kutsogolera
Ntchito	Maubale
Kutsimikizika kwa munthu	Kumvera
Mpikisano	Kugwira ntchito limodzi



6. Santhulani mndandanda wa maudindo a kayendetsedwe ka zinthu kwa okhulupirira kuli m'musiku. Tili ndi udindo pa:
- |                            |                           |
|----------------------------|---------------------------|
| a. Chilengedwe cha Mulungu | Genesis 1:26-28           |
| b. Zinsinsi za Mulungu     | 1 Akorinto 4:1            |
| c. Uthenga Wabwino         | 1 Atesalonika 2:4         |
| d. Mphatso zauzimu         | 1 Petro 4:10              |
| e. Chikhululukiro          | Mateyu 6:12; 18:21-22     |
| f. Chikondi                | 1 Yohane 4:7-8            |
| g. Maganizo                | Afilipi 4:8               |
| h. Mphamvu                 | Machitidwe 1:8            |
| i. Nthawi                  | Aefeso 5:15-16            |
| j. Kaonedwe ka zinthu      | 1 Samuel 16:7             |
| k. Kaonedwe ka zinthu      | Afilipi 2:2               |
| l. Chikhulupiriro          | James 2:14-17             |
| m. Ndalama                 | 2 Akorinto 9:6-11         |
| n. Matamando               | Ahebri 12:15-16           |
| o. Utumiki                 | Agalatiya 6:2             |
| p. Thupi                   | Aroma 12:1                |
| q. Chikhalidwe             | Tito 1:7-9                |
| r. Banja                   | 1 Timoteyo 3:4-5, 12; 5:8 |

## **CHAPUTALA 2**

### **MIPANDO YA UTSOGOLERI**

#### **ZOLINGA**

Mukamaliza chaputala chino mukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kudziwa mipando yapadera ya utsogoleri mu utumiki
- Kufotokozera momwe atsogoleriwa amagwirira ntchito limodzi mu utumiki
- Kufotokozera momwe mphatso zauzimu zimagwirira ntchito mu utsogoleri
- Kupeza mipando ina ya utsogoleri m’Baibulo

#### **VESI LOTSOGOLERA**

**Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; (Aefeso 4:11)**

#### **MAU OYAMBA**

Mpingo ndi chipangizo chimene Mulungu akugwiritsa ntchito tsopano lino kudzimbulutsa yekha ku dziko lapansi. M’phunziro lino muphunzira za atsogoleri omwe aikidwa mu mpingo ndi Mulungu. Muphunziranso za mipando ina ya maudindo yomwe yadzuka chifukwa cha zosowa zina ndi zina za pa mpingo.

Baibulo limapereka zoyenerereza zapaderadera zomwe anthu amene akutenga mipando ya utsogoleri akhale nazo. Muphunzira zambiri za zoyenerereza zimenezi mu Chaputala 4.

#### **MIPANDO YAPADERA YA UTSOGOLERI**

##### **MIPANDO:**

Baibulo limafotokozera za mipando isanu ya utsogoleri yomwe yaikidwa ndi Mulungu mu mpingo:

**Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; (Aefeso 4:11)**

Mipando ya utsogoleri iyi yaikidwa ndi Mulungu mu mpingo. Zimakhala ndi maitanidwe a padera mu mpingo komanso mphatso zauzimu zapadera. Simukuyenera kugwira ntchito m’ mipando imeneyi popeza kuti mwafuna kapena wina wakuuzani kuti mutero ayi. Mukuyenera kukhala kuti mwaitanidwa ndi Mulungu ndipo wakupatsani mphatso zauzimu kuti muthe kutero.

## **NTCHITO YA MIPANDO IMENEYI**

Mwachidule ntchito za mipando ya utsogoleri imeneyi nayi:

**Mtumwi:** Mtumwi ndi munthu amene ali ndi kuthekera kwapadera koyambitsa mipingo yatsopano malo osiyanasiyana ndi kuyang'anira mipingo ingapo ngati wamkulu. Mau oti "mtumwi" amatanthauza "nthumwi, munthu wotumidwa ndi mphamvu ndi ulamuliro wonse kukagwira ntchito m'malo mwa wina." Mtumwi amakhala ndi ulamuliro kapena mphamvu zapadera zokafalitsa Uthenga Wabwino padziko lapansi pokhazikitsa magulu a okhulupirira mwa dongosolo. Mau ena omwe tingawiritse ntchito lero ndi akuti "mishonale" kapena "wobzala mipingo." Mtumwi Paulo ndi chitsanzo chabwino cha utumiki wa utumwi.

**Mneneri:** Mneneri ndi munthu amene amalankhula mau owuziridwa ndi Mulungu mwa chindunji ndipo ali ndi udindo waulamuliro mu mpingo. Iye amakhala ndi udindo wolandira ndi kulankhula uthenga wa pompopompo wa Mulungu kwa anthu ake mwa malankhule odzodzedwa ndi Ambuye. Agabo ndi chitsanzo chabwino cha m'Chipangano Chatsopano. Onani Machitidwe 21:11

**Mlaliki:** Mlaliki amakhala ndi kuthekera kwapadera kogawa Uthenga Wabwino kwa anthu osakhulupirira mu njira yoti amatembenuka mtima nabwera kwa Ambuye ndi kukhala ziwalo zodalirika za Thupi la Khristu. Tanthauzo la mau oti "mlaliki" ndi lakuti, "iye amene abwera ndi uthenga wabwino." Philipo ndi chitsanzo chabwino cha mlaliki. Onani Machitidwe 21:8 and Machitidwe 8.

**M'busa:** Azibusa ndi anthu amene amadzipereka kutenga udindo wosamalira gulu la anthu otembenuka mtima kwa nthawi yaitali.

**Aphunzitsi:** Aphunzitsi ndi okhulupirira omwe ali ndi kuthekera kwapadera kophunzitsa Mau a Mulungu mu njira yakuti anthu ena amaphuzitsika ndi kugwiritsa ntchito zomwe aphunzirazo.


## **CHOLINGA CHAO**

Mipando iyi inakhazikitsidwa kuti ikakwaniritse zolinga zotsatirazi:

**kuti akonzere ojera mtima: ku nchito ya utumiki, kumangirira thupi la Kristu; kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa cikhulupiriro, ndi wa cizindikiritso ca Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro, ku muyeso wa msinkhu wa cidzaloca Kristu. Kuti tisakhalenso makanda, ogwedezekagwedezeka, natengeka-tengeka ndi mphepo yonse ya ciphunzitsa, ndi tsenga la anthu, ndi kucenjerera kukatsata**

**cinyengo ca kusoceretsa; koma ndi kucita zooni mwa cikondi tikakule m'zinthu zonse, kufikira iye amene ali mutu ndiye Kristu; (Aefeso 4:12-15)**

Chithunzi choonetsi zolinga za Utimikisi



Zosatira ndi zakuti pamakhala umodzi wa ziwaloni zonse za thupi mwachikondi.

**MOMWE AMAGWIRIRA NTCHITO LIMODZI**

Mautumiki a utsogoleri asanu amenewa amagwira ntchito limodzi mu mpingo motere.

**Mtumwi:** Amatengera Uthenga Wabwino ku dera latsopano ndi kukhazikitsa mpingo.

**Mlaliki:** Amalalikirira Uthenga Wabwino mu njira yakuti anthu osakhulupirira amatembenuka mtima nakhala mbali imodzi ya mpingo.

**Mneneri:** Amapereka uthenga wapaderadera kuchokera kwa Mulungu kupita ku mpingo motsogozedwa ndi Mzimu Woyera.

**Aphunzitsi:** Amapereka upangiri wa m’Mau womwe umadutsa pa kulalikira Uthenga Wabwino kwa mlaliki. Amathandiza anthu otembenuka mtima kumene kuti akule muuzimu ndi kuwaphunzitsa kukhala anthu okhulupirika omwe amakaphunzitsanso ena.

**Abusa:** Amatenga udindo wosamalira okhulupirira kwa nthawi yaitali.

### **MPHATSO ZAUZIMU MU UTSOGOLERI**

Mphatso zapadera za utsogoleri zisanu zomwe taonazi, si maudindo okhawo amene ali mu mpingo.

**Koma tsopano, Mulungu anaika ziwalo zonsezo m'thupi, monga anafuna. (1 Akorinto 12:18)**

Tatchula kale mphatso zapadera za utsogoleri monga mtumwi, mneneri, mlaliki, m’busa, ndi mphuzitsi. Apa tiona mndandanda wa mphatso zina zomwe Mzimu Woyera amapereka kwa okhulupirira:

Mphatso zolankhula: Uneneri, kuphunzitsa, kulimbikitsa, mau a nzeru, ndi mau a chidziwitso. Mphatso zotumikira: Kutumikira, kuthandiza, utsogoleri, kayendetsedwe ka zinthu, kupereka, kuchita chifundo, kuzindikira mizimu, ndi kuchereza alendo.

Mphatso za zizindikiro: Malilime, kutanthauzira malilime, zozizwa, ndi machiritso.

Mavesi omwe amatchula za mphatso zomwe tatchulazi ndi awa:

- **Aroma 12:1-8**
- **1 Akorinto 12:1-31**
- **Aefeso 4:1-16**
- **1 Petro 4:7-11**

(Maphunziro a Harvestime International Institute ali ndi phunziro lotchedwa, “Utumiki wa Mzimu Woyera” lomwe limafotokoza tsatanetsatane wa mphatso za Mzimu Woyera komanso momwe tingadziwire mphatso za Mzimu Woyera zathu).

### **MPHATSO ZOFUNIKIRA KWA OYENDE TSA ZINTHU**

Kwa iwo omwe ndi oyendetsa zinthu, pali mphatso ziwiri zauzimu zomwe ndizofunikira kwambiri: mphatso ya kutsogolera (kuweruza) ndi mphatso yoyang’anira (maweruziro).

Mphatso ya utsogoleri imapezeka pa Aroma 12:8. Munthu wokhala ndi mphatso ya utsogoleri amakwanitsa kukhazikitsa madongosolo omwe ndi ogwirizana ndi zolinga za Mulungu ndi

kufotokozerana ena momveka bwino madongosolowo. Amathanso kumema anthu kuti akakwaniritse masomphenya amenewa kuti Mulungu akalemekezeke.

Mu 1 Akorinto 12:28 muli mphatso yotchedwa “maweruziro” yomwe ndi yoyang’anira. Munthu wokhala ndi mphatso imeneyi amatha kupereka upangiri, kuika zinthu m’ malo, komanso kupanga ziganizo m’ malo mwa anthu ena. Ziri ngati munthu amene amayendetsa chingalawa. Ameneyenera kutenga udindo wopanga ziganizo zomwe zimathandizira ulendo ukhale wabwino ngakhale chigalawacho sichake.

Tito ndi chitsanzo chabwino cha munthu wokhala ndi mphatso ya kuyang’anira. Mtumwi Paulo anayambitsa mpingo ku Krete. Amene amayendetsa mpingo umenewu ndi Tito.

**kwa Tito, mwana wanga weni weni monga mwa cikhulupiriro ca ife tonse: Cisomo ndi mtendere za kwa Mulungu Atate ndi Kristu Yesu Mpulumutsi wathu. Cifukwa ca ici ndinakusiya iwe m'Krete, kuti ukalongosole zosowa, nukaike akuru m'midzi yonse, monga ndinakulamulira; (Tito 1:4-5)**

Mphatso ziwirizi zimagwira ntchito limodzi. Munthu wokhala ndi mphatso ya utsogoleri amakhala ndi kuthekera komema anthu ndi kugwira nawo ntchito bwino kukwaniritisa masomphenya. Pamene wokhala ndi mphatso yoyang’anira amaonesetsa kuti zinthu ziri m’ malo mwake popereka upangiri wa momwe zinthu zikhaliro popanga ziganizo zoyenera.

### **WINA ALIYENSE ANGATHE KUTUMIKIRA**

Nkhani yotsogolera si ya okhawo omwe ali ndi mphatso ziwirizi kapena omwe ali ndi mphatso zisanu zija ayi. Okhulupirira okhala ndi mphatso zina atha kufunsidwa kuti atumikire m’ magawo osiyana-siyana.

Mwachitsanzo munthu wokhala ndi mphatso yopereka atha kusankhidwa udindo wotsogolera gulu loyendetsa chuma cha mpingo. Munthu wokhala ndi mphatso ya machiritso atha kufunsidwa kutsogolera gulu la anthu otumikira pakati pa odwala ngakhale m’ chipatala.

Mphatsozi zimapereka mwayi waukulu wa utsogoleri mu utumiki. Ngakhale munthu amene alibe mphatso yautsogoleri, koma ngati ali ndi chidwi ndi mphatso yake atha kukhala mtsogoleri m’ gawo lakelo.

### **MAUDINDO ENA A M’BAIBULO**

Palinso maudindo ena omwe ali m’ Baibulo omwe simphatso zauzimu. Ndi mipando yomwe inakhazikitsidwa mu mpingo poona zosowa zina zomwe mpingo uli nazo. Maudindo monga atumiki, akulu ampingo, ndi oyang’anira atchulidwa mu Chipangano Chatsopano.

Zolembedwa za m'Chipangano Chatsopano zinasungidwa ndi Mulungu kuti zikhale chitsanzo chathu pa momwe tingayendetsere mpingo lero. Ndipo maudindo amenewa akuyenera akhale akugwira ntchito mu mpingo lero. Cholinga cha maudindo ngati amenewa ndi kuthandizira iwo amene ali ndi mautumiki monga atumwi, aneneri, alaliki, abusa, aphunzitsi, ndi ena amene ali ndi mphatso ya kutsogolera komanso kuyang'anira. Gwiritsani ntchito mlozo wotsatirawu kuti muphunzire zambiri za maudindowa:

<b>UDINDO</b>	<b>NDIME</b>	<b>NTCHITO</b>
Woyang'anira	1 Timothy 3:1-7 Philippians 1:1 Titus 1:5-9 I Peter 5:2-3	Anthu ambiri amaganiza kuti udindo woyang'anira ndi yofanna ndi yaubusa. Woyanganira amakhala nthawi yaitali pa ntchitoyi
Atumiki aamuna	1 Timoteyo 3:8-13 Afilipi 1:1 Machitidwe 6:1-7	Ndime zimenezi zikuonetsera kuti anthu awa amakhala ndi utumiki wotumikira
Atumiki aakazi	1 Timoteyo 3:11 Aroma 16:1-2	Udindo uwu sikuti watchulidwa m'Baibulo ayi koma anthu ena anaona kuti ndi wofunikira
Akulu a mpingo	Acts 20:17,28-32 Acts 14:23; 15 Acts 16:4; 11:30 I Timothy 5:17 I Peter 5:1-4 Titus 1:5 James 5:14	Mavesi awa amaonetsa kuti akulu a mpingo amapereka utsogoleri popanga ziganizo mu mpingo, kutumikira ku zosowa za okhululupirira, kuthandizira pa kakulidwe ndi chisamaliro cha okhulupirira mu mpingo

(Dziwani kuti mau oti “akulu” agwiritsidwa ntchito koyamba pa Eksodo 3:16 polankhula za atsogoleri a Israel. Ndipo pali mavesi ambiri okamba za izi m’Baibulo. Akulu awa ndi osiyana ndi udindo wa utsogoleri womwe tili nawo mu mpingo lero wa akulu a mpingo. Mavesi omwe aperekedwawo ndi okhuza akulu ampingo osati akuluakulu a Israel).

Akulu ampingo, atumiki, ndi oyang’anira sakuyenera kuyendetsa mpingo mwaokha popanda utsogoleri wa mtumwi, mneneri, mlaliki, mphunzitsi, ndi m’busa. Akulu ampingo, atumiki ndi oyang’anira amasankhidwa ndi anthu pamene mautumiki asanuwo anaikidwa ndi Mulungu mwini.

### **MAUTUMIKI ENA NDI ENA**

Pakupita kwa nthawi, mpingo wakhala ukumana ndi mavuto ena amene apangitsa kuti pakhale kuthekera kokhazikitsa maudindo ena mu mpingo ngati njira imodzi yothana ndi mavutowo. Maudindo amenewa sanatchulidweko m’Baibulo koma ndi ofunikira ku utumiki ndi chiyanjano cha mpingo wa pamalo. Gawo la “Kupiriza Kuphunzira” la phunziro lino litipatsira mndandanda wa maudindowa.

### **DONGOSOLO LA MAUDINDO MU MPINGO**

Mmusimu muli dongosolo la maudindo onse omwe mwaphunzira kuonetsera momwe amagwilira ntchito onse pamodzi.

#### **MPINGO**

Mautumiki Apadera a Utsogoleri



Atumwi

Aneneri

Alaliki

Abusa

Aphunzitsi



Kuthandizidwa ndi mphatso za oweruza, atsogoleri, oyang’anira, atumiki, akulu a mpingo, ndi chiwalo china chirichonse mu mpingo chomwe chikugwiritsa ntchito mphatso yake moyenera malo amene Mulungu wamuika.



Maziko oikidwa ndi Atumwi ndi Aneneri



Aefeso 2:20



OMANGIDDWA PA TANTHWE, YESU KHRISTU

Mateyu 16:18; 1 Akorinto 3:11; Aefeso 2:20

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Loloweza osaonera.

---

---

2. Onani maudio omwe ali mu mndandanda woyambawo. Werengani tanthauzo lake mu mndandanda wachiwiriwo. Kenako lembani nambala ya tanthauzo lake pa mpata womwe uli kumayambiriro kwa udindowo.

___ Mneneri	1. Wotumidwa mwa ulamuliro kukakhazika mipingo
___ Atumwi	2. Wotumidwa kulankhula uthenga wochokera kwa Mulungu
___ M'busa	3. Amagawa uthenga kwa anthu ochimwa nkumalapa
___ Mlaliki	4. Amadyetsa, kuteteza ndi kusamalira nkhusa
___ Mphunzitsi	5. Amaphuzitsa Mau a Mulungu momveka bwino.
___ Mtsogoleri	6. Amalimbikitsa anthu kukwaniritsa masomphenya
___ Oyang'anira	7. Amaonetsa njira ngati woyendetsa chingalawa.

3. Lembani maudio ena a utsogoleri wa m'Baibulo omwe mwaphunzira

---

---

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwa bukhu lino)

## **KUPITIRIZA KUPHUNZIRA**

M'musimu muli mndandanda wa mipando ina ya utsogoleri mu mpingo:

### **UTUMIKI WA PEMPHERO NDI MACHIRITSO**

- Pemphero lopembedzera
- Kudzodza ndi mafuta
- Kadzutsa wa mapemphero
- Magulu a mapemphero
- Utumiki wa kuchipatala
- Kusala kudya
- Uphungu wa pemphero
- Kulumikizana m'mapemphero

### **MAUTUMIKI OCHITACHITA**

- Kuthandizira mu ofesi
- Mlembi wa mpingo
- Otumiza mauthenga pa mpingo
- Othandizira kophika
- Sukulu za mkomba phala za pampingo
- Kukonza zoonongeka
- Kukonza mgonero
- Kusamalira ana
- Kuthandizira mu chuma
- Mautumiki a zamasewero
- Ma asha
- Maukwati
- Kusoka zovala za magulu oyimba osiyanasiyana
- Kuchereza alendo
- Kusunga chuma cha mpingo
- Magulu a ntchito zosiyanasiyana
- Utumiki wa zosangalatsa
- Kukonzekeretsa nkhani zodziwitsana

### **MAUTUMIKI A MAPHUNZIRO**

- Aphunzitsi a Baibulo
- Atsogoleri a maphunziro a masiku owerengeka
- Utumiki wa achinyamata
- Olalikira m'misonkhano ya padera
- A kafukufuku
- Oyang'anira nyumba yosungira mabuku pa mpingo

- Ma kalasi a akuluakulu
- Mautumiki a wana
- Kupanga ophunzira
- Aphunzitsi a kalasi ya wana
- Ophunzitsa mu maphunziro a Baibulo
- Kuphunzitsa okhulupirira kumene

#### **MAUTUMIKI OPEREKA UPHUNGU**

- Uphungu wa pemphero
- Uphungu wa mabanja
- Uphungu wa kwa achinyamata
- Kulimbikitsa ena
- Kuyendera anthu m'manyumba
- Kuyendera odwala m'chipatala
- Kuthana ndi zovuta pa mpingo

#### **MAUTUMIKI OFIKIRA ANTHU**

- Utumiki wolalikira ana
- Utumiki wa m'mabasi
- Zisudzo
- Utumiki wa m'masukulu a sekondale
- Za ndale
- Zokalalikira kutali
- Misonkhano ya chitsitsimutso
- Ma pologalamu a pawayilesi ndi kanema
- Kulalikira m'makwalala
- Kulalikira m'sukulu za ukachenjede
- Mautumiki azimayi ndi azibambo
- Utumiki wa khomo ndi khomo
- Kugawa mabaibulo ndi ma tiraki

#### **MAUTUMIKI A UTSOGOLERI**

- Okonza dongosolo
- Oyang'anira maphunziro a sande sukulu
- Atsogoleri a miraga
- Oyang'anira utumiki wa kukalalikira kutali
- A pamando a komiti
- Oyang'anira maphunziro
- Oyang'anira mpingo wamkulu

#### **MAUTUMIKI A CHIFUNDO**

- Kuchereza alendo
- Kudyetsa anthu
- Kuyendera odwala
- Kusamalira alendo
- Kuveka ausiwa
- Nyumba zosamalirako anthu
- Kupereka chisangalalo
- Utumiki wa kundende
- Kuthandiza okalamba
- Mayendedwe
- Kulera ana
- Mautumiki akutali
- Utumiki wa m'makwalala
- Kuthandiza anthu opinimbira
- Kuthandiza anthu omwe azunzika
- Kuthandiza olumala
- Kuthandiza osowa
- Utumiki azimayi omwe sali pabanja

#### MAUTUMIKI ENA

- Nyimbo
- Magulu oyimba
- Kuimba zida
- Makwaya
- Kutanthauzira
- Zisudzo
- Kulemba ndi kusindikiza zolembalemba za Chikhristu
- Kulemba nyimbo
- Kukongoletsa mu tchalitchi
- maluso

## **CHAPUTALA 3**

### **KUDZODZA KWA UTSOGOLERI**

#### **ZOLINGA**

Mukamaliza phunziro lino mukhala mukukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Lembani Vesi Lotsogolera osaonera
- Tanthauzirani mau oti “kudzodza.”
- Kudziwa mitundu itatu ya kudzodza
- Kufotokozera cholinga cha mtundu uliwonse
- Kudziwa tsinde la kudzodza kwauzimu.
- Kufotokozera zolinga za kudzodza.
- Kudziwa pamene kudzodza kwa Mulungu kumagonera.
- Kufotokozera mphamvu zomwe zimatsutsana ndi odzodzedwa a Mulungu.
- Kufotokozera kufunika kotumikira mbali imene Mulungu wakudzodza.
- Kufotokozera momwe mungasungire kudzodza kwa Mulungu.

#### **VESI LOTSOGOLERA**

**Koma munakweza nyanga yanga ngati ya njati; Anandidzoza mafuta atsopano.  
(Masalimo 92:10)**

#### **MAU OYAMBA**

Mulungu amafuna atsogoleri atachita bwino komanso kusintha zinthu mu Ufumu wa Mulungu. Kodi mungakhale bwanji mtsogoleri wotere? Kukhala ndi chidziwitso komanso ukadaulo mu kachitidwe ka zinthu nkofunika pa utsogoleri wopambana. Palinso zomuyenereza munthu pa udindo wa utsogoleri molingana ndi Mau a Mulungu zomwe ndi zofunika. Mphatso zauzimu, maluso, maphunziro, ndi ukatswiri ndi zofunikanso. Muphunzira za izi kutsogoloku. Komabe chinthu chofunika kwambiri kwa mtsogoleri ndi kudzodza kwa Mzimu Woyera. Popanda kudzodza kwa Mulungu simungatsogolere, kukonza, kukusa ndi kulalikira mwamphamvu. Chaputala chino chikuyang’ana kwambiri za kudzodza kwa Mzimu Woyera komwe ndi kofunika kwambiri kwa iwo amene aitanidwa ndi kusankhidwa ndi Mulungu kuti atsogolere.

#### **KUDZODZA**

Kudzodza kumatanthauza kupatula kapena kuyeretisa china chake ndi mafuta. Mafuta amaimilira Mzimu Woyera.

Dzina lakuti “Khristu” m’Chigriki limatanthuza “wodzodza.” Yesu analengeza za utumiki wake wa padziko lapansi polengeza kuti:

**Mzimu wa Ambuye uli paine, Cifukwa cace iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino: Anandituma Ine kulalikira am'nsinga mamasulidwe, Ndi akhungu kuti apenyenso, Kuturutsa ndi ufuru ophwanyika, (Luka 4:18).**

Yesu ananena momveka bwino kuti chifukwa cha kudzodza kwa Mzimu Woyera anakwanitsa:

**Mzimu wa Ambuye uli paine, Cifukwa cace iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino: Anandituma Ine kulalikira am'nsinga mamasulidwe, Ndi akhungu kuti apenyenso, Kuturutsa ndi ufuru ophwanyika, Kulalikira caka cosankhika ca Ambuye. (Luka 4:18-19)**

Ngati kunali kofunika kuti Yesu adzodzedwe kuti atumikire bwino, ndiye kuti nkofunikanso kuti ife tidzodzedwenso.

## **MITUNDU ITATU YA KUDZODZA**

Pali mitundu itatu ya kudzodza yomwe yatchulidwa mu Chipangano Chakale. Izi ndi zitsanzo zachilengedwe kapena mitundu ya zinthu zauzimu zomwe Mulungu akufuna kuti atsogoleri ake akhale nazo.

### **KUDZODZA KWA WAKHATE: MAUBALE**

Khate ndi nthenda yoipa kwambiri yomwe imadya mnofu wa munthu wa wodwalayo. Zala za m’manja, za m’mapazi, ndi ziwalo zina za m’thupi kumangoduka.

M’Chipangano Chakale munthu wa khate amatchotsedwa m’ mudzi naikidwa kunja kwa mudzi popeza nthendayi inali yopatsirana. Ngati njira imodzi yodziwitsira anthu kuti asabwere pafupi, iye amafuula, “wodetsedwa” kuli konse akupita. Khatelo limakhala likudya pang’ono pang’ono mnofu wa munthuyo kenako amangodzifera chifukwa cha ululu wochuruka.

Mulungu amagwiritsa ntchito zitsanzo za kuthupi pofuna kufotokozera zinthu zauzimu. Khate limagwiritsidwa ntchito ngati chitsanzo cha uchimo. Monga momwe khate limaonongera khutu la munthu, ntchimo limaononga moyo wauzimu ndi utumiki wanu.

Chilamulo cha m’Chipangano Chakale, Mulungu anapereka malangizo apaderadera a momwe munthu wodwala khate angakhalire woretsetwa. Werengani Levitiko 14 musanapirire ndi

phunziro lino. Langizo liri lonse lomwe mwawerenga la momwe wakhate angayeretsedwere ndi chithunzithunzi chabe cha momwe munthu angayeredwere ku uzimu:

**Mbalame yonyamula uchimo:** Mbalame imodzi iphedwe ndipo mwazi wake uikidwe pa ina. Ichi ndi chizindikiro cha Yesu kukhetsa mwazi kutinyamulira machimo athu.

Kulapa ndi kuvomereza: Izi ndi zomwe mukuyenera kuchita kuti mubadwe mwatsopano ndi kuyeretsedwa ku machimo.

**Madzi oyenda:** Chizindikiro cha ubatizo wa madzi.

**Mafuta odzodza:** Chizindikiro cha ntchito ya Mzimu Woyera m'moyo wanu. Onani kuti mafutawo amaikidwa pa khutu, chala chachikulu, ndi chala chakuphazi cha wakhateyo.

Chimodzimodzi mtsogoleri akuyenera kulandira kudzodza kwa:

- a. Khutu: Kuti azitha kumva liu la Mulungu.
- b. Dzanja: Kuti athe kutumikira Mulungu.
- c. Chala: Kuti ayende mu ubale wabwino ndi Iye.

Kudzodza kofunika kwambiri kwa mtsogoleri ndi kudzodza kwa “wakhate” popeza kumaimilira ubale wa munthu ndi Mulungu. Ngati mukutsogolera anthu mukuyenera kukhala pa ubale wabwino ndi Mulungu. Mukuyenera kubadwa mwatsopano, kumva liu la Mulungu, kumtumikira, ndi kuyenda ndi Ambuye.

### **KUDZODZA KWA WANSEMBE: CHIYERO**

Atsogoleri akuyeneranso kukhala ndi kudzodza kwa wansembe. Werengani Eksodo 29 ndi 30 komanso Levitiko 8 musanapitilire ndi phunziro lino. Kudzodza kwa wansembe kunali kudzodza kwa chiyero, kupatulidwa kuti mukatumikire Mulungu pokhala ndi moyo ndi chikhalidwe choyenera.

Mu nthawi ya Chipangano Chakale, panali zinthu zambiri zomwe wansembe samayenera kuchita nawo chifukwa cha kupatulika ndi kuyeretsedwa kwa ntchito yake. Chifukwa cha kudzodza kwa utsogoleri pa iye, zinthu zina zomwe zimatha kudetsa wansembe, sizimadetsa anthu wamba. Ngati mtsogoleri, mukuyenera kukhala ndi kudzodza kwa wansembe kwa chiyero ndi kupatulidwa ku ntchito yotumikira Ambuye. Mukuyenera kukhala moyo walingana ndi Mau a Mulungu. Pali zinthu zina zomwe simungachite nawo chifukwa cha kupatulika kwa ntchito yanu. Chifukwa cha kudzodza kwapaderadera kotsogolera anthu ena, pali zinthu zinthu zina zomwe anthu angathe kuchita osadetsedwa koma inu nkudetsedwa nazo.

### **KUDZODZA KWA MTSOGOLERI: UDINDO NDI MPHAMVU**



Mtundu wachitatu wa kudzodza mu Chipangano Chakale ndi kudzodza kwa utsogoleri. Uku kunali kudzodza kwa iwo amene anapatsidwa udindo wotsogolera anthu a Mulungu monga mafumu, aneneri ndi akulu a nkondo. Kudzodza kwa utsogoleri ndi kumene kumakhazikitsa udindo wopatsidwa ndi Mulunguwu ndi kumpatsa mphamvu yakukwaniritsa ntchitoyo. Mwachitsanzo, kudzedwa kwa Sauli pa udindo woyang'anira anthu a Mulungu:

**Pamenepo Samueli anatenga nsupa ya mafuta, nawatsanulira pamutu pace, nampsona iye, nati, Sanakudzozi ndi Mulungu kodi, mukhale mfumu ya pa colowa cace? (1 Samueli 10:1).**

Nkhani ya kudzedwa kwa Davide ikupezeka pa 1 Samuel 16. Apa zikuonekeratu kuti mphamvu ya Mulungu inabwera pa Davide chifukwa cha kudzodza:

**Ndipo anatomiza munthu, nabwera naye. Tsono iye anali wofiirira, ndi wa nkhope yokongola, ndi maonekedwe okoma. Ndipo Yehova anati, Nyamuka umdzoze, pakuti ndi ameneyu. Pamenepo Samueli anatenga nyanga ya mafuta, namdzoza pakati pa abale ace; ndipo mzimu wa Yehova unalimbika pa Davide kuyambira tsiku lomweli. (1 Samueli 16:12-13).**

Kudzodza kwa utsogoleri kumakhazikitsa udindo, mphamvu ndi ulamuliro wa udindowo. Kudzera nkudzodzaku, Mzimu wa Mulungu umatsikira pa munthuyo kuti athe kutsogolera bwino anthu a Mulungu. Lonjezo la m'Chipangano Chatsopano pa kudzodza uku liri pa Machitidwe 1:8.

**Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko. (Machitidwe 1:8)**

Kukwaniritsidwa kwa lonjezo ili kuli pa Machitidwe 2. Ubatizo wa Mzimu Woyera m'Chipangano Chatsopano ndi kukwaniritsidwa kwa mphamvu ya kudzodza kwa utsogoleri. Kudzodza udindo m'Chipangano Chatsopano kwafotokozeredwa bwino mu Aefeso:

**Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; (Aefeso 4:11)**

Mulungu wadzodza anthu ena kuti akhale atsogoleri mu mpingo ndipo wapatsa kudzodza kwa mphamvu kuti akathe kukwaniritsa maitanidwe awo.

**KUDZODZA KUMACHOKERA KWA MULUNGU**

Mitundu itatu ya kud zodza yomwe tayiwonayi imachokera kwa Mulungu. Pamene Samu eli anadzodza Sauli, iye anati, “Mulungu wakudzodza iwe. (1 Samu eli 10:1; 15:17). Pamene Yesu amalengeza za kud zodza kwake anati, “Ambuye wandidzodza ine.” (Luka 4:18; onaninso Machitidwe 10:38). Ndi Mulungu amene amadzutsa anthu odzodzedwa. Mulungu ananena kwa Samu eli:

**Ndipo ndidzadziukitsira wansembe wokhulupirika, amene adzacita monga cimene ciri mumtima mwanga ndi m'cifuniro canga; ndipo ndidzammangira nyumba yokhazikika, ndipo iyeyu adzayenda pamaso pa wodzozedwa wanga masiku onse. (1 Samu el 2:35).**

Kudzodza sikubwera chifukwa chakuti mpingo wakudzodza ayi (ngakhale kuti sizolakwika kud zodza anthu). Kud zodza kwa utsogoleri kumachokera kwa Mulungu:

**Ndipo inu, kudzoza kumene munalandira kucokera kwa iye, kukhala mwa inu, ndipo simusowa kuti wina akuphunzitseni; koma 9 monga kudzoza kwace kukuphunzitsani za zinthu zonse, ndipo kuli koono, sikuli bodza ai, ndipo monga kudaphunzitsa inu, mukhale mwa iye. (1 Yohane 2:27)**

Stefano anadzodzedwa ndi anthu kukhala mtumiki. Koma Mulungu anamudzodza kukhala mlaliki (Machitidwe 6). Ndi kud zodza kwa Mulungu, osati kwa munthu, komwe ndi kofunika kwambiri.

## **MAZIKO A KUDZODZA**

Koma Mulungu podzodza munthu amaona chiyani? Mulungu akamadzodza munthu sayang'ana nzeru, maphunziro, ukadaulo, kapena kuthekera kwa mtundu wina uliwonse. Kud zodza kwa Mulungu sikutengera maonekedwe a munthu. Koma mtima wa munthu.

Pamene Samu eli anapita kunyumba kwa Jesse kukadzodza mfumu, amayang'ana munthu amene ali ndi maonekedwe okoma.

**Ndipo kunali, pakufika iwo, iye anayang'ana pa Eliyabu, nati, Zoonadi, wodzozedwa wa Yehova ali pamaso pace. Koma Yehova ananena ndi Samu eli, Vsayang'ane nkhope yace, kapena kutalika kwa msinkhu wace, popeza Ine ndinamkana iye; pakuti Yehova saona monga aona munthu; pakuti munthu ayang'ana cooneka ndi maso, koma Yehova ayang'ana mumtima. (1 Samu el 16:6-7).**

Mulungu anadzodza Davide poyang'ana mtima wake. Mulungu amaonena zomwe munthu ali mkati mwake.

## **CHOLINGA CHA KUDZODZA**

Zina mwa zolinga za kud zodza nazi:

### **KUMAKWANIRITSA ZOLINGA ZA MULUNGU**

Mulungu amapereka kud zodza kwa utsogoleri kwa anthu kuti akathe kukwaniritsa zolinga zake.

Yesu anapanga izi kukhala zomveka bwino:

**Mzimu wa Ambuye uli paine, Cifukwa cace iye anandidzoza Ine ndi uze anthu osauka Uthenga Wabwino: Anandituma Ine kulalikira am'nsinga mamasulidwe, Ndi akhungu kuti apenyenso, Kuturutsa ndi ufuru ophwanyika, (Luka 4:18)**

### **KUMAPEREKA NZERU ZA UTSOGOLERI**

Kud zodza kumapereka nzeru pa munthu kuti akatsogolere anthu osati kutsogoleredwa:

**Ndipo inu, kud zoza kumene munalandira kucokera kwa iye, kukhala mwa inu, ndipo simusowa kuti wina akuphunzitseni; koma 9 munga kud zoza kwace kukuphunzitsani za zinthu zonse, ndipo kuli koono, sikuli bodza ai, ndipo munga kudaphunzitsa inu, mukhale mwa iye. (1 Yohane 2:27)**

### **KUMAONONGA GOLI**

Kud zodza ndi komwe kumaononga magoli omwe amamanga anthu omwe mukuwatumikira.

Baibulo limaonetsa kuti pali mitundu itatu ya magoli:

1. Pali goli la uchimo:

**Ine ndine Yehova Mulungu wanu, amene ndinakuturutsani m'dziko la Aigupto, kuti musakhale akapolo ao; ndipo ndinatyola mitengo ya magoli anu, ndi kukuyendetsani coweramuka. (Levitiko 26:13)**

2. Pali goli lomanga anthu kuti akhazikike mu zofuna za thupi:

**Pakuti cimene ndicita sindicidziwa; pakuti sindicita cimene ndifuna, koma cimene ndidana naco, ndicita ici. (Aroma 7:15)**

3. Pali goli lomwe limachita kuikidwa pa munthu ndi anthu ena. Goli limeneli litha kukhala la kutsutsika, miyambo, kapena makhalidwe oipa omwe amachita kuikidwa pa munthu:

**Inde, amanga akatundu olemera ndi osautsa ponyamula, nawasenza pa mapewa a anthu; koma iwo eni okha safuna kuwasuntha amenewo ndi cala cao. (Mateyu 23:4)**

Kud zodza kumaononga magoli onsewa:

**Ndipo padzakhala tsiku lomwelo, kuti katundu wace adzacoka pa phewa lako, ndi gori lace pakhosi pako; ndipo gori lidzathedwa cifukwa ca kudzoza mafuta. (Yesaya 10:27)**

Magoli awa sangaonongeke ndi kuzama kwa chiphunzitso. Sangaonongeke ndi kuchuluka kwa maphunziro, uphungu kapena dongosolo la mpingo. Magoliwa amaonongeka ndi kudzodza kwa Mulungu kobweretsedwa ndi atsogoleri auzimu omwe amadziwa bwino kubweretsa uthenga wa mamasulidwe kwa omangidwa m'goli.

### **KUMAONETSERA MTUNDU WA UDINDO**

Mulungu amadzodza anthu kukatumikira m'maudindo osiyanasiyana a utumiki. Mwachitsanzo, udindo wa wansembe umadziwika ndi “mtundu wa kudzodza” (Numeri 18:8).

Chipangano Chatsopano chimafotokoza momveka bwino kuti Mulungu mphatso zauzimu ndi maitanidwe osiyanasiyana kwa okhulupirira. Mukuyenera kudziwa maitanidwe amene Mulungu wakupatsani, mphatso zanu zauzimu, komanso cholinga chanu chenicheni mu dongosolo la Mulungu kuti mukayende mu kudzodza kwa Mzimu Woyera. Mukakamira kutumikira mu dera limene Mulungu sanakuitanireni kapena kukudzodzani, mukumana ndi zokhoma. Ndi chifukwa chake mukuyenera kumvetsa mfundo yotsatirayi.

### **YENDANI NKUDZODZA KWANU**

Mulungu amadzodza anthu kuti akatumikire m'maudindo, mautumiki, komanso maitanidwe osiyanasiyana. Atsogoleri ambiri amalephera chifukwa chosamvetsa mfundo imeneyi.

Amalimbana ndi kuchita mautumiki amene Mulungu sanaitanireko kapena kuwadzodza:

- Werengani Numeri 16. Pamene Kora ndi amuna ena amaona kuti ali ndi kudzodza kofanana ndi Mose, Mulungu anawatsutsa.
- Werengani Numeri 17. Mulungu anatsimikira anthu za kudzodza kwa paderadera komwe kunali pa Aaroni.
- Werengani 1 Samuel 13:8-14. Pamene Mfumu Sauli anayesera kuchita imene analibe nayo kudzodza kwake, anaweruzidwa ndi kukanidwa ndi Mulungu.
- Werengani Machitidwe 19:13-16. Pamene ana amuna asanu ndi awiri a Skeva anayesera kutumikira nkudzodza komwe analibe, anakumana ndi zokhoma.

Tumikirani nkudzodza komwe Mulungu anakupatsani, mukapanda kutero mukhala wopanda mphamvu komanso mukumana ndi zovuta zambiri.

### **YEMBEKEZERANI KUKUMANA NDI ZOKHOMA**

Ngati mwadzodzedwa ndi Mulungu, yembekezerani kuti Satana, ziwanda ndi anthu achikunja alimbana nanu:

**Adzikhazikitsa mafumu a dziko lapansi, Nacita upo akulu pamodzi, Kutsutsana naye Yehova, ndi Wodzozedwa wace, ndi kuti. (Masalimo 2:2)**

**Cimene adani anu, Yehova, atonza naco; Cimene atonzera naco mayendedwe a wodzozedwa wanu. (Masalimo 89:51)**

Mphamvu zakumdima zilimbana nanu chifukwa zikudziwa kuti muli ndi kudzodza komwe kudzakwaniritsa zolinga za Mulungu.

### **KUDZODZA KWATSOPANO**

Davide akulankhula za “mafuta atsopano” omwe ali chizindikiro cha kudzodza kwatsopano kopitilira kwa Mulungu.

**Koma munakweza nyanga yanga ngati ya njati; Anandidzoza mafuta atsopano. (Masalimo 92:10)**

Mumakhalabe ndi kudzodza kwatsopano kwa Mulungu pamene mukayenda m’kudzodza kwa mitundu itatu komwe taona kale m’mbuyomu.

### **KUDZODZA KWA WAKHATE: UBALE**

Kudzodza kwanu sikupitilira pokhapokha ubale wanu ndi Mulungu ukhale ukuyenda bwino. Mukuyenera kukhala wolumikizana ndi Mulungu nthawi zonse m’pemphero, kusanthula malemba kuti mumve liu lake, kumtumikira, ndi kuyenda m’njira zake. Kutumikira pa udindo ndi ulamuliro popanda ubale wabwino ndi Mulungu kumapangitsa munthu kukhala wopanda mphamvu nakhala wotayidwa kunja:

**koma 4 ndipumpuatha thupi langa, ndipo ndiliyesa capolo; kuti, kapena ngakhale rdalalikira kwa ena, 5 ndingakhale votayika ndekha. (1 Akorinto 9:27)**

**Si yense wakunena kwa Ine, Ambuye, Ambuye, adzalowa mu Ufumu wa Kumwamba; koma wakucitayo cifuniro ca Atate wanga wa Kumwamba. Ambiri adzati kwa Ine tsiku lomwelo, Ambuye, Ambuye, kodi sitinanenera mau m'dzina lanu, ndi m'dzina lanunso kuturutsa mizimu yoipa, ndi kucita m'dzina lanunso zamphamvu zambiri? Ndipo pamenepo ndidzafukulira iwo, Sindinakudziwani inu nthawi zonse; cokani kwa Ine, inu akucita kusayeruzika. (Mateyu 7:21-23)**

### **KUDZODZA KWA WANSEMBE**

Mukuyenera kukhala moyo wachiyero kuti muyendebe nkudzodza kwatsopano kwa Mulungu pa moyo ndi utumiki wanu. Makhalidwe anu akhale oyera ndi kukhala wangwiro ndi woona mtima mdera liri lonse la moyo wanu.

### **KUDZODZA KWA MTSOGOLERI: UDINDO NDI MPHAMVU**

Mukuyenera kutumikira nkudzodza kumene Mulungu wakuitanirani. Musamatengera mautumiki ndi maitanidwe a anthu ena. Mukuyeneranso kulandira kudzadzidwa kopitilira kwa Mzimu Woyera komwe kumapangitsa kuti munthu akhalebe wamphamvu mu zomwe Mulungu wamuitanira.

### **MOMWE ZIMAGWIRIRA NTCHITO LIMODZI**

Kudzodza kwa mitundu itatu uku kumagwira ntchito limodzi kuti mukhalebe ndi kudzodza kwatsopano kwa Mulungu pa moyo wanu.

- Popanda ubale wabwino ndi Mulungu simungakhale wa mphamvu ndipo simungakwanitse kukhala moyo wachiyero.
- Kutsindika za chiyero popanda mphamvu mumakhala mgoli la chilamulo.
- Kukhala ndi mphamvu koma osakhala moyo wachiyero kudzakupangani kukhala munthu amene watumikira ena koma iyeyo nkukhala “wotayidwa kunja.”

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osonera.

---

---

---

2. Kodi akati “kudzodza” amanthauza chiyani?

---

---

3. Kodi mafuta ndi chizikiro cha chiyani?

---

---

4. Lembani mitundu itatu ya kud zodza yomwe yalankhulidwa m’phunziro lino ndi kufotokozera tanthauzo la kud zodza kuli konse.

---

---

---

5. Kodi tsinde la kud zodza kwa utumiki ndi ndani?

---

6. Fotokozerani cholinga cha kud zodza.

---

---

7. Kodi Mulungu akamad zodza amayang’ana chiyani? Maphunziro, ukadaulo, kapena nzeru?

---

---

8. Fotokozerani chifukwa chomwe m’phamvu za kum’tima zimakhala zikulimbana ndi odzodzedwa a Mulungu.

---

---

---

9. Kodi kutumikira m’udindo umene Mulungu wakupatsa ndi kofunika motani?

---

---

---

10. Kodi mungatani kuti mukhalebe ndi kudzodza kwatsopano pa moyo wanu?

---

---

---

(Mayankho a mafunso onsewa ali kumapeto kwa bukhu lino)

### **KUPITIRIZA KUPHUNZIRA**

1. Santhulani za ubale wa Mulungu ndi anthu omwe wawadzodza.
  - Mulungu amapatsa mamasulidwe ndi chifundo iwo amene wawadzodza: Masalimo 18:50
  - Amamva ndi kupulumutsa odzodzedwa: Masalimo 20:6
  - Amayang'ana nkhope za odzodzedwa ake: Masalimo 84:9
  - Iye ndi nyonga yakupulumutsa ya odzodzedwa: Masalimo 28:8
  - Amapereka mabvumbulutso kwa odzodzedwa ake (nyali ya odzodzedwa): Masalimo 132:17
  - Mulungu amadzodza kuchotsa mdani: 2 Mbiri 22:7
2. Werengani zambiri za kudzodza:
  - Kutchulidwa koyamba kwa kudzodza: Genesis 31:13
  - Kudzodza kumayendera limodzi ndi chimwemwe ndi chilungamo: Masalimo 45:7; Ahebri 1:9
  - Chilema chachibadwidwe sichingaletse kudzodza: 2 Samuel 3:39
  - Kudzodza kukugwiritsidwa ntchito kuchiritsa odwala mu Marko 6:13 ndi Yakobo 5:14; wakhungu mu Yohane 9:6, 11; ndi akhungu lauzimu mu Chibvumbulutso 3:8
  - Mafuta oyera amagwiritsidwa ntchito m'Chipangano Chakale: Eksodo 30:31
  - Umodzi ukuyerekezedwa ndi kudzodza: Masalimo 133:2
  - Kudzodza kukuyerekezedwa ndi chiyero: Eksodo 29:29
  - Mau a Mulungu ndi odzodzedwa: Levitiko 7:36
3. Mwaphunzira kale momwe kudzodza kumagwiritsidwira ntchito m'Chipangano Chakale kwa akhate, ansembe, ndi atsogoleri. Kumagwiritsidwanso ntchito kudzodza:



- Zopereka: Eksodo 29:36
  - Zinthu za m' chihema: Levitiko 8, Numeri; Eksodo 40
  - Maguwa ansembe: Genesis 31:13
4. Popeza kuti atsogoleri anadzodzedwa ndi Mulungu, tikuyenera kukhala osamalitsa ndi kusalimbana nawo. Onani Numeri 16; 1 Sameul 24 ndi 26; 2 Samuel 1; 1 Mbiri 16:22; Masalimo 105:15.
  5. Kudzodza kwa munthu sikwa Mulungu. Onani 2 Samuel 19:10. Werengani nkhani yomvetsa chisoni ya Absalom amene anadzodzedwa ndi anthu (2 Samuel 18-20).
  6. Werengani za kudzodza kwa:
    - Yoswa: Deuteronomu 34:9 ndi Numeri 27:18, 22
    - Sauli: 1 Samuel 10:15-27
    - Davide: 1 Samuel 16:1-13
    - Yesu: Luka 4:18
  7. Santhulani Machitidwe 7:25 ndi Eksodo 2:11-15. Mose anali ndi maitanidwe oyenera koma ulamuliro wolakwika poyamba. Anayamba kutumikira mu ulamuliro wake wa iye yekha m'malo mwa ulamuliro wa Mulungu.
  8. Werengani Amosi 7:14-15. Amosi sanali mtumiki. Anali woweta nkhosa ndi wolima m'munda. Koma Mulungu atamuitana anakhala mneneri.

## **CHAPUTALA 4**

### **ZOYENERA ATSOGOLERI**

#### **ZOLINGA**

Pomaliza chaputala mukuyenera kukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kutanthauzira “zomuyenereza munthu.”
- Kutanthauzira chipatso cha Mzimu chakunja
- Kutanthauzira chipatso cha Mzimu chamkati.
- Kudziwa ndime zenizeni ziwiri zomwe zikukamba za zoyenereza atsogoleri auzimu.
- Kulemba mfundo zinayi zofunika atsogoleri auzimu.

#### **VESI LOTSOGOLERA**

**Pakuti ife ndife cipango cace, olengedwa mwa Kristu Yesu, kucita nchito zabwino, zimene Mulungu anazipangiratu, kuti tikayende m'menemo. (Aefeso 2:10)**

#### **MAU OYAMBA**

Mulungu akaitana wokhulupirira ku utsogoleri, amafuna atamukonzekeretsa ku utumiki. Popeza kuti ntchito ndi maitanidwe zimakhala zosiyanasiyana, zoyenereza munthu m'maitanidwe ndi mautumiki m'Thupi la Khristu zimakhalanso zosiyana. Mulungu amakonzekeretsa mtsogoleri wina aliynse mu njira zosiyanasiyana.

Pamene Mulungu akupatsa atsogoleri makhalidwe apaderadera ogwirizana ndi maitanidwe awo, pali machitidwe ena omwe akufunika kuti mtsogoleri wauzimu wina aliynse akhale nawo. Makhalidwe kapena zoyenereza zimenezi ndiye mutu wa phunziro lino. Tikhala tikukamba za zofunikira atsogoleri, chipatso cha mzimu, zoyenera atsogoleri zapaderadera koma za onse.

#### **ZOYENERA ATSOGOLERI MOLINGANA NDI MAU A MULUNGU**

Zoyenezazi si maluso obadwa nawo. Ndi makhalidwe kapena machitidwe ofunika atsogoleri ndipo afotokozeredwa m'Mau a Mulungu momveka bwino. Ndi maumboni a moyo waumulungu.

Anthu amatengeka ndi kuthekera kwa mtsogoleri kuiwala za makhalidwe ake. Mwachitsanzo, anthu akhoza kumutchula munthu kuti ndi m'busa wabwino chifukwa cha kalalidwe kake kokoma. Koma mwina ngakhale akukopa anthu ndi malankhulidwe ake okoma, alibe makhalidwe a umulungu ofunika atsogoleri molingana ndi Mau a Mulungu.

Utsogoleri wa uzimu ukuyenera kuonedwa molingana ndi mfundo za m’Baibulo. Utumiki wamphamvu siwamphatso zauzimu, mphamvu, kapena kuthekera kwa umunthu. Kupambana kwa utumiki kukuyenera kuyesedwa molingana ndi chikhalidwe cha umulungu chomwe munthu ali nacho chomwe chimatchulidwanso kuti “chipatso chauzimu.”

**Inde comweco pa zipatso zao mudzawazindikira iwo. (Mateyu 7:20).**

Chipatso kapena makhalidwe auzimu a munthu amabvumbulutsa chomwe munthuyo ali mkati mwake:

**palibe mtengo wabwino wakupatsa zipatso zobvunda; kapenanso mtengo woipa wakupatsa zipatso zabwino, Pakuti 12 mtengo uli wonse uzindikirika ndi cipatso cace. Pakuti anthu samachera nkhuju paminga, kapena pamtungwi samachera mphesa, 13 Munthu wabwino aturutsa zabwino m'cuma cokoma ca mtima wace; ndi munthu woipa aturutsa zoipa m'coipa cace: pakuti m'kamwa mwace mungolankhula mwa kucuruka kwa mtima wace. (Luka 6:43-45).**

Munthu atha kukhala ndi machitidwe okopa kuti mwina ena nkumaona ngati ndi mphamvu yauzimu. Penanso kuchita zozizwa kumene m’dzina la Ambuye Yesu. Koma Yesu anati:

**Si yense wakunena kwa Ine, Ambuye, Ambuye, adzalowa mu Ufumu wa Kumwamba; koma wakucitayo cifuniro ca Atate wanga wa Kumwamba. Ambiri adzati kwa Ine tsiku lomwelo, Ambuye, Ambuye, kodi sitinanenera mau m'dzina lanu, ndi m'dzina lanunso kuturutsa mizimu yoipa, ndi kucita m'dzina lanunso zamphamvu zambiri? Ndipo pamenepo ndidzafukulira iwo, Sindinakudziwani inu nthawi zonse; cokani kwa Ine, inu akucita kusayeruzika. (Mateyu 7:21-23)**

Yuda anachenjeza za iwo amene “adzakwawira mkati” mwa mpingo ndi kuphunzitsa chiphunzitso chonyenga. Iye anatchula njira imodzi yomwe tingagwiritse ntchito kuti tiwazindikire. Kukhala opanda chipatso m’ moyo wao:

**Iwo ndiwo okhala mawanga pa mapwando anu a cikondano, pakudya nanu pamodzi, akudziweta okha opanda mantha; mitambo yopanda madzi, yotengekatengeka ndi mphepo; mitengo ya masika yopanda zipatso, yofafa kawid, yozuka mizu; (Yuda 12)**

Chinthu chofunikira kwambiri pa utumiki wina uliwonse ndi chipatso popeza kuti Malemba amati, “Mudzawazindikira ndi zipatso zawo.”

## ZINTHU ZOFUNIKIRA POYAMBA

Pali zinthu zinayi zofunikira kuti zichitike kaye pa mtsogoleri wina aliyense. Mkhristu akuyenera akhale:

1. **Wobadwa mwatsopano:** Akuyenera kukhala wokhulupirira Yesu ngati Mbuye ndi Mpulumutsi wake molingana ndi Yohane 3.
2. **Wobatizidwa ndi Mzimu Woyera:** Akuyenera kukhala ndi umboni wakuti ndi mboni yamphamvu molingana ndi Machitidwe 1:8.
3. **Woitanidwa ndi kudzodzedwa kuti akhale mtsogoleri:** Anthu akuyenera kukhala kuti ayitanidwa komanso kudzodzedwa kuti akhale paudindo wotsogolera mu mpingo.
4. **Wokhwima muuzimu:** Mtsogoleri asakhale wa maganizo osasinthika (1 Akorinto 3:1) kapena wakhanda muuzimu (1 Timoteyo 3:6). Akuyenera akhale kuti waphunzira bwino chiphunzitso choyambilira cha chikhulupiriro cha Chikhristu chomwe chafotokozeredwa pa Ahebri 6:1-3 ndi kunka ku mulingo wakukula muuzimu.

Kukhwima muuzimu kumakhalapo pamene munthu ali pa ubale wabwino ndi Ambuye m'chikhalidwe chopemphera ndi kusanthula Mau. Ngati mungatsogolere anthu ena mu njira za Ambuye, mukuyenera kumalumikizana ndi Mulungu ndi kukula m'chidziwitso cha Mau ake. Mutha kupita kumisonkhano ya atsogoleri, ku sukulu ya ukachenjede wa Baibulo kapena kuwerenga mabuku ambiri autsogoleri koma ngati simufunafuna Ambuye panokha, utsogoleri wanu ukanika.

## CHIPATSO CHA MZIMU

Chipatso cha Mzimu ndi chikhalidwe cha Mzimu chobvumbulutsidwa m'moyo wa wokhulupirira. Ndi makhalidwe auzimu omwe akufunika kukhala mwa Mkhristu wina aliyense, makamaka atsogoleri auzimu.

Baibulo limakamba za mitundu iwiri ya chipatso chamzimu: chipatso chakunja cha kulalikira ndi chipatso cha mkati cha makhalidwe a umulungu. Atsogoleri auzimu akuyenera kubala chipatso pakukhala mboni zamphamvu sofalitsa Uthenga Wabwino:

**Inu simunandisankha Ine, koma Ine ndinakusankhani inu, ndipo ndinakuikani, kuti mukamuke inu ndi kubala cipatso, ndi kuti cipatso canu cikhale; kuti cimene ciri conse mukapempha Atate m'dzina langa akakupatseni inu. (Yohane 15:16)**

Lamulo lamizira la Yesu asanakwere kunka kumwamba linali lakuti:

**Ndipo ananena nao, mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse. (Marko 16:15)**

Anawabetchera ophunzira ake powapatsa masomphenya aakulu a kholola lauzimu:

**Kodi simunena inu, kuti, Yatsala miyezi inai, ndipo kudza kumweta? Onani ndinena kwa inu, Kwezani maso anu, nimuyang'ane m'minda, kuti mwayera kale kufikira kumweta. Wakumweta alandira kulipira, nasonkhanitsira cobala ku moyo wosatha; kuti wofesayo akakondwere pamodzi ndi womwetayo. (Yohane 4:35-36)**

Solomoni anati:

**Cipatso ca wolungama ndi mtengo wa moyo; Ndipo wokola mtima ali wanzeru. (Miyambo 11:30).**

Mphamvu ya Mzimu Woyera imalola okhulupirira kuti akhale obala zipatso muuzimu polalikira Uthenga Wabwino:

**Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko. (Machitidwe 1:8)**

Njira ya kukhala wobereka muuzimu yaperekedwa pa 2 Timoteyo 2:2:

**Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso. (2 Timoteyo 2:2)**

Chifukwa cha kufunika kwa chipatso cha kulalikira Uthenga Wabwino, Harvestime International Institute imapereka phunziro lotchedwa “Ulaliki wa Mtupatupa.”

Kuphatikiza pa chipatso chazimu cha kulalikira, atsogoleri akuyenera kukhala ndi chikhalidwe chofanana ndi Khristu:

**pakuti cipatso ca kuunika ticipeza m'ubwino wonse, ndi cilungamo, ndi coonadi, (Aefeso 5:9)**

Mu chipatso cha Mzimu Woyera mulinso makhalidwe apaderadera awa:

### **CHIKONDI:**

Chikondi ndi momwe munthu amamvera zokhuzana munthu wina. Ndi chilakolako chachikulu chosamalira, ndi kukhuzika. Kumva chifundo, kumvetisa, kulimbikitsa, kumvetsera komanso kukhala bwenzi.

Mtsogoleri akuyenera kukhala wokonda Mulungu (Marko 12:30). Mtsogoleri akuyenera kuonetsera chikondi omutsatira, okhulupirira, komanso anthu osapulumsidwa (1 Petro 1:22; Luka 6:27; 32; 35; Mateyu 5:43-44; 19:19; Yohane 13:34-35; 15:9, 12; 1 Yohane 2:9-10). Ntchito ya mtsogoleri kwa anthu ndiko kugwira ntchito ya chikondi (1 Atesalonika 1:3). Chikhulupiriro chimagwira ntchito kudzera mu chikondi (Agalatiya 5:6) chimodzimodzinso mphatso zauzimu (1 Akorinto 13). Chikondi ndi mfungulo ya kuchita bwino m'mautumiki onse (1 Akorinto 13.).

Chikondi chimafunika luso lotha kucheza bwino ndi anthu. Ndiko kuthekera kochita zofunika komanso zovuta kuchita koma osakhumudwitsa anthu ena.

### **CHIMWEMWE**

Chimwemwe ndiko kukhala wokondwa ndi wosangalala. Ndi chikhumbokhumbo cha Mulungu kuti inu mukhale ndi chimwemwe (Yohane 15:11; 17:13). Ophunzira anadzadzidwa ndi chimwemwe ndi Mzimu Woyera (Machitidwe 13:52). Gwero la chimwemwe si zinthu za dziko lapansi koma Mulungu (Masalimo 16:11). Popeza kuti chimwemwe chenicheni ndi chauzimu osati chodalira zooneka ndi maso, mtsogoleri angathe kukondwe m'mayesero (Yakobo 1:2; 2 Akorinto 7:14). Angathe kupirira ndi chimwemwe (Akolose 1:11).

### **MTENDERE**

Mtendere ndi pamene pali bata, kumvana ndi umodzi. Osati pamene pali mkangano, nkhwana kapena madandaulo. Mtsogoleri wokhala ndi mtendere mumtima amakhala wodalarika komanso wotha kuupeza mtima zinthu zikayamba kuvuta.

Chisokonezo chimatsutsana ndi mtendere. Mulungu sabweretsa chisokonezo pamalo.

Chokhumba chake nchakuti anthu akhale pa mtendere (1 Akorinto 14:33). Mtendere weniweni umadza ndi Yesu Khristu (Machitidwe 10:36); Aefeso 2:14; Aroma 5:1; Yohane 14:27; 16:33). Mtsogoleri akuyenera kukhala anthu ofuna zokhazo zobweretsa mtendere pamalo (Aroma 14:19) ndi kukhala pa mtendere ndi wena (2 Akorinto 13:11; Ahebri 12:14). Umodzi womwe ndi wofunika pa utumiki uliwonse wamphamvu, umasungika ndi mtendere (Aefeso 4:3). Mtendere wa Mulungu ukuyenera kulamulira mu mtima wa wotsogolera (Akolose 3:12).

### **KUPIRIRA**

Kupirira ndi chikhalidwe chomulola munthu kukwanitsa kudutsa mu nyengo zowawa mwa msangala ndi mofatsa. Paulo mu utumiki wake anaonetsera chikhalidwe chakupirira (2 Timoteyo 3:10). Tikuyenera kukhala anthu opirira koma ndi chimwemwe (Akolose 1:11).

Mtsogoleri akuyenera kulalikira Mau a Mulungu ndi chipiriro (2 Timoteyo 4:2) ndi kukhala ndi wena ndi chikhalidwe chimenechi (Aefeso 4:2). Akuyenera “kuvala” chipiriro ngati chikhalidwe chazimu (Akolose 3:12).

### **KUFATSA**

Kufatsa ndi chikhalidwe chokhala ndi moyo wodekha, osati wachiwawa, kapena ndeu. Ndi chifundo cha chete komanso chaulemu. Mau a Mulungu amatchenjeza kuti tisakhale anthu a chiwawa koma ofatsa ndi anthu onse (2 Timoteyo 2:24). Iye si anthu a ndeu omwe amakhala kukangana ndi mapokoso (Tito 3:2). Tikuyenera kukhala anthu osavuta kukhala nawo.

Kutanthauza kuti anthu asamaope akafuna kutifikira (Yakobo 3:17).

Mtsogoleri wofatsa amakhala wopambana. Davide analemba kuti:

**Ndipo mwandipatsa cikopa ca cipulumutso canu: Ndipo dzanja lamanja lanu landigwiriziza, Ndipo cifatso canu candikuza ine. (Masalimo 18:35).**

### **WOKOMA MTIMA**

Kukoma mtima ndi makhalidwe a chiyero kapena olungama. Mulungu amakhutitsa anjala ndi kukoma mtima (Masalimo 107:9). Monga okhulupirira, ukoma ndi zifundo za Mulungu zimatitsata (Masalimo 23:6).

### **CHIKHULUPIRIRO**

Chikhulupiriro ndi maganizo otsimikizika ndi oyembekezera pa Mulungu (Ahebri 12:1). Ndiko kutsimikizika kuti zonse zimene Mulungu ananena ndi zoonza ndipo palibe chosatheka.

Chikhulupiriro chimachita zinthu zazikulu mu Ufumu wa Mulungu chikayendera limodzi ndi ntchito ya utumiki.

Chikhulupiriro ndiko kudalira kwatunthu mwa Mulungu zomwe zimapangitsa otsatira kutsimikizika ndi kuumba chikhulupiriro chawo. Ndiko kutsimikizika konena kuti, “Ndingathe kuchita zonse mwa Khristu Yesu wondipatsa mphamvu ine.”

### **KULEZA MTIMA**

Kuleza mtima ndiko kudzigwira pamene uli ndi kuthekera kochita zinthu. Kupereka chilango mu mpingo kukuyendera kuchitika ndi kuleza mtima konse (Agalatiya 6:1). Ndipo zimathandizira mtsogoleri kuti akwanitse kusungitsa bata ndi umodzi mu mpingo (Aefeso 4:1-3). Mtsogoleri akuyenera kukhala woleza mtima nthawi zonse (Tito 3:2; 2 Timoteyo 2:24-25). Munthu wanzeru amakhala wofatsa (Yakobo 3:13). Okhulupirira onse akulimbikitsidwa kukhala ndi chikhalidwe choleza mtima (Akolose 3:12; 1 Timoteyo 6:11; Zefaniya 2:3).

## **KUDZILETSA**

Kudziletsa ndiko kudzigwira m'mene munthu akumvera, akuganizira ndi kuchitira zinthu. Kudziletsa kumathandiza mu zinthu zambiri (1 Akorinto 9:27 ndi 9:19-27). Tikuyenera kuphatikizapo kudziletsa ku makhalidwe a moyo wathu (2 Petro 1:6).

## **ZOYENEREZA ZAPADERADERA**

Kuonjezera pa chipatso chauzimu, Baibulo likufotokozanso za makhalidwe a paderadera ofunika atsogoleri. Makhalidwewa akupezeka pa 1 Timoteyo 3 ndi Tito 1. Zoyenera ziri m'musizi ndi zokhuzana ndi azibusa, oyang'anira, akulu, ndi atumiki. Ngakhale izi ziri chomwechi, makhalidwewa ndi ofunika kwa atsogoleri a maudindo osiyanasiyana:

## **OYANG'ANIRA NDI ATSOGOLERI**

**Opanda chilema:** Akhale ndi mbiri yabwino ndi amakhalidwe abwino komanso osati ophwanya Mau a Mulungu: 1 Timoteyo 3:2; Tito 1:6, 7.

**Mwamuna wa mkazi m'modzi:** Ngati ndi wokwatira, akhale kuti ali ndi mkazi mmodzi: 1 Timoteyo 3:2; Tito 1:6. (Kugwira ntchito limodzi mu utumiki nkofunikiranso).

**Wofatsa:** Wodekha mu zinthu zonse: Tito 1:8; 1 Timoteyo 3:2

**Wodziletsa:** Aonetse kudziletsa m'magawo onse a moyo ndi zochitika zake. Ngati munthu akufuna kutsogolera ena, akuyenera kutha kudziletsa yekha. Tito 1:8

**Wolongosoka:** Kutanthauza kuti akhale wokhala nacho chidziwitso, wanzeru, komanso wotha kuchita zinthu: 1 Timoteyo 3:2; Tito 1:8.

**Wochereza alendo:** Akhale womasuka kwa anthu: 1 Timoteyo 3:2; Tito 1:8

**Wotha kuphunzitsa:** Akhale ndi kuthekera kophunzitsa Mau a Mulungu kwa ena: 1 Timoteyo 3:2; Tito 1:9.

**Wosati woledzera:** 1 Timoteyo 3:3; Tito 1:7.

**Wodekha:** Osati wachiwawa: 1 Timoteyo 3:3

Wopanda liuma: Asakhale wongoyang'ana za iye yekha osafuna kumva maganizo a ena: Tito 1:7

**Asakhale khanda muuzimu:** Akhale wokhulupirira wokhwima muuzimu: 1 Timoteyo 3:6.

**Wokonda zokoma:** Wothandizira zonse zomwe ziri zoyenera kupititsa patsogolo ntchito ya Mulungu: Tito 1:8

**Wolungama:** Wokhala bwino ndi anthu mwachilungamo osati mokondera: Tito 1:8

**Wokhazikika m'Mau:** Tito 1:9



**Woyera:** Wolungama, woyeretsedwa: Tito 1:8

**Wosakhumba chuma:** Asakhale wadyera ndi ndalama. Akhale wosakonda ndalama: Tito 1:7; 1 Timoteyo 3:3

**Woweruza bwino nyumba yake:** Aonetsere utsogoleri m'nyumba mwake: 1 Timoteyo 3:4-5

**Wokhala ndi ana okhulupirira:** Akhale ndi ana omwe amudziwa Ambuye osati opulukira: Tito 1:6

**Wa mbiri yambwino:** Akhale wambiri yabwino pakati pa osakhulupirira: 1 Timoteyo 3:7

#### **ATUMIKI:**

**Waulemu:** Akhale wodzilemekeza ndi kuonetsa chikhalidwe cha kukhwima mu nzeru: 1 Timoteyo 3:8

**Osanena pawiri:** Asakhale wonena zinthu zina kwa ena zina kwa ena: 1 Timoteyo 3:8

**Wosamwetsa vinyo:** 1 Timoteyo 3:8

**Wosakhumba chuma:** Asakhale wadyera ndi ndalama: 1 Timoteyo 3:8

**Wokhazikika m'chikhulupiriro:** 1 Timoteyo 3:9

**Ayesedwe kaye:** Akhale munthu amene wadutsa m'mayesero auzimu ndipo apezeke wopanda chifukwa: 1 Timoteyo 3:10

**Akhale wopanda chirema:** Asapezeke ndi mulandu wina uliwonse wosakhala bwino: 1 Timoteyo 3:10

**Mwamuna wa mkazi m'modzi:** Ngati ali pa banja, akhale ndi mkazi m'modzi: 1 Timoteyo 3:12

**Woweruza bwino nyumba yake:** Aonetsere utsogoleri m'nyumba mwake: 1 Timoteyo 3:12

**Wobvomerezeka:** Osati khanda muuzimu, koma wobvomerezeka ndi mpingo: 1 Timoteyo 3:10

#### **ZOYENEREZA ZINA ZOFUNIKIRA**

Izi ndi zina mwa zowayenera zoonjezera zomwe ndi zofunika kwa atsogoleri:

#### **MASOMPHENYA**

Munthu amene akutsogolera akuyenera kukhala ndi masomphenya. Masomphenya ndiko kudziwa cholinga chako mu dongosolo lake la Mulungu, kutha kumva liu lake, ndi kudziwa chifuniro ndi zolinga zake.

Paulo anali chitsanzo chabwino cha mtsogoleri wa masomphenya. Iye amatha kutsogolera anthu ena popeza anali ndi masomphenya odziwika bwino pazomwe Mulungu anamuitanira.

Kumapeto kwa utumiki wake iye anati, “Sindinakhala wosamvera ku masomphenya a kumwamba.”

Masomphenya amampanga mtsogoleri kuona zinthu za mtsogolo osati zokhazo zooneka pafupi ndi kukhulupirira Mulungu kuti achita zazikulu.

### **MAGWIRIDWE NTCHITO A PAMWAMBA**

Mtsogoleri azikhala wokhuzika ndi momwe ntchito ikugwirikira, osati mongoyerekeza kapena mopanda luso lenileni popeza ndi za Ambuye. Akuyenera kukhala wochita zinthu mwa luso komanso moonesetsa kuti zonse zayenda bwino osati waulesi ndi wosalabadira. Akhale wosunga nthawi, wochita zinthu motsindika, wolemekeza atsogoleri, ndi wodalirika.

### **WOKHAZIKIKA M’MAGANIZO**

Akhale munthu wokhazikika pa chiganizo chomwe wapanga osasinthasintha ndi zochitika wamba. Kuthekera kounika zinthu ndi kupanga chiganizo choyenera mwamsanga, ndi umboni wogwirika kuti munthuyo ali ndi utsogoleri mwa iye.

### **KUKHALA WA MSANGALA**

Kuthekera koono mbali yosangalatsa ya zinthu, kumathandizira makamaka mu nthawi zowawa.

### **KULIMBA MTIMA**

Mtsogoleri asakhale wamantha. Akhale wolimba mtima ndi kuima pamene zotsutsa zadza ndi Satana kapena anthu (Nume 6:11).

### **MAGANIZO OLONGOSOKA**

Maganizo omaona zinthu zikulephereka, amabweretsa kukhumudwitsidwa mosavuta ndipo kugonjetsedwa sikutenga nthawi. Mavuto amakhala mayeso kwa atsogoleri. Kodi amakukhumudwitsani, kukuonongani, kukugonjetsani, kapena kukutchingani kuti musachite zinthu? Atsogoleri akuyenera kukhala ndi maganizo owona zinthu zikutheka, mzimu wachilimbikitso osati wokhumudwitsa. Maganizidwe anu sakhuzi kachitidwe kanu kokha ngati mtsogoleri, ayambukira kwa anthu okutsatirani. Mtsogoleri womaona zinthu zikulephereka nakhumudwitsidwa, amakhala ndi omutsatira omaona zinthu zikulephereka ndi okhumudwa monga momwe iyeyo alili.

### **WOTHA KUSULA ANTHU**

Ntchito yaikulu ya mtsogoleri ndiyokonzekeretsa anthu ku ntchito ya utumiki (Aefeso 4:12). Munthu wotha kukonzekeretsa anthu amatha kubweretsa pamodzi anthu, kuwalimbikitsa ndi

kuwapatsa kuthekera. Amaonetsa chidwi ndi machawi mu ntchito ya Mulungu. Ndipo amalimbikitsa omutsatira kuti nawonso akhale ndi makhalidwe omwewo ku ntchito ya Mulungu. Ngati mbali imodzi yosula ndi kukonzekeretsa anthu ku utumiki, amapereka ntchito kwa anthu osati kuchita chirichonse yekha. Mtsogoleri amaumba atsogoleri ena. Wotereyu sachita nsanje kapena mantha akaona wina akuchita bwino nayamikiridwa kapena kukwezedwa paudio.

### **ULAMULIRO**

Munthu wotsogolera akuyenera kukhala wa ulamuliro panso pa ulamuliro wa Mulungu. Akuyenera kutsogolera anthu ndi mphamvu komanso ulamuliro zopatsidwa kwa iye ndi Mulungu.

### **WODZIPEREKA**

Mtsogoleri akuyenera kukhala wodzipereka kwatunthu ku ntchito ya Mulungu, Ufumu wake, kwa iwo omutsatira, komanso ntchito ya utumiki.

### **WOYAMBITSA ZINTHU**

Atsogoleri ena amangoonera zimene anthu ena akuchita, nachita zimenezo.

Ena amakhazikika pa zomwe apezeka.

Pamene ena amasinthika nayamba kuganiza monga mwa maganizo a anthu a pamalopo ndipo amateteza m'mene angathere kaganizidwe koteroka. Nanena, "Umu ndi m'mene timachitira." Koma atsogoleri abwino amayambitsa zinthu. Amakhala omasuka kusintha zinthu. Samangika mu zomwe anthu anakhazikikamo kuyambira kale. Mtundu wa mtsogoleri uyu amakhala wa waluso komanso osakopere zinthu, womasuka ku kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera kuti akachite zinthu zatsopano mu njira zatsopano. Amatha kusintha madongosolo omwe aikidwa moyenera ngati pangafunike kutero kuti ntchito ya Mulungu ipite patsogolo.

### **CHIDZIWITSO NDI NZERU**

Mtsogoleri akuyenera aonetsere kuganiza kozama popanga ziganizo ndi kuchita zinthu. Akhale ndi nzeru zokwanira kuti akathe kudziwa momwe angatsogorere. Kuthekera uku kutha kupezeka kudzera m'maphunziro, ukadaulo, ndi chitsogozo cha Mzimu Woyera.

### **MAPHUNZIRO**

Maphunziro ndi ofunikira pa utsogoleri, komabe tisaiwale kuti Yesu anasankha anthu osaphunzira. Anakhala atsogoleri a mphamvu kudzera m'mphamvu ya Mulungu.

### **UKADAULO**

Popeza kuti Yoswa anali ndi ukadaulo pa nkondo, anasankhidwa kukhala mtsogoleri wa Israel pamene amalowa m'dziko la malonjezano.

### **KUKHALA WOKONZEKA KULIPIRA DIPO**

Yesu ananena kuti pali dipo pakukhala wophunzira wake. Anachenjeza omwe ankafuna kumutsatira kuti ayambe aunika kaye dipo la kukhala wotsatira Yesu. Atsogoleri akuyenera kukhala okonzeka kusenya mtanda, kuzikaniza okha, ndi kugwira ntchito mkatikati mwa mavuto ndi kupsinjika komanso kusungulumwa.

### **MZIMU WOTUMIKIRA**

Yesu anaonetsa kuti zowayenereza atsogoleri auzimu ndi zosiyana ndi za dziko lapansi. Atsogoleri a Chikristu akuyenera kuonetsa mtima wodzichepetsa, wachifundo, wotumikira ndi kutsogolera ena monga m'busa. Izi ndi zofunika kwambiri kotero kuti maphunziro athu awiri otsatirawa akhazikika pa zoyenereza zimenezi.

### **KUDZUTSA MAKHALIDWE A UTSOGOLERI MWA INU**

Pamene mumaphunzira mndandanda wa chipatso chauzimu, ndi zoyenereza zinazi m'phunziro lino, mutha kumadzimva kuti simungakwanitse kukhala ndi makhalidwe ofunika atsogoleri. Ngati mukuganiza motero, ndi zoon. Simungakwanitse popeza si nkhani yochita kudzipanga nokha. Izi zitha kuchitika ndi mphamvu ya Mzimu Woyera yochitachita mkati mwanu. Ndipo ndi ndondomeko yomwe ndi yopitilira. Mau a Mulungu amanena kuti ndife chimango cha Mulungu. Mau oti “ndife” akuonetsera kuti ntchitoyo ikuchitikabe kudzera mu mphamvu ya kulenga ya Mulungu:

**Pakuti ife ndife cipango cace, olengedwa mwa Kristu Yesu, kucita nchito zabwino, zimene Mulungu anazipangiratu, kuti tikayende m'menemo. (Aefeso 2:10)**

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osonera.

---

---

---

2. Kodi mau oti “zoyenerenza” amanthauza chiyani?

---

---

---

3. Kodi chipatso cha kulalikirira ndi chotani?

---

---

4. Kodi chipatso cha makhalidwe ofanana ndi Khristu ndi chotani?

---

---

---

5. Onani chipatso chazimu mu mndandanda 1. Werengani kufotokozerwa kwake mu mndandanda 2. Lembani nambala ya katanthauziridwe kabwino ka chipatso chirichonse pa kanzerepo.

Mndandanda 1

- \_\_\_ Kudziletsa
- \_\_\_ Chikhulupiriro
- \_\_\_ Kufatsa
- \_\_\_ Chifundo
- \_\_\_ Kukoma mtima
- \_\_\_ Chimwemwe
- \_\_\_ Chipiriro
- \_\_\_ Mtendere
- \_\_\_ Chikondi

Mndandanda 2

- 1. Kumva chikondi chozama, kusamalira
- 2. Chimwemwe, kukondwa
- 3. Kudekha, umodzi
- 4. Kupirira kodekha
- 5. Kuupeza mtima osati wandeu
- 6. Makhalidwe a chilungamo
- 7. Kutsimikizika kwakukuru mwa Mulungu
- 8. Kudzigwira mkachitidwe ka zinthu
- 9. Kudziletsa

6. Perekani ndime zenizeni ziwiri zomwe zimafotokozerwa bwino za zowayenerenza atsogoleri zapaderadera mu mpingo.

---

---

7. Kodi ndi makhalidwe anayi ati omwe akuyenera kukhala ndi atsogoleri onse?

---

---

---

---

(Mayankho a mafunso onsewa ali kumapeto kwa bukhu lino).

## KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

1. Yesu Khristu anali ndi chipatso chonse cha Mzimu Woyera mwa Iye. Santhulani zitsanzo zotsatirazi:

Chipatso Chakunja:

- Kulalikira Yohane 10:16; Marko 1:38

Chipatso Chamkati

- Chikondi Marko 10:21; Yohane 11:5, 36
- Chimwemwe Yohane 15:11
- Mtendere Yohane 14:27
- Chipiriro 1 Petro 3:15
- Kuleza mtima 2 Akorinto 10:1
- Kukoma mtima Aroma 11:22
- Chikhulupiriro Mateyu 17:14-21
- Kufatsa 2 Akorinto 10:1
- Kudziletsa Luka 4:1-13

2. Santhulaninso zowayenereza atsogoleri zomwe mwaphunzira ndipo mupeze ndime zomwe zikuonetsera Yesu akuchita makhalidwewo.
3. Onaninso mndandanda womwe ukufotokozera zowayenereza atsogoleri m'phunziro lino. Santhulani moyo wanu. Kodi tinganene kuti muli pati?
4. Werengani nkhani ya Yesu akutembelera mtengo wa mkuyu pa Mateyu 21:18-20. Yesu sanatembelere mtengowo popeza kuti anali ndi njala ndipo kuti mtengowo unalibe zipatso. Iye amapereka phunziro lalikuru kwambiri. Mtengo wa mkuyu uja unali nawo maonekedwe okoma. Unali ndi masamba obiriwira ndipo umaoneka monga uli ndi zipatso, koma unalibe.

Kukhala ndi maonekedwe auzimu kokha sikokwanira. Atsogoleri ena amangooneka auzimu kunja kokha m'machitidwe awo koma mkati mwao alibe makhalidwe ofanana ndi Khristu. Awa ndiwo mavuto amene anali ndi Afarisi, gulu la atsogoleri a chipembedzo mu nthawi ya Yesu. Yesu anati kwa iwo:

(Mateyu 23:27)

Mulungu amayang'ana kwambiri kukhala obala chipatso mwa atsogoleri ndi okhulupirira onse, osati maonekedwe chabe ayi.

5. Onani zoyenereza zinayi zimene Mose anazinena zokhuza atsogoleri a Israel (Numenti 27:17). Amayenera kukhala amuna omwe ndi:
- Angapite patsogolo pawo: Yemwe angatsogolere.
  - Angalowe patsogolo pawo: Yemwe angawapembedzere kwa Mulungu.
  - Angawatsogolere potuluka: Yemwe angakhale patsogolo pawo ku nkondo.
  - Angawalowetse: Yemwe angawatsogolo polowa m'dziko.
  - Angapereke utsogoleri woyenera kuti “mpingo wa Ambuye usakhale monga nkhosa zopanda m'busa.”
6. Kusiyana kwa atsogoleri a dziko ndi atsogoleri auzimu:

### **Mtsogoleri wa ku dziko**

### **Mtsogoleri Wauzimu**

Wodzimva kuthekera	Wotsamira pa Mulungu
Amangodziwa anthu	Amadziwanso Mulungu
Amapanga ziganizo zake zokha	Amafuna chifuniro cha Mulungu
Wodzikuza	Wodzichepetsa
Wa nzeru zayekha	Wotsata njira za Mulungu
Amamva bwino anthu akamamvera	Amamvera Mulungu
Amatsogozedwa ndi zokhumba zake	amatsogozedwa ndi chikondi
Wodzidalira yekha	Wodalira Mulungu.

7. Miyambo 28 amasiyanitsa mtsogoleri wabwino ndi mtsogoleri woyipa:

### **MTSOGOLERI WABWINO**

- Ndi wokhazikika ndi wolimba mtima (sathawa)	vesi 1-2.
- Amaima pa choonadi posayang'ana zolimba	vesi 4
- Amasunga malamulo	vesi 4, 9.
- Amafuna bvumbulutso la Mulungu mu zonse	vesi 5, 11
- Amakondweretsa makolo	vesi 7
- Ndi woona mtima	vesi 6, 8
- Ndi munthu wa pemphero	vesi 9
- Wochita bwino mu zonse zabwino	vesi 10, 20, 25
- Munthu womvetsa zinthu mosamalitsa	vesi 11
- Wobweretsa chimwemwe pamalo	vesi 12
- Amabvomereza machimo ake	vesi 13
- Amaopa Mulungu	vesi 14
- Wopanda chisiliro	vesi 16
- Amatsogolera kwa nthawi yaitali	vesi 16
- Wamtendere	vesi 17
- Amayenda moongoka mtima	vesi 18
- Wachangu	vesi 19
- Wokhulupirika	vesi 20



- Wosapembedza anthu	vesi 21
- Sachita mantha ndi chidzudzulo	vesi 23
- Amaika banja lake patsogolo	vesi 24
- Wodzichepetsa ndi kudalira pa Ambuye	vesi 25
- Amadalira chitsogozo cha Mulungu	vesi 26
- Wachifundo pa anthu omuzungulira	vesi 27
- Amathandiza olungama kuti akule	vesi 28

## **MTSOGOLERI WOYIPA**

- Wamantha kuthawa popanda chifukwa	vesi 1
- Wosakhazikika	vesi 1-2
- Wopondereza osauka	vesi 3
- Wodzikuza ndi wotchuka pakati pa oyipa	vesi 4
- Wosazama mchidziwitso	vesi 3
- Wopanda chifundo ndi anthu	vesi 3, 27
- Wosalabadira malamulo	vesi 4
- Samvetsa bwino zinthu	vesi 5, 16
- Wa machitidwe a chitayiko	vesi 6, 18
- Bwenzi la osalungama	vesi 7
- Womvetsa chisoni makolo	vesi 7
- Wopeza chuma mwachinyengo	vesi 8, 20, 22
- Wosakonda pemphero	vesi 9
- Wosokeretsa olungama	vesi 10
- Wanzeru mwayekha	vesi 11
- Wochititsa mantha akakhala pa mpando	vesi 12, 28
- Wobisa machimo ake	vesi 13
- Woumitsa mtima wake	vesi 14
- Wolamulira ngati mkango wokwiya	vesi 15
- Wachiwawa	vesi 15, 17
- Wachisiliro	vesi 16
- Amagwa mosavuta	vesi 10, 18
- Amakhala wosaweruzika	vesi 14
- Waulesi ndi wolamulidwa ndi anthu oyipa	vesi 19
- Waziphuphu ndi wopembedza anthu	vesi 21
- Wolakwa	vesi 20
- Amakhala wosauka muuzimu	vesi 22
- Wonyengeka	vesi 23
- Saika patsogolo banja lake	vesi 24
- Wamwano	vesi 25
- Wobweretsa mikangano pamalo	vesi 25
- Wodalira kuthekera kwake osati Mulungu	vesi 26
- Wophwasula osati kumangilira	vesi 24
- Wosaganizira ogwira nawo ntchito	vesi 27

## **CHAPUTALA 5**

### **KUTSOGOLERA MONGA KAPOLO**

#### **ZOLINGA:**

Mukamaliza phunziro lino muzikwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera.
- Kupeza mtundu umodzi wa utsogoleri womwe ndi wa Chikhristu basi.
- Kudziwa chitsanzo chimodzi chachikuru cha utsogoleri wotumikira.
- Kufotokozero momwe kutsogolera ngati wotumikira kumapangira munthu kukhala wamphamvu.
- Kulemba kusiyana kunayi kwa pakati pa atsogoleri a Chikhristu ndi a dziko lapansi.
- Kudziwa yemwe tikumtumikira.
- Kufotokozero momwe tingakhalire atumiki atsogoleri otumikira.

#### **MAVESI OTSOGOLERA**

**Mukhale nao mtima m'kati mwanu umene unalinso mwa Kristu Yesu, ameneyo, pokhala nao maonekedwe a Mulungu, sanaciyesa colanda kukhala wofana ndi Mulungu, koma anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe akapolo, nakhala m'mafanizidwe a anthu; (Afilipi 2:5-7)**

#### **MAU OYAMBA**

Utsogoleri pa dziko lapansi umayendera limodzi ndi ndalama, mphamvu, maphunziro kapena ukadaulo. Ndipo pali machitidwe osiyanasiyana a utsogoleri pa dziko lapansi. Machitsanzo, ulamuliro wa nkhanza ndi ulamuliro wa demokalase womwe anthu amakhala ndi ufulu wosankha anthu omwe akufuna kuti awalamulire pochita masankho.

Yesu atabwera pa dziko lapansi anasanduliza dodolido kamvetsedwe komwe anthu anali nako kokhuza utsogoleri pokhala moyo wonga kapolo. Chaputala chino chikukamba za mfundo za m'Chipangano Chatsopano za kutsogolera monga kapolo.

#### **CHITSANZO CHOSIYANITSA**

Yesu anasiyanitsa utsogoleri wa dziko lapansi ndi utsogoleri wauzimu. Iye anati:

**Ndipo Yesu anawaitana, nanena nao, Mudziwa kuti iwo amene ayesedwa ambuye a mitundu ya anthu amacita ufumu pa iwo; ndipo akuru ao amacita ulamuliro pa**

**iwo. Koma mwa inu sikutero ai; kama amene ali yense afuna kukhala wamkuru mwa inu adzakhala mtumiki wanu; ndipo amene ali yense afuna kukhala woyamba mwa inu adzakhala kapolo wa onse. (Marko 10:42-44)**

Kutsogolera monga kapolo ndi komwe kumasiyanitsa utsogoleri wa Chikhristu ndi utsogoleri wa dziko lapansi. Utsogoleri wa Chikhristu ndi wokhawo womwe ndi wosiyana ndi mautsogoleri ena onse.

### **CHITSANZO CHACHIKULU**

Chitsanzo chachikulu kwambiri cha kutsogoleri monga kapolo ndi Ambuye Yesu Khristu. Kapolo ndi munthu amene amatumikira ena modzichepetsa, modzipereka, ndi mwa chikondi. Yesu anaphunzitsa ndi kuonetsera momwe utsogoleri wotumikira umakhalira. Iye anakana maganizo onse okhuza momwe anthu amatsogolerera nabweretsa mtundu wina wa utsogoleri. Mau oti “kapolo” ndi achilendo kwambiri pa nkhani ya utsogoleri, koma Yesu ananena momveka bwino kuti anabwera kuti akatumikire:

**Koma sipadzatero ndi inu; komatu iye ali wamkuru mwa inu, akhale ngati wamng'ono; ndi iye ali woyamba, akhale ngati wotumikira. (Luka 22:26)**

Marko akunenanso kuti Yesu anabwera osati kuti akatumikiridwe koma kuti akatumikire:

**Pakuti ndithu, Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa, koma kutumikira, ndi kupereka moyo wace dipo la kwa anthu ambiri. (Marko 10:45)**

Paulonso akuphera mphongo pa nkhani yomweyi:

**koma anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe akapolo, nakhala m'mafanizidwe a anthu; (Afilipi 2:7)**

### **KULONDOLA MAPAZI**

Atsogoleri a mu mpingo woyamba anatsata mapazi a Yesu pa utsogoleri wawo. Anadzitchula okha kuti ndi akapolo:

- Paulo, kapolo wa Yesu Khristu... (Aroma 1:1)
- Yakobo, kapolo wa Mulungu...ndi Khristu. (Yakobo 1:1)
- Petro, kapolo wa Yesu Khristu. (2 Petro 1:1)
- Yuda, kapolo wa Yesu Khristu. (Yuda 1)
- Lolani akapolo anu kukalankhula mau ndi kulimbika mtima. (Machitidwe 4:29)

Ifenso tikuyenera kulondola mapazi omwewa. Tikhale akapolo a iwo amene tikuwatumikira.

### **MPHAMVU ZA KAPOLO**

Mwina mutha kumadzifunsa kuti, “Kodi ndingakhale bwanji mtsogoleri ngati ndikuwatumikira anthuwo ngati kapolo? Ndiye kuti ndikutsogoleranso pamenepo? Chifukwa chiyani tikutsindika kwambiri nkhani yotumikira?” Yankho la mafunso onsewa ndi lakuti kutumikira mwa ukapolo muli mphamvu. Kutsogolera ngati kapolo sikutanthauza kuti utsogoleri wanu ndi wofooka ayi. Komanso sizikutanthauza kuti utsogoleri ukhale wa lobodolobodo potsutsana ndi adani auzimu.

Mphamvu yake yagona pakuti utsogoleri wa ukapolo umamchepetsa munthu kufika pa mulingo wakuti Mulungu amugwiritse ntchito. Izi zikuonekeranso m’ moyo wa Yesu Khristu. Werengani Afilipi 2:5-11. (Musanthula za izi bwino lomwe patsogolopa m’phunziro lomwe lino). Ndime iyi ikutionetsera momwe Yesu analandilira mphamvu ndi ulamuliro kudzera mu kudzichepetsa yekha ngati kapolo ndi kufa pa mtanda (vesi 5-8), Yesu anakwezedwa mu mphamvu zazikulu (vesi 9-11). Palibe munthu amene amayembekezera kuti mtsogoleri angapachikidwe pa mtanda, koma mtanda unakhala mphamvu ya Mulungu ya kupulumutsa (1 Akorinto 1:18). Zinthu zambiri mu Ufumu wa Mulungu zimakhala zotembenezidwa. Timakhala a mphamvu pamene tili ofooka, timalandira tikapereka, timakhala ndi moyo pakufa. Ngati mtsogoleri, mumakhala wa mphamvu mukamatumikira ngati kapolo.

### **MAGAWO ANAYI A KUSIYANA**

Werengani Mateyu 20:25-28 ndi Marko 10:42-44. Ndime zimenezi zikuonetsera zinthu makhalidwe anayi a kusiyana kwa utsogoleri wa Chikhrstu ndi wa dziko lapansi:

1. Atsogoleri a dziko amalamulira anthu owatsatira. Atsogoleri otumikira samapondereza owatsatira.
2. Atsogoleri a dziko amakhala ndi ulamuliro pa owatsatira. Mau oti “ulamuliro” mu chiganizo ichi akuimilira mphamvu. Iwo amadziona kukhala pamwamba pa owatsatira. Koma atsogoleri a Chikhrstu amaitanidwa kukatumikira osati kukatumikiridwa.
3. Atsogoleri a dziko ndi mafumu a otsatira awo. Mau oti “mfumu” mu ndime imeneyi amatanthauza kukhala patsogolo. Mu Ufumu wa Mulungu, oyamba (atsogoleri0 amakhala otsiriza.
4. Atsogoleri a dziko amakhala ambuye kwa iwo owatsatira. Mau oti “ambuye” amatanthauza kwa iwo ofunika kutumikiridwa. Mtsogoleri wa Chikhrstu amatumikira omutsatira.

### **KODI TIMATUMIKIRA NDANI?**

Ngati atumiki otsogolera, timatumikira thupi la Khristu. Paulo anauza anthu a ku Akorinto:

**Pakuti tilalikira si za ife tokha, koma Kristu Yesu Ambuye, ndi ife tokha akapolo anu, cifukwa ca Kristu. (2 Akorinto 4:5)**

Timatumikiranso mtundu wa anthu womwe ukutayika ndi kufa. Werengani fanizo la Msamariya wa chifundo mu Luka 10:25-37. Kukhala ndi mzimu wotumikira kumabweretsa mphamvu ndi ulamuliro chifukwa pamene tikutumikira ena timakhala tikutumikira Ambuye.

**Indetu, indetu, ndinena ndi inu, Kapolo sali wamkulu ndi mbuye wace; kapena mtumwi sali wamkuru ndi womtuma iye, (Yohane 13:16)**

### **KODI MUNGAKHALE BWANJI MTSOGOLERI WOTUMIKIRA**

Werengani Afilipi 2:5-8. Ndimeyi imafotokozera za momwe mungakhalire mtsogoleri wotumikira pa kutsatira chitsanzo cha Ambuye Yesu. Kuti mtsogolere ngati mtumiki mukuyenera:

### **KUKHALA NDI MAGANIZO OYENERA**

Kutumikira ngati mtsogoleri kumayamba ndi momwe munthu amaganizira. Mukuyenera kukhala ndi maganizo onga a Khristu:

**Mukhale nao mtima m'kati mwanu umene unalinso mwa Kristu Yesu, ameneyo, pokhala nao maonekedwe a Mulungu, sanaciyesa colanda kukhala wofana ndi Mulungu, koma anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe akapolo, nakhala m'mafanizidwe a anthu; (Afilipi 2:5-7)**

Mulungu amagwiritsa ntchito anthu omwe mtima ndi maonedwe awo a zinthu ndi oyenera. Davide anadzodzedwa kukhala mfumu popeza Mulungu anaona mtima wake (1 Samuel 16:7). Zolinga zimachokera mu mtima. Zolinga zathu ngati anthu nthawi zambiri ndi zodzikonda. Ngati mukufuna kukhala mtsogoleri wotumikira, zolinga komanso maganizo anu zikuyenera kukhala zosinthika.

### **DZICHEPETSANI NOKHA**

**koma anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe akapolo, nakhala m'mafanizidwe a anthu; (Afilipi 2:7)**

Musatanganidwe ndi zokhumba, malingaliro, udindo kapena mbiri yanu. Ziperekeni zonsezi kwa Ambuye ndi kudzichepetsa nokha. Izi ndi zoti mukuyenera kuchita ndi inu osati Mulungu.

### **KHALANI MU ZOMWE ANTHU ALI**

Yesu anakwanitsa kutsogolera ngati mtumiki pokhala pakati pa anthu mu zomwe iwo ali ndi kukwaniritsa zosowa zawo:

**koma anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe akapolo, nakhala m'mafanizidwe a anthu; ndipo popezedwa m'maonekedwe ngati munthu, anadzicepetsa yekha, nakhala womvera kufikira imfa, ndiyo imfa ya pamtanda. (Afilipi 2:7-8)**

Yesu anayesedwa monga munthu, anazunzika monga munthu, ndipo thupi lake linali nazo zofooka ndi zosowa za ngati munthu aliyense. Ngati mungatumikire iwo amene mukuwatsogolera, mukuyenera kukhala mu zomwe anthuwo ali, mu zofooka zawo, mazunzo awo komanso zosowa zawo.

### **KHALANI OMVERA**

Yesu anakhala womvera kuti akatumikire:

**ndipo popezedwa m'maonekedwe ngati munthu, anadzicepetsa yekha, nakhala womvera kufikira imfa, ndiyo imfa ya pamtanda. (Afilipi 2:8)**

Yense wokhala ndi ulamuliro ngati mtsogoleri alinso pansu pa ulamuliro wa utsogoleri. Ngati mtsogoleri wa Chikhristu, muli pansu pa ulamuliro wa Mulungu. Muthanso kukhala ndi pansu pa mtsogoleri wa mpingo wanu. Kuti mutumikire bwino ngati mtsogoleri, mukuyenera kukhala omvera kwa atsogoleri anu.

### **IFANI KU UCHIMO NDI KU THUPI LANU**

Yesu anakhala omvera kufikira imfa:

**ndipo popezedwa m'maonekedwe ngati munthu, anadzicepetsa yekha, nakhala womvera kufikira imfa, ndiyo imfa ya pamtanda. (Afilipi 2:8) (Afilipi 2:8)**

Paulo anati, “ndikufa tsiku ndi tsiku” (1 Akorinto 15:31). Kufa kumene Paulo akulankhula apa ndi kufetsa thupi la uchimo nthawi ndi nthawi. Izi ndi zomwe zikufunika kwa iwo amene angatsogolere potumikira. Mukuyenera kupachika tchimo ndi umunthu wake. Kusenza mtanda ndi kowawa, komabe monga momwe Yesu anachitira, muphunzira mfundo za utsogoleri wa kutumikira kudzera nkupirira.

### **TUMIKIRANI MWA CHIKONDI**

Chifukwa cha chikondi chake chachikulu, Yesu anadzicepetsa yekha, natenga maonekedwe a kapolo, nakhala ngati munthu ndi kumvera kufikira imfa:

**Umo muli cikondi, sikuti ife tinakonda Mulungu, koma kuti iye anatikonda ife, ndipo anatuma Mwana wace akhale ciombolo cifukwa ca macime athu.**

**Okonedwa, ngati Mulungu anatikonda ife kotero, ffenso tiyenera kukondana wina ndi mnzaceo (1Yohane 4:10:11)**

Chikondi ndichofunika kwambiri pa kutsogolera ngati mtumiki. Chikondi chimayamba mu mtima, kenako chimadzaonekera kunja mu zochita za munthu zoonekeratu. Ngati munthu wamkonda kwambiri umakhala wokonzeka kumtumikira.

Mtsogoleri wotumikira amalimbikitsa anthu amene akuwatumikira. Samawagwiritsa ntchito koma kugwira nawo limodzi ntchito mowathandiza moyo wao wauzimu kuti ukule. Iye amapereka m'malo momangotenga. Kuphwasula kumakhala kosavuta koma kumanga kumatenga nthawi ndipo ndi kovuta.

Werengani 1 Akorinto 13 ndipo paliponse pomwe pali mau oti “chikondi” muikepo mau akuti “mtsogoleri wotumikira.” Mwachitsanzo, “Mtsogoleri wotumikira amapirira.” Izi zikuthandizani kuti mumvetse bwino za tanthauzo la chikondi chomwe chimayenera kuonekera mwa atsogoleri otumikira.

### **MUOLENI MULUNGU AKHALE PATSOGOLO**

Yesu atabwera ku dziko lapansi ngati kapolo, anasiya ufulu wake wakukhala bwana wa moyo wake. Ananena kuti, “Osati chifuniro change koma chanu chichitike.” Mukasankha kukhala kapolo, mumasiya ufulu wokhala wolamulira moyo wanu. Simukhalanso mukumanga ufumu wanu wanu koma Ufumu wa Mulungu. Simukhalanso mukuphunzitsa maganizo kapena zikhulupiriro zanu koma uthenga wa Mbuye wanu. Osati chifuniro chanu koma chifuniro cha Mulungu. Yesu anabwera kudzatumikira mwa kusankha yekha. Tsopano chisankho ndi chanu. Musankha kutumikira kodi? Kumbukirani: Mumadaliridwa ndi udindo wotsogolera molingana ndi mlingo wa momwe mumadzipekera potumikira.

## MAFUNSO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osonera.

---

---

2. Kodi ndi utsogoleri uti umodzi womwe ndi Chikhristu basi?

---

---

3. Kodi chitsanzo chachikulu cha utsogoleri wotumikira ndi ndani?

---

---

4. Fotokozerani momwe kutsogolera motumikira kumabweretsera mphamvu.

---

---

---

5. Lembani kusiyana kunayi kwa utsogoleri wa Chikhristu ndi wa dziko.

---

---

6. Kodi ngati atsogoleri, timatumikira ndani?

---

---

7. Pogwiritsa ntchito Afilipi 2:5-8, fotokozerani momwe mungakhalire mtsogoleri wotumikira.

---

---

---

---

(Mayankho a mafunso onsewa ali kumapeto kwa bukhu lino)



## **KUPITIRIZA KUPHUNZIRA**

Werengani vesi ili:

(Aroma 14:18).

Vesi ili likuonetsera zotsatira za utsogoleri wabwino:

1. Kutumikira Khristu, komwe kumapangitsa...
2. Kulandiridwa ndi Mulungu ndi...
3. Kubvomerezedwa ndi anthu.

Tsopano santhulani Aroma 12 mpaka 14. Lembani mndandanda wa zinthu zomwe mukuyenera kuchita kuti mukhale mtumiki wa Khristu yemwe walandiridwa ndi Mulungu ndi kubvomerezedwa ndi anthu. Tsatirani chitsanzo chiri m'musichi

**NDIME**

**NDICHITE CHIYANI**

Aroma 12:1

Kupereka thupi langa ngati nsembe yamoyo, yoyera ndi yobvomerezeka kwa Mulungu.

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

---

## CHAPUTALA 6

### KUTSOGOLERA NGATI M'BUSA

#### ZOLINGA

Mukamaliza phunziro lino muzikwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kudziwa M'busa Wabwino
- Kudziwa gulu lenileni limodzi la nkhoa
- Kulemba mwachidule ntchito za m'busa
- Kulemba mwachidule machenjezo a m'busa woipa
- Kugwiritsa ntchito maluso a ubusa wa kuthupi mu utsogoleri.

#### MAVESI OTSOGOLERA

**Wetani gulu la Mulungu liri mwa inu, ndi kuliyang'anira, osati mokangamiza, koma mwaufulu, kwa Mulungu; osatsata phindu lonyansa, koma mwacangu; osati monga ocita ufumu pa iwo a udindo wanu, koma okhala zitsanzo za gululo. (1 Petro 5:2-3)**

#### MAU OYAMBA

Chitsanzo china cha kuthupi chofotokozera bwino utsogoleri ndi cha ubusa. Ku thupi, m'busa ndi munthu yemwe amayang'anira nkhoa. Ndipo anthufe timayerekezedwa ndi gulu la nkhoa muuzimu. Mwina ndife nkhoa zosokera (Yesaya 53:6) kapena ndife mbali imodzi ya nkhoa zomwe ziri “m'gulu” la nkhoa za Ambuye.

Yesu amadzitchula yekha kuti ndi “M'busa Wabwino” ndipo anafotokozera mwa tsatanetsatane zomwe zimachitika mu ubusa. Nkhani ya ubusa ndi chitsanzo chabwino kwambiri cha utsogoleri wauzimu (onani Yohane 10). Kuti mukhale mtsogoleri wamphamvu, mukuyenera kuphunzira kutsogolera ngati mtumiki.

Peter akutsimikizira kuti tikuyenera kutsogolera ngati abusa:

**Wetani gulu la Mulungu liri mwa inu, ndi kuliyang'anira, osati mokangamiza, koma mwaufulu, kwa Mulungu; osatsata phindu lonyansa, koma mwacangu; (1 Petro 5:2)**

#### MFUNDO ZA UBUSA

Popeza Yesu anadzitchula yekha “M’busa Wabwino” ndiye kuti tikuyenera kutengapo chitsanzo cha utsogoleri kuti timvetse mfundo za ubusa. Tsegulani pa Yohane 10 m’Baibulo mwanu ndipo igwiritseni ntchito pamene mukusanthula mfundo zofunikira za ubusa:

### **GULU LIMODZI, M’BUSA M’MODZI**

Mfundo yoyamba yofunika kuimvetsa ndi yakuti pali gulu limodzi la nkhusa ndipo palinso m’busa m’modzi. “Gulu” ndi mpingo womwe ndi onse amene anatembenuka mtima. Ndipo “M’busa” ndi Yesu Khristu. Ndipo khomo lolowera mu gulu limeneli ndi limodzi lokha, Yesu Khristu:

**Ine ndine khomo; ngati wina alowa ndi Ine, adzapulu-mutsidwa, nadzalowa, nadzaturuka, nadzapeza busa. (Yohane 10:9)**

**Ndipo nkhusa zina ndiri nazo, zimene siziri za khola ili; izinso ndiyenera kuzitenga, ndipo zidzamva mau anga; ndipo zidzakhala gulu limodzi, mbusa mmodzi, (Yohane 10:16)**

Azibusu amagawa nkhusa zawo kuzisiyanitsa ndi nkhusa zina kuti zisamavute kuzisamalira. Amatha kusamalira nkhusa zambiri. Chimodzimodzinsu ku utsogoleri wakuuzimu. Komano pali gulu limodzi lokha. Ndipo gululi lapangidwa ndi okhulupirira enieni omwe ndi a M’busa Wabwino, Yesu Khristu. Ngati mtsogoleri kapena “m’busa,” ndiwe “m’busa wamng’ono.” Umatsogolera gali lina lake la nkhusa zake pansu pa ulamuliro wa M’busa Wabwino. Kumbukirani nthawi zonse kuti kugawikana kwa mipingo ndi kapena magulu opempherera kunapangidwa ndi anthu mbali ina ndi cholinga chakuti nkhusa zizisamaliridwa moyenera komanso pazikhala dongosolo labwino mu kachitidwe ka zinthu. Koma chilungamo chake ndi chakuti pali gulu limodzi lokha.

Musamagawe anthu mu gulu la nkhusa za M’busa Wabwino ndi zipembedzo. Musadzimangire nokha “gulu lanu” la chipembedzo kapena mpingo. Koma mangani gulu la M’busa Wabwino. Musaike malamulo omwe apangitse nkhusa zina zibalalike. Yesu ananena kuti wina aliyense amene afuna, abwere kwa Iye koma akhale kuti akudzera pakhomo ndiye Ambuye Yesu Khristu mwini.

Gulu la nkhusa la Mulungu si losankhidwiratu. Khomo ndi lotseguka ku nkhusa zonse:

**Ndipo nkhusa zina ndiri nazo, zimene siziri za khola ili; izinso ndiyenera kuzitenga, ndipo zidzamva mau anga; ndipo zidzakhala gulu limodzi, mbusa mmodzi, (Yohane 10:16)**

## **MULUNGU NDIYE AMENE AMAPEREKA NKHOSA**

Popeza kuti pali gulu limodzi lokha, nkhusa zonse zimaperikedwa ndi Mulungu:

**Atate wanga, amene anandipatsa izo, ali wamkulu ndi onse; ndipo palibe wina angathe kuzikwatula m'dzanja la Atate. (Yohane 10:29)**

Otsatira anangoperikedwa kwa ife ndi Mulungu kuti tikawasamalire koma ndi nkhusa za Mulungu.

## **NKHOSA ZINA SIZIBWERA**

Pali chinthu china chomvetsa chisoni chomwe ngati m'busa mukuyenera kuchidziwa. Ena amene ayitanidwa adzakana kubwera. Yesu anati:

**Koma inu simukhulupira, cifukwa simuli a mwa nkhusa zanga. (Yohane 10:26)**

Pali ena amene ayitanidwa koma adzakana kumtsatira. Adzakana kukhala mbali imodzi ya gululi. Ndi zomvetsa chisoni koma ndi zooni. Koma musataye mtima. Tsogolerani iwo amene apatsidwa kwa inu.

## **M'BUSA AMADZIWA NKHOSA ZAKE**

Yesu anati:

**Ine ndine Mbusa Wabwino; ndipo ndizindikira zanga, ndi zanga zindizindikira ine, (Yohane 10:14)**

Mu nthawi ya utumiki wa Yesu, abusa amakhala pa ubale wabwino kwambiri ndi nkhusa zawo. Nkhusa ikamabadwa m'busa amakhalapo kuti ayisamalire kufikira moyo wake wonse. Kuti mukhale mtsogoleri wabwino mukuyenera kudziwa nkhusa zomwe Mulungu wakupatsani muzisamalire. Muonesetse kuti pakhale ubale wabwino ndi nkhusazo. Yesu anati M'busa Wabwino “amaitana nkhusa zake ndi dzina.” (Yohane 10:3)

## **NKHOSA ZIMADZIWA M'BUSA**

Pamene m'busa akudziwa nkhusa zake, nkhusazo zimadziwanso m'busa wao:

**Nkhusa zanga zimva mau anga, ndipo Ine ndizindikira, ndipo zinditsata Ine. (Yohane 10:27)**

Yesu anena kuti nkhusa zimadziwa mau a m'busa. Zimamva ndi kumtsatira popeza zimamdzwa ndi kumkhulupirira.

Ngati m'busa mukuyenera kuonesetse kuti pali kukondana ndi kukhulupirirana pakati pa inu ndi nkhusa zanu. Kuti izi zitheke, mukuyenera kupezeka pakati pa nkhusa zanu osati kumadzipatula.

Nkhosa zionere makhalidwe abwino kwa inu pamene muli pakati pawo pamene mukutsatira Khristu:

**Ndipo ndikutamandani kuti m'zinthu zonse mukumbukila ine, ndi kuti musunga miyambo monga ndinapereka kwa inu. (1 Akorinto 11:1)**

Anthu sikuti amatsatira munthu popeza kuti ndi mtsogoleri ayi. Mukuyenera kuwapanga kuti akukhulupirireni kuti muwatsogolere bwino. Izi zimachitika pamene muwalola kuti akudziweni.

### **M'BUSA AMASAMALIRA NKHOSA**

Abusa abwino amasalira nkhusa zawo. Mukuyenera kusamalira miyoyo ya nkhusa zanu.

Mukuyenera kuonesetsa kuti miyoyo ya nkhusa zanu yabwezeretsedwa ku ubale wabwino ndi Mulungu:

**Atsitsimutsa moyo wanga; Anditsogolera m'mabande a cilungamo, cifukwa ca dzina lace. (Masalimo 23:3)**

Kusamalira nkhusa ndiko kuzitonhoza mu nthawi ya chisoni ndi zosowa. M'busa amagwiritsa ntchito ndodo kuti afikire ndi kukoka nkhusa yogwera m'mbuna kuti ayione ngati yavulala ndi kuitonhoza (Masalimo 23:4)

Kusamilira anthu ndiko kuwatsogolera kwa Khristu, M'busa Wabwino, yemwe angakwaniritse zosowa zawo zonse.

**Masalimo 23:1 Yehova ndiye mbusa wanga; sindidzasowa. (Masalimo 23:1)**

Davide polankhula za Mulungu monga m'busa wake muuzimu anati:

**Andigonetsa ku busa lamsipu: Anditsogolera ku madzi ndikha. (Masalimo 23:2)**

Pamene nkhusa zasamaliridwa bwino, zimagona pansu ndi kukhutira. Nkhusa, ku thupi ngakhale kuuzimu, zimagona pansu pokhapokha:

**Palibe chinthu chochititsa mantha:** Mantha a pa munthu kapena mdani amabalalitsa nkhusa.

Mukuyenera kuphunzitsa nkhusa kuti:

**pofuna kukhala aphunzitsi a lamulo ngakhale sadziwitsa zimene azmena, kapena azilimbikirazi. (1 Timoteyo 1:7)**

**Pamene palibe kulimbana ndi nkhusa zina:** Nkhusa zomangokhalira kulimbana sizimadya mokwanira kapena kupumula. Komanso simabala muuzimu. Mu nthawi ya anthu akale a m'Baibulo, nkhusa zikayamba kumenyana m'busa amaika mafuta pa mutu pa nkhusazo omwe amangitsa kuti pazitelera. Kotero sizimagundananso nkumamenyana. Phunzitsani nkhusa kuti zizilimbana ndi mdani osati zokhazokha. Pakani mafuta a Mzimu Woyera pamitu pawo.

**Pamene palibe tizirombo toluma.** Kuthupi, kuli tizirombo tina tomwe timabisala mu ubweya wa nkhusa ndipo timaluma nkhusazo ndi kusowetsa mtendere nkhusa kapena kuzidwalitsa kumene. Zina zimaikira mazira ndikuswa ndipo tiana taketo timalowa m'maso mwa nkhusa ndi kubweretsa khungu kapena kupha kuphene nkhusayo.

Davide ananena kuti m'busa “anadzodza mutu wake ndi mafuta” (Masalimo 23:5). Nthawi imeneyo nkhusa zimagwiritsa ntchito mafuta potsuka nkhusa ngati zili ndi matenda a pakhungu kapena matenda ena aliwonse. Koma kuuzimu, tiziromboti tikhoza kuyerekezedwa ndi uchimo. Uchimo umapangitsa khungu ndi imfa. Mafuta a Mzimu Woyera akuyenera kugwiritsidwa ntchito kuchotsa tizirombo tauchimo pakati pa nkhusa.

Pamene palibe njala ndi ludzu: Ngati mukufuna kuti nkhusa zikhalebe mgulu pamodzi ndi zinzawo, mukuyenera kumazidyetsa mokwanira bwino. Mtsogoleri azitengere nkhusa ku msipu wobiriwira ndi kuzidyetsa ndi choonadi cha Mau a Mulungu:

**Wetani gulu la Mulungu liri mwa inu, ndi kuliyang'anira, osati mokangamiza, koma mwaufulu, kwa Mulungu; osatsata phindu lonyansa, koma mwacangu; (1 Petro 5:2)**

Kutsogolera anthu ku msipu wobiriwira kokha sikokwanira. Mukuyeneranso kuwapanga kuti agone pansu ndi kusalabadiranso zinthu zina. Mukuyenera kuwayalira gome la zinthu zabwino za Mulungu (Masalimo 23:5). Mukuyenera kutsogolera nkhusa ku madzi osatha (Yohane 4) omwe athetse ludzu lawo. Dzadzani zikho zawo ndi Mau a Mulungu kufikira kusefuka (Masalimo 23:5).

Kuthupi, nkhusa zikakhala ndi ludzu zimanka ziyendayenda kufunafuna madzi. Ngati sizitsogoleredwa ku madzi abwino, zimakamwa madzi oyipa. M'busa amayenera kuzilondora ndi kuonesetsa kuti zisamwe madzi oyipa komanso zisadye zomera zakupha zokhala m'mbali mwa akasupe. Ngati m'busa, tsogolerani nkhusa zanu ku madzi abwino. Yesu anati:

**Koma tsiku lomariza, lalikirulo la phwando, Yesu anaimirira napfuula, ndi kunena, Ngati pali munthu akumva Ludzu, adze kwa Ine, namwe. (Yohane 7:37)**

Yeremiya analankhula za “zitsime zopanda madzi.” Zitsime zimenezi zikuyenera kudzadzidwa ndi madzi a moyo (Yeremiya 2:13).

Ndi zosangalatsa kuona pa Masalimo 23:2 kuti m'busa akutsogolera nkhusa ku “madzi odikha.” Madzi odikha amatanthauza madzi oyenda ndithu koma mopanda phokoso. Madzi amenewa amakhala oyera ndi okoma. Si madzi ongokhazikika omwe amakhala a pfungo loipa ayi. Awa

ndi abwino. Komanso si madzi othamanga mwamphamvu omwe amaononga zinthu ayi. Koma a phee. Izi zikutanthauza chiphunzitso chokhazikika cha Baibulo chosasunthika ndi mphempho za mkuntho za ziphunzitso zongofuna kukopa anthu.

### **M'BUSA AMALANGA NKHOSA**

Kusamalira nkhoa kumaphatikizaponso kulanga. Ndodo zimene abusa amatenga zimakhala zokusira nkhoa ku njira yoyenera. Sizikhala zokondweretsa ku nkhoa koma ndi zoyenera. Ndodo ya m'busa wa nkhoa zakuthupi, ndi chitsanzo chabwino cha ulamuliro wa Mau a Mulungu wokhala pa m'busa wauzimu. Ndodo imasungitsa mwambo. Siikhala yokoma nthawi zonse, koma ndi yoyenera.

Kutsogolera kumaphatikizapo kulanga, kudzudzula ndi kuongolera kuti nkhoa zikhale pa njira yoyenera. Nkhosa zikasokera, kusamalira kumaphatikizapo kuzilondola ndi kukazichotsa ngakhale mozikakamiza kuti zibwerere m'khola (Luka 15). Zitsogolereni nkhoa kuchoka mu uchimo kukhala mu chilungamo:

**Atsitsimutsa moyo wanga; Anditsogolera m'mabande a cilungamo, cifukwa ca dzina lace. (Masalimo 23:3)**

Nkhosa zimati zikasiyidwa zokha zimalowerera. Zimatha kumangodya malo amodzi omwewo mpaka msipu kutha kapena kubalalika kunka kumadera a kutali. Izi ziri chimodzimodzi ndi anthu:

**Tonse tasocera ngati nkhoa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa Iye mphulupulu ya ife tonse. (Yesaya 53:6)**

Potsogolera anthu ku njira za chilungamo, mumakhala mukuongolera kuti zikayende mu njira za Mulungu.

### **M'BUSA AMADZUTSA NKHOSA ZOMWE ZAGWA**

Nkhosa za kuthupi zimatha kugwa pansu chagada ndikumakanika kudzukanso yokha. Zikatero nkhosayo imakhala pa ngozi yodyedwa ndi chirombo mosavuta. M'busa akuyenera kubwera ndi kuithandizira ndi ndodo yake kuidzutsa.

Kugwaku kumachitika pamene:

**Nkhosa zakomedwa ndi kukhuta msipu:** Zimadzigwetsa dala ndi kumagubuduzika mosangalala koma kenako nkumakanika kudzukanso. Kuuzimu, okhulupirira amatha kukhazikika m'chuma ndi kutengeka ndi zokoma za dziko lapansi osalabadiranso za Mulungu, Ufumu wake, kapena miyoyo ya anthu otayika. Zikatero sakhala achangu ndi amphamvu ku



ntchito ya utumiki ndipo amakhala pa ngozi yolikhwiridwa ndi mdani. Nkhosa zoterezi zithandizeni pozionetsera kufunikira kochita zinthu zomwe zokhala ndi phindu lamuyaya ndi kuwalimbikitsa kuchita ntchito ya mu Ufumu.

Nkhosa ziri ndi ubweya wochuruka: Pamene ubweya wa nkhusa wakula modutsa mulingo, imayangidwa ndi zinthu monga minga, zitsotso ndipo imayamba kulemedwa ndi zinthuzi nkumakanika kudzuka ndi kuyenda. Zikatero kumakhala kosavuta kuti nkhusayo igwidwe ndi chirombo. Pofuna kuthandiza, m'busa amadula zoyangayanga zija ndipo nkhusayo imakhala ikukana ndi kuponya matheke.

Kuuzimunso chimodzimodzi, okhulupirira amatha kulemedwa ndi “zosamalira za moyo uno” ndi “tchimolo limangotizinga.” Dulani zinthu zonsezi kuti nkhusa zikhale za changangu ndi zamphamvu ku ntchito ya Mulungu. Titha kulimbana nazo kuti zitheke komabe ndi zofunikira. Pamene nkhusa zanepa kwambiri: Nkhosa zomwe zanepa kwambiri sizingathe kudzuka zokha pamene zagwa koma kumangogubuduzika. Okhulupirira ena amafika pa mulingo wakuti anepa kwambiri muuzimu. Amangophunzira zinthu za Mulungu koma osamagawirako ena basi nkumangokula ndi kunepa okha.

Kuthupi, nkhusa zoterezi sizikhala zathanzi kwambiri kapena kubereka mofunikira. Izi ziri chomwechonso muuzimu. Abusa auzimu akuyenera kuthandiza nkhusa zonenepazi kuti zidzuke ndi kuyamba kugwira ntchito ya Mulungu.

### **M'BUSA AMATSOGOLERA NKHOSA**

Yesu anati:

**Pamene adaturutsa zonse za iye yekha, azitsogolera; ndi nkhusa zimtsata iye; cifukwa zidziwa mau ace. (Yohane 10:4)**

Mau oti utsogoleri amatanthauza kutsogolera: Mukuyenera kukhala patsogolo pa nkhusa ndi kuzitsogolera. Osati kumangoziua kopita ayi, mumazionetsa pokhala patsogolo kuti muzitsogolere kopita. Kutsogolera uku kumachitika pamene mukuchita zomwe mumaphunzitsa pokhala ndi makhalidwe okoma oti iwowo aziona. M'busa amakhala chitsanzo cha mtsogoleri, osati “mbuye” wongofuna kudzionetsera kuti ndi mtsogoleri. Petro anati atumikira.

**osati monga ocita ufumu pa iwo a udindo wanu, koma okhala zitsanzo za gululo. (1 Petro 5:3)**

### **M'BUSA AMATUMIKIRA MOSAKAKAMIZIKA**

Petro anati:

**osati monga ocita ufumu pa iwo a udindo wanu, koma okhala zitsanzo za gululo. (1 Petro 5:3)**

Musatsogolere chifukwa chakuti mwauzidwa, kukakamizidwa kapena poti mumayenera mutero ayi. Mukuyenera kutsogolera chifukwa chakuti mukufuna mutatsogolera. Kwaniritsani maitanidwe anu mosakakamizidwa.

### **M'BUSA AMAPEREKA MOYO WAKE CHIFUKWA CHA NKHOSA**

Yesu anati:

**Ine ndine Mbusa Wabwino; mbusa wabwino ataya moyo wace cifukwa ca nkhusa. (Yohane 10:11).**

Yesu anali nsembe yokhayo yoyenera kumachimo a mtundu wa anthu. Simungafere nkhusa zanu mu njira imeneyi. Anthu ambiri sangalole kufera anzawo kapena chifukwa cha chikhulupiriro chawo.

Komabe pali zinthu zina zimene mtsogoleri amayenera kutaya mu njira inayake. Mukuyenera kulolela kutaya zokhumba kapena maloto anu chifukwa cha anthu ena. Kutumikira ndi kusamalira anthu kumabweretsa zovuta zambiri. Kumatenga nthawi yambiri ndipo mutha kumakanika kuchita zinthu zomwe mumalalaka mutachita.

Yesu anaonetsera mfundo imeneyi mu fanizo la nkhusa yotayika pa Luka 15. Nkhusa zonse zinali zomvera komanso pamalo ake oyenera kupatula imodzi yomwe inatayika. Sichinali chinthu chapafupi kupita kukayang'ana mkati mwa mdima. Zinali zinthu zovuta komanso zoopsa. Koma m'busayo analolela kutaya moyo wake kuti akapululumutse nkhusayo.

### **M'BUSA AMATETEZA NKHOSA**

**Siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga, Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wocuruka. (Yohane 10:10)**

**Wolipidwa amene sakhala mbusa, amene nkhusa siziri zace za yekha, aona mmbulu ulinkudza, nasiya nkhusazo, nathawa; ndipo mmbulu uzikwatula, nuzibalalitsa; cifukwa ali wolipidwa, ndipo sasamala nkhusa. (Yohane 10:12-13)**

M'busa wabwino amakhala ndi nkhusa naziteteza, posawerengera dipo lomwe akuyenera kupereka.

Aganyu ndi atsogoleri amene amagwiritsa ntchito udindo wawo wa utsogoleri kuti apeze chuma, mphamvu, kapena ulemu. Akutumikira kuti iwo eni akapindule. Chidwi chawo sichikhala pa nkhusa ndipo amathawa mdani akafika (1 Petro 5:2).

## **MACHENJEZO KWA ATSOGOLERI**

Werengani Ezekiel 34. Chaputala chimenechi chiri ndi machenjezo ochuluka kwa abusa oyipa omwe analamulira Israel. Koma machenjezo amenewa akupitanso kwa atsogoleri onse omwe ndi abusa oyipa. Mulungu akulengeza matsoka ndi maweruzo pa abusa omwe:

1. Sadyetsa nkhusa: vesi 2
2. Amabera nkhusa: vesi 3
3. Amadzisamalira okha osati nkhusa: vesi 2-3, 8
4. Salabadira zosowa za nkhusa: 4  
(satonthoza ovulala, kulimbikitsa nkhusa zofowoka, kapena kusamalira nkhusa zodwala muuzimu)
5. Safunafuna nkhusa zotayika: vesi 4 ndi 6
6. Amalamulira mwa nkhusa ndi mwamphamvu: vesi 4
7. Amabalalitsa nkhusa: vesi 5-6
8. Amalola mdani aononge nkhusa: vesi 8
9. Amalola matenda a uchimo ndi magawano kuti aononge nkhusa: vesi 21

## **LONJEZANO KWA ABUSA**

Ngati mukutsatira mfundo za Baibulo za kutsogolera ngati m'busa, mutha kuima pa lonjezano ili:

**Ndipo pakuonekera Mbusa wamkulu, mudzalandira korona wa ulemerero, wosafota. Momwemonso, anyamata inu, mverani akulu. (1 Petro 5:4).**

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osonera

---

---

---

2. Kodi M'busa Wabwino ndi ndani?

---

3. Kodi gulu limodzi loona la nkhusa ndi chiyani?

---

4. Lembani mwachidule mfundo za ubusa zomwe mwaphunzira m'phunziro lino. Kodi ntchito za m'busa nzotani?

---

---

---

---

5. Lembani mwachidule machenjezo omwe aperekedwa kwa abusa oyipa pa Ezekiel 34.

---

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwa bukhu lino)

## KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

1. Fufuzani moyo wanu molingana ndi mfundo za utsogoleri waubusa zomwe mwaphunzira m'phunziro lino. Kodi inu mfundo zimenezi mumazigwiritsa ntchito pa moyo ndi utumiki wanu? Kodi mukulephera pati? Kodi mungachite bwino bwanji?
2. Werengani Masalimo 23 pogwiritsa ntchito mlozo uwu: Ngati m'busa Wambuye ndiye:
  - Wopereka wanu: vesi 1
  - Mtendere wanu: vesi 2
  - Wokonza njira wanu: vesi 3
  - Chitetezo chanu: vesi 4
  - Wokonzekeretsa wanu: vesi 5
  - Wochuruka wanu: vesi 5
  - Lonjezano lanu: vesi 6

Zoonjezera zina pa Masalimo 23: Pokamba za ukoma ndi zifundo mu vesi 6, onani:

- Kufupikira kwake: “Zidzanditsata ine.”
- Kupitirizika kwake: “Zikhalapobe moyo wathu wonse”
- Kukhazikika kwake: “Masiku onse”
- Kutsimikizika kwake: “Indedi”

Lingalirani funso ili: Kodi ukoma ndi zifundo zimakutsatani? Kodi mukamakhala m'moyo uno mumasiya m'mbuyo chilimbikitso, mphamvu, ukoma ndi zifundo?

Polankhula za chigwa chomwe chikuyimira nyengo zamavuto m'moyo wathu wa Chikhristu, onani:

- Chithunzithunzi si chinthu chenichenicho. Chimayimilira china chake. Chimodzimodzinso chigwa. Chigwa ndi chithunzithunzi cha nkondo ya mdani yomwe imachitika muuzimu.
- Ndi ulendo chabe. Simukhala m'chigwa mpaka kalekale. Sakunena kuti “ndidzafera momwemo” kapena “kukhala momwemo.”
- Ndi kuyenda, osati “kuthawa” mwa mantha ayi.
- M'zigwa mumakhala zomera zochita bwino kwambiri. Funso lalikuru si lakuti kodi mudutsa m'chigwa ayi popeza mufune musafune mukumana ndi zigwa zochuruka pa moyo wanu. Funso lalikuru ndi lakuti, “kodi mudzachita chiyani mukamadzadutsa

m'chigwa.” Kodi mudzadya zabwino za Mulungu zomwe zimapezeka m'zigwa mokhamokha?

- Ndodo (chidzudzulo) ndi chibonga (chisamaliro) za m'busa zimakhala mbali imodzi ya moyo wa m'chigwa.
- Phunzirani zambiri za zomwe Baibulo likulankhula zokhuza ubusa powerenga ndime izi:
- Numeri 27:17
- Masalimo 23; 80:1
- Yesaya 40:11
- Ezekiel 34; 37:24
- Zekariya 10:2; 11:15-17
- Mateyu 9:36; 25:32; 26:31
- Marko 6:34; 14:27
- Yohane 10
- Ahebri 13:20
- 1 Petro 2:25; 5:4

## CHAPUTALA 7 NTCHITO ZA ATSOGOLERI

### ZOLINGA

Mukamaliza chaputala chino mudzakwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kudziwa ntchito zofunikira kwambiri za atsogoleri
- Kutanthauzira “kukonzekeretsa”
- Kulemba mwachidule zotsatira za “kukonzekeretsa” anthu ku ntchito ya utumiki.
- Kudziwa ntchito zeni zeni za atsogoleri.

### VESI LOTSOGOLERA

**Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; kuti akonzere oyera mtima: ku nchito ya utumiki, kumangirira thupi la Kristu; (Aefeso 4:11-12)**

### MAU OYAMBA

M'mbuyomu mwaphunzira za MOMWE mungasogolere ngati mtumiki, kapolo komanso m'busa. Phunziro lino ndi maphunziro ena otsatirawa, muphunzira za ZOMWE mtsogoleri amachita.

Utsogoleri umakhala ndi zochitika zambiri. Ntchito ndi udindo kapena chochitika. Ndi zosatheka kukambirana ntchito ina iri yonse yomwe mtsogoleri anaitanidwira kukachita koma tiona ntchito zochepe chabe.

### CHOFUNIKA CHOYAMBILIRA

Chofunika choyambilira cha mtsogoleri chafotokozeredwa mu ndime iyi:

**Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; kuti akonzere oyera mtima: ku nchito ya utumiki, kumangirira thupi la Kristu; (Aefeso 4:11-12)**

Mulungu anaika atsogoleri kuti akakonzekeretse okhulupirira ku ntchito ya utumiki. Mau oti “kukonzekeretsa” amanthauza kuphunzitsa ndipo “ntchito ya utumiki” ndi udindo, kapena ntchito ina iriyonse imene ingachitike mu utumiki.

Ntchito yaikulu ya atsogoleri ndi kukonzekeretsa okhulupirira ku ntchito ya utumiki. Popeza kuti wokhulupirira wina aliyense wapatsidwa mphatso yauzimu, atsogoleri ali kuthekera kochita chiri

chonse mu utumiki pogwiritsa ntchito mphatso zimenezi. Chotero wokhulupirirawa akuyenera kukonzekeretsedwa kuti akamtumikire bwino Mulungu.

Kukonzekeretsa kumaphatikizapo kuphunzitsa, kulalikira, kusula, ndi kuonetsera.

Kumaphatikizaponso kusonkhanitsa okhulupirira pamodzi kukachita ntchito ya utumiki. Izi zikutanthauza kuti atatha kusulidwa, aikidwe malo osiyanasiyana molingana ndi mphatso zawo kuti atumikire.

Kukonzekeretsa kumatanthauzanso kuti kuphunzitsa anthu ena kuti akhale atsogoleri ndipo ena otsatira. Magulu onse awiri ndi ofunikira mu utumiki. Chaputala 10 cha bukhu lino chikufotokozera bwino za kuphunzitsa atsogoleri ndi otsatira.

Ngati ndinu mtsogoleri yemwe waitanidwa ndi kusankhidwa ndi Mulungu mukuyenera kuyamba kusula ena kukachita ntchito ya Mulungu. Iyi ndiye ntchito yanu yoyambilira ngati mtsogoleri.

Zomwe zimachitika okhulupirira akakonzekeretsedwa ku ntchito ya utumiki ndi izi:

- Ntchito ya utumiki imachitika: Aefeso 4:12
- Thupi la Khristu (mpingo) limalimbikitsidwa (kumangalirika) Aefeso 4:12
- Anthu amakula muuzimu: Aefeso 4:13-15
- Umodzi umakhalapo: Aefeso 4:13
- Anthu amaumbika mchikhalidwe cha Khristu: Aefeso 4:13
- Anthu amazama ndi kukhazikika m'choonadi: Aefeso 4:15-16
- Thupi la Khristu limagwira bwino ntchito: Aefeso 4:16

## **MAUDINDO A MU NDONDOMEKO YA KUKONZEKERETSA**

Mu kukonzekeretsa okhulupiriraku muli maudindo ambiri ndipo ena mwa iwo ndi awa:

### **KUKHALA CHITSANZO**

Taona kale za udindo wa mtsogoleri pa kukhala chitsanzo kwa otsatira ake. Ngati chitsanzo, atsogoleri akuyenera akhale oti ayitanidwa, adzodzedwa, adindo ndi abusa okhulupirika, komanso otumikira onse. Moyo wake ukuyenera kuonetsera makhalidwe oyenera atsogoleri omwe taphunzira mu Chaputala 4. Akuyenera kukhala munthu wa pemphero komanso wokonda kusanthula Mau. Chitsanzo chanu chikuyenera kukhala chaumulungu chifukwa:

**Wophunzira saposaphunzitsi wace; koma yense, m'mene atakonzedwa mtima, adzafanana ndi mphunzitsi wace. (Luka 6:40)**



Kuthekera kolamulira ndi kutsogolera ena kumayenera kuyamba ndi kudzilamulira wekha munthu. Mukuyenera kukhala chitsanzo mu makhalidwe anu, mkayendedwe kanu ndi Ambuye, kuchitira umboni ndi mu ntchito iriyonse ya utumiki.

### **KUSAMALIRA**

Udindo wina pa kukonzekeretsa okhulupirira ku ntchito ya utumiki ndi kusamalira otsatira.

Udindo uwu tinautsindika pamene timaphunzira za kutsogolera ngati kapolo komanso ngati m'busa. Anthu ndi ofunika kwambiri kuposa mapologalamu ndi zochitikachitika.

Ngati mtsogoleri mwaitanidwa kuti mukasamalire anthu omwe Mulungu wakupatsani kuti mukawatumikire. Mukuyenera kuwakonda, kukhala wokhudzika ndi mavuto awo, kutumikira moyo wawo wauzimu, kuthupi komanso zosowa zawo zina ndi zina molingana ndi momwe Mulungu wakupatsirani kuthekera. Mbali imodzi ya kusamalira ndi pamene m'busa akutenga nthawi yopempherera omutsatira ake. Musachimwe polephera kupempherera anthu omwe Mulungu wakupatsani kuti mukawatumikire.

### **KUTSOGOLERA**

Mtsogoleri akuyenera kumatsogolera. Amapereka upangiri kwa anthu kuti akakwaniritse chomwe Mulungu waitanira kukachita. Atsogolereni anthu ku chimene Mulungu akufuna kuti apite, osati komwe iwo amafuna okha atapita. Izi zikuphatikizapo kuwapatsa uphungu woyenera kuti akayende m'njira za Mulungu kudzera m'Mau ake.

### **KUPANGA CHIGANIZO**

Kutsogolera anthu kumasoweka kuti munthu azipanga ziganizo. Pa mfundo zokhazikika pa kupanga chiganizo zomwe zingakuthandizeni kuchita chinthu ichi. Muphunzira izi mu Chaputala 8.

### **KUTHANA NDI MIKANGANO**

Paliponse pamene pali anthu, mikangano siimatha. Mtsogoleri akuyenera kukwanitsa kumathana ndi mikangano yoteroyo motsogozedwa ndi Ambuye. Padzakhala anthu ena omwe adzafunika kuwapatsa chilango chifukwa chakugwa mu uchimo kapena kuchoka pa choonadi kuti akonzeke. Chaputala 9 chikufotokozerabwino za momwe mungachitire ntchito imeneyi.

### **KUUNIKA MOSAMALITSA ZOMWE ZIKUCHITIKA PA MALOPO.**

Kuti muchite bwino pa ntchito ya utumiki mukuyenera kudziwa bwino anthu omwe mukuwatumikira. Kudziwa mavuto awo, zosowa zawo komanso zinthu zomwe zimakhuzamiyoyo yawo. Kuti muthe kuchita izi mukuyenera kuchita kauniuni wa zomwe zikuchitika

m'miyoyo yawo. Kuunika uzimu wao, zochitika mthupi mwao, katundu yemwe amagwiritsa ntchito komanso zochitika m'chikhalidwe chawo. A Harvestime International Institute ali ndi phunziro lotchedwa “Kauniuni wa Zochitika Pakati pa Anthu” ndipo akufotokozera bwino mfundo zochitira kauniuni ndi zolinga za utumiki.

## **KUDZIWA CHOLINGA**

Tikati cholinga tikunena za masomphenya auzimu. Baibulo limati:

**Popanda cibvumbulutso anthu amasauka; Koma wosunga cilamulo adalitsika.**

**(Miyambo 29:18)**

Mu cholinga kapena masomphenya auzimu muli zinthu ziwiri zofunika kuzimvetsa:

1. Zolinga za Mulungu
2. Mbali yanu pokwaniritsa zolinga ndi madongosolo a Mulungu.

Mukadziwa cholinga chanu mu utumiki, mumadziwa mosavuta mbali imene Mulungu wakuyika mu dongosolo lake. Cholinga chimakhazikitsa masomphenya a utumiki. Mumadziwa bwino chomwe mukuyenera kuchita kuti mukakwaniritse masomphenya a Mulungu pa moyo wanu. Mumakonzana ndi kukwaniritsa madongosolo oyenera kukafikira chomwe Mulungu waikiza pa mtima panu. Mukadziwa cholinga cha Mulungu komanso mbali imene Iye wakuikani mumakwaniritsa mosavuta maitanidwe anu a utsogoleri.

Phunziro lotchedwa “Kuyang’anira mwa Zolinga” lidzakuthandizani kupeza cholinga chanu mu dongosolo la Mulungu.

## **KUKONZEKERA ZINTHU**

Kudziwa cholinga chanu mu utumiki ndi kosiyana ndi kukwaniritsa cholinga chanu. Mukuyenera kukonzana ndi kukwaniritsa madongosolo okuthandizani kutero. Mukuyenera kuphatikizapo ntchito pa chidziwitso ndi chikhulupiriro chanu kuti mukachite ntchito ya utumiki. Kukonzana madongosolo motsogodzedwa ndi Mzimu wa Mulungu kumathandiza kuti mukagwire ntchito mogwirizana ndi Mulungu pamene mukukwaniritsa zolinga zake.

Mukuyenera kukhala ndi dongosolo lokhazikika kuti mukakwaniritse zolinga zanu mu utumiki. Ngati ndinu mtsogoleri thandizani okutsatirani kuti apange madongosolo othandizira gulu lanu pamodzi kuchita ntchito ya utumiki. Kukonzana dongosolo kumaphatikizapo kuona:

- Zomwe muchite
- Momwe muchitire (ndondomeko ya kachitidwe kanu)

- Nthawi yomwe muchitire zimenezo
- Anthu omwe achite
- Zomwe zikufunika
- Ndondomeko ya kuunikira zomwe muchite kuti muone ngati zikukwaniritsa zolinga za dongosolo lanu.

Kukonza dongosolo ndi ntchito yaikulu kwambiri zedi kwa mtsogoleri. Ndi mfundo ya Baibulo ndipo yafotokozeredwa bwino mu phunziro lotchedwa, “Kuyang’anira mwa Zolinga” la Harvestime International Institute.

### **KUKWANIRITSA DONGOSOLO**

Mtsogoleri akatha kupanga dongosolo, akuyenera kuyambapo kukwaniritsa dongosololo. Kuti mukachite zomwe ziri mu dongosolo lanu, mukuyenera kuchita zinthu zomwe ziri m’musizi. Mfundo iriyonse ya izi yafotokozeredwa bwino mu phunziro la “Kuyang’anira mwa Zolinga.”:

- Kusankha anthu oti akwaniritse madongosolo
- Kuwafotokozerera momveka bwino za dongosolo ndi ntchito ya utumiki yomwe ikufunika kuchitika.
- Kuwapatsa udindo ndi ulamuliro wa kukwaniritsa dongosolo.
- Kuphunzitsa omwe asankhidwa kuti akhale ndi luso loyenera pa ntchitoyo.
- Kuika anthu m’ malo moyenera molingana ndi tsatanetsatane wa dongosolo la ntchito
- Kuika masiku oyambira ndi kumalizira ntchito zosiyanasiyana komanso kuona ngati zinthu zikuyenda bwino
- Kupanga dongosolo la chuma chomwe chifunike pa ntchito yonseyo.
- Kupanga ziganizo
- Kuunika kuti muone ngati zinthu zikuyenda bwino.
- Kauniuni wa ntchito ya utumiki. Kuunikira kumathandiza kuti mukadziwe ngati zomwe mwachita zikugwirizana ndi dongosolo lanu komanso dongosolo la Mulungu mu utumiki wanu.

### **KULANDIRA MPHAMVU PA NTCHITO YANU**

Monga tanena kale ndi kovuta kukambirana za ntchito zonse zimene mtsogoleri akuyenera kuchita, koma zimene zachulidwazo ndiye zofunikira kwambiri pa udindo wa utsogoleri.

Lonjezano Imwe mugwiritse ntchito pamene mukuchita ntchito yomwe Mulungu wakuitanirani pa utsogoleri ndi ili:

**kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa cikhulupiriro, ndi wa cizindikiritso ca Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro, ku muyeso wa msinkhu wa cidzaloca Kristu. (Afilipi 4:13)**

Pamene mwapanikizika ndipo mukudzifunsa nokha zomwe mungachite kuti mukakwaniritse maitanidwe, thamangirani pa Ambuye ndi kukhala pamaso pake panokha. Simuthedwa nzeru kapena kukhumudwitsidwa pamene mudikira pa Ambuye m'pemphero:

**Inu mudzasunga mtima wokhazikika mu mtendere weni weni, cifukwa ukukhulupirirani Inu. (Yesaya 26:3)**

Pempherani pemphero lomwe Mfumu Solomo anapemphera ngati mtsogoleri:

**Ndipo kapolo wanu ndiri pakati pa anthu anu amene Inu munawasankha, anthu ambirimbiri osawerengeka, kapena kulembeka m'unyinji wao. Patsani tsono kapolo wanu mtima womvera wakuweruza anthu anu; kuti ndizindikire pakati pa zabwino ndi zoipa; pakuti akutha ndani kuweruza anthu anu ambiri amene? (1 Mafumu 3:8-9)**

## MAFUNSO ODZIFUNSA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osonera

---

---

---

2. Kodi ntchito yaikulu ya atsogoleri ndi yotani?

---

---

---

3. Tanthauzirani “kukonzekeretsa.”

---

---

4. Kodi zotsatira zabwino za kukonzekeretsa okhulupirira ndi zotani?

---

---

---

---

5. Lembani mwachidule maudindo a atsogoleri omwe akukonzekeretsa okhulupirira ku ntchito ya utumiki.

---

---

---

---

---

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwa bukhu lino)

## **KUPITIRIZA KUPHUNZIRA**

1. Mkatikati mwa phunziro lino takhala tikukamba za maphunziro awiri a Harvestime International Institute otchedwa, “Kauniuni wa Pakati pa Anthu” ndi “Kuyang’anira mwa Zolinga.” Monga tanenera kale m’phunziro lino tikuganiza kuti mutaphunzira nawo maphunzirowa kuti mudziwe zambiri za ntchito yoyang’anira molingana ndi Mau a Mulungu.
2. Zitsanzo zina zofotokozerana ntchito za atsogoleri nazi:

## **KUMANGA MALINGA A YERUSALEMU**

### **VUTO:**

Nehemiya analandira lipoti lakuti otsala a m’Yuda omwe anabwelera kuchokera ku ukapolo anali kukulukutika ndipo malinga a Yerusalemu anali bwinja naotchedwa ndi moto: Nehemiya 1:2-3.

### **YANKHO:**

Nehemiya anasala kudya napemphera: Nehemiya 1:4-11

Anabvumbulutsa mkwiyo wake a mfumu: Nehemiya 2:1-2

Anauza amfumu chifukwa chomwe anali wachisoni: Nehemiya 2:3

Amfumu anafunsa, “Vuto lako ndi chiyani? Nehemiya 2:4

Nehemiya anapempha chitsogozo kwa Mulungu asanayankhe: Nehemiya 2:4

Anapempha amfumu kuti amlole apite ku Yuda kukamanga malinga: Nehemiya 2:5

Amfumu anabvomera pempho lake: Nehemiya 2:6

Nehemiya anapempha amfumu kuti ampatse makalata akuti agwiritse ntchito ndi kukatenga matabwa m’nkhalango: Nehemiya 2:7-8

Nehemiya atafika anakhala miyezi itatu akuyendera mzindawo kuti aone bvuto lenileni ndi kukonza dongosolo la kagwiridwe ka ntchito: Nehemiya 2:12-16

Nehemiya auza anthu ena za chilinganizo chake kuti amuthandize kumanga linga: Nehemiya 2:17-3:32

Pamene adani a Israel amafuna kuimitsa ntchitoyo, anthu anapemphera nakhala tcheru: Nehemiya 4:1-13

Pamene anthu anachita mantha, Nehemiya anawalimbikitsa: Nehemiya 4:14

Atangowauza adani awo kuti anali wokonzeka kudziteteza okha, anabwerera nakagwira ntchito yomanga: Nehemiya 4:15

Nehemiya anapeza njira ina yogwirira ntchito nakhalanso tcheru nthawi yomweyo: Nehemiya 4:16-23

### **ZOTSATIRA**

Anamaliza kumanga m’masiku 52: Nehemiya 6:15

Anthu analemekeza Mulungu: Nehemiya 12:27-29, 31-42

Anthu anadziyeretsa okha nayeretsanso mzinda: Nehemiya 12:30

Anapereka nsembe kwa Mulungu: Nehemiya 12:43

Pamene adani a Israel anaona za chipambana namva za chikondwerero, anasungunuka mitima: Nehemiya 6:16

### **KUCHOKA PA CHOONADI**

#### **VUTO:**

Amuna ena amaphunzitsa chiphunzitso chonama ku Antiokeya: Machitidwe 15:1

Paulo ndi Banaba sanathe kuthana ndi vutolo: Machitidwe 15:2

#### **YANKHO**

Mpingo wa ku Antiokeya unaganiza zopempha upangiri kuchokera kwa atumwi ndi akulu ampingo ku Yerusalemu; Machitidwe 15:2-3.

Nthumwi za ku Antiokeya zinafotokozera momwe Amitundu amatembenukira mtima kudzera m'chikhulupiriro basi: Machitidwe 15:4.

Atumwi ndi akulu ampingo anakumana m'chipinda chomata kuti akambirane za nkhanayi: Machitidwe 15:6.

Petro anakumbutsa anthu za chimene Mulungu anachita kwa Koneliyo ndi a panyumba pake: Machitidwe 15:7-11.

Paulo ndi Banaba anapereka umboni wa momwe anawagwiritsira ntchito pakati pa Amitundu. Machitidwe 15:12

Yakobo anakumbukira za momwe aneneri a m'Chipangano Chatsopano ananenera za kutembenuka mtima kwa Amitundu. Machitidwe 15: 13-18.

Yakobo anapereka yankho la vutolo. Machitidwe 15:19-21.

Atumwi, akuluakulu, pamodzi ndi mpingo wonse unagwirizana ndi ganizolo. Machitidwe 15:22

Kalata inalembedwa. Machitidwe 15:22-30

Yuda ndi Sila anasankhidwa kuti akapereke kalata. Machitidwe 15:22

Yuda ndi Sila anakapereka kalata komanso uthenga wa pakamwa womwe anapatsidwa. Machitidwe 15:30, 32.

#### **ZOTSATIRA:**

Mpingo unakondwera. Machitidwe 15:31

Yuda ndi Sila anabwerera ku Yerusalemu mwa mtendere. Machitidwe 15:33

Ntchito ya Mulungu inapirira popanda vuto. Machitidwe 15:35.

Malangizo omwe anali m'kalatamo anaperekedwa ku mipingo ina yatsopano ndi Paulo, Sila komanso Timoteyo.

### **KUWERUZA ANTHU**

#### **VUTO**

Anthu amayima pa mzere kuyambira m'mawa mpakana madzulo kudikirira Mose kuti aweruze milandu yawo. Eksodo 18:13

Mose amayesera kuthana ndi milandu yonse yekha. Eksodo 18:14-16

Zinthu izi zinabweretsa mabvuto ambiri kwa Mose komanso anthu onse. Eksodo 18:18

#### **YANKHO**

Yetero anamuza Mose kuti aziweruza milandu yofunikira yokha yokha. Eksodo 18:19

Anakonza dongosolo lopeza anthu omuthandiza ntchito. 18:19-22

Mose anauza anthu za vutolo. Deuteronomu 1:9-12

Mose anauza mtundu uliwonse usankhe anthu anzeru ndipo anawaika kukhala atsogoleri. Deuteronomu 1:13

Mose anawaphunzitsa atsogoleri za kagwiridwe kawo ka ntchito. Deuteronomu 1:16-18

#### **ZOTSATIRA**

Mose anathandizidwa pa utsogoleri wake. Eksodo 18:22

Mose anali nako kuthekera kogwira bwino ntchito ya utsogoleri. Eksodo 18:23

### **AZIMAYI AMASIYE OSALABADIRIDWA**

#### **VUTO**

Ophunzira amachurukirachurukira ndipo zinabweretsa chisokonezo m'kakhalidwe kawo ka tsiku ndi tsiku. Azimayi ena amasiye anayamba kudandaula popeza anaona kuti sakulabadiridwa. Machitidwe 6:1

Atumwi anayamba kutanganidwa ndi vuto la chisamaliro cha anthu kumbali ya chakudya zomwe zinayamba kubwezeretsa m'mbuyo ntchito yolalikira Mau a Mulungu. Machitidwe 6:2



Anthu anakumbutsidwa za udindo waukuru wa atumwi khumi ndi awiriwo, womwe ndi pemphero ndi kulalikira Mau. Machitidwe 6:3-4

Anthu anauzidwa kuti asankhe amuna asanu ndi awiri kuti athane ndi vutoli. Machitidwe 6:3

Anthu anasankha amuna asanu ndi awiri. Machitidwe 6:5

Atumwi anabvomereza chisankho cha anthu kudzera m'pemphero ndi kuyala manja pa iwo. Machitidwe 6:6

### **ZOTSATIRA**

Anakwanitsa kumaona zosowa za wina aliyense ndipo umodzi unabwezeretsedwanso. Atumwi tsopano anayamba kukwanitsa kumagwira ntchito zawo momasuka. Machitidwe 6:7

## **CHAPUTALA 8**

### **KUPANGA ZISANKHO**

#### **ZOLINGA:**

Mukamaliza chaputalachi muzikwanitsa kuchita izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kufotokoza kagwiritseidwe ntchito ka Baibulo popanga zisankho
- Kulemba mwachidule ndondomeko zopangila zisankho
- Kufotokoza cholinga cha chitsanzo
- Kufotokoza ubwino wa chitsanzo popanga zisankho
- Kugwiritsa ntchito chitsazo cha Baibulo popanga zisankho

#### **VESI LOTSOGOLERA**

**Kufatsa mtima ndi osauka Kuposa kugawana zofunkha ndi onyada. (Miyambo 16:9)**

#### **MAU OYAMBA**

Tsiku lililose azitsogoleri amavutika kupanga zisankho. Chisankho china chilichose ndi chofunika chifukwa zimakhala ndi zotsatira pa moyo wa mtsogoleri komanso utumiki. Muyenera kupeza mayankho pa zovuta zokhudzana ndi moyo wanu wa tsiku ndi tsiku komaso kuganiza kuti mupanga chani. Zisankho zimasonyeza tsogolo lamunthu. Zisankho za mtsogoleri zimasonyeza tsogolo osati la mtsogoleri yekha komaso anthu amene akuwatsogolera. Moyo wa munth ndi zotsatira za zisankho ndi ziganizo zimene amapanga. Pangani zisankho zoyenera. Kukana kupanga zisankha ndi kupangaso zisankho. Phunziro iri lipereka ndondomeko zopangira zisankho zabwino mogwirizana ndi Bibulo.

#### **KUPANGA ZISANKHO POGWIRITSA NTCHITO BAIBULO**

Kupanga zisankho pogwiritsa ntchito Baibulo sipogwiritsa ntchito mawula, kapena mpavu kuwanthu. Mavuto a njira iyi anafotokozedwa mu nkhani ya ana a Israeli ku Kannani (Numeli 13). Njira yova maganizo ambiri imabweretsa zisankho zolakwika, zokondwera komaso mpikisano. Mawula amabweretsa kuptwetekedwa ntima, nkwiyo komaso magawano. Izi si njira zopangira zisankho zofana ndi Baibulo. Izi ndi njira zimene mpingo unatengera kuchokera ku dziko.

Machitidwe 15 ndi chitsazo chabwino cha m'mene tingapangile zisankho pogwiritsa ntchito Baibulo. Chitsazo ichi chikugwirizana ndi chikhalidwe cha chiyuda. Pothana ndi vutoli azitsogoleri anakumana ndi kupemphera, anawonetsetsa fundo, andipo anapeza yankho motsogozedwa ndi mzimu woyera. Mulungu amayika atsogoleri.

Mulungu amayika atsogoleri kuti azipanga zisankho, Ndipo amawapatsanzeru kuti akwaniritse ntchito imene apatsiddwa. Azitsogoleri akafuna kuti apange zisankho zofunika kwambiri ayenera kukumana, kukambirana ndi kuwunikaso bwinobwino ndi kugwirizana fundo yoofumika mmogwirizana ndi mzimu woyera.

### **NDONDOMEKO YAKAPANGIDWE KA ZISANKHO**

Pali ndondomeko zothandiza popanga zisankho.

- Pezani vuto

Vuto ndi chani kapena fuso lake ndi liti limene lifunika yankho? Pezani uthenga ose ofunika okhudzana ndi nkhani yofufuzidwa, Lembani vuto mwachidule, simungapange chisankho chabwino pokhapokhapo mutapeza vuto.

- **TSATILANI NDONDOMEKO YOPANGILA ZISANKHO**

Fanizo ndi chitsazo chitsazo cha zinthu zina. Chimapereka chitsazo cha m'mene munga tsatilire zinthu zina. Fanizo la kapangidwe ka zisankho limapereka chitsazo cha m'mene mungapangilire zisankho. Tsamba lotsatilaro pali fanizo la Baibulo lofotokoza m'mene mungapangire zosakho mogwirizana ndi cholinga cha Mulungu. Onani fanizoli ndipo werengani mfundo zotsatira zimene zinafotokozeredwa;

### **CHITSANZO CHA M'BAIBULO CHA KAPANGIDWE KA ZISANKHO**

Pezani vuto, funso kapena zochitika m'moyo zimene zifunika chitsogozo

Kodi malemba ananena mwachindunji, molamula, kapena ngati fundo yoti aliyese atengepo

mbali.

INDE	AYI	
GAWO 1	GAWO 2	GAWO 3

<p>Pangani chisankho ngati chikugwirizana ndi lamulo la Baibulo, fundo za m'baibulo, kapena chitsazo.</p>	<p>M'chitidwe opereka mafuso, pangani chisankho powonaso mafuso awa;          Kodi Mulungu alemekazeka?          Chokulimbikitsani ndi chani?          Kodi ndi zoyenera?          Kodi chilimbikitsa kukula moyo wawuzimu?          Kodi ndi khalidwe lopereka ukapolo?          Kodi ndizosephana ndi mawu</p>	<p>Kodi ndi zokhudzana ndi zochitika m'moyo; pitililani ndi ndondomeko izi;          Werengani malemba;          Vetserani kwa mzimu ngati akutsogolerani pa zoti muchite.          Funani upangiri wa chikhristu.          Unikani zimene zakuchitikirani.</p>
	<p>a Mulungu?          Kodi zithela ku mayesero?          Kodi zipereka mawonekedwe a choyipa?          Kodi ziwononga chikumbuntima chako          Kodi ena ziwakhudza bwanji?          Pepherani ndipo pangani chiganizo.          Onani ngati muli ndi ntendere.          Ngati mulube ntendere pitilizani ku funa ambuye potsatila fanizoli.</p>	<p>Gwiritsani ntchito mawu a Mulungu pa chitsogozo Pangani chisankho.          Onani ngati muli ndi ntendere</p>

### **KUGWIRITSA NTCHITO FANIZO**

Ndondomeko yoyamba pogwiritsa ntchito fanizo la Baibulo ndi kupeza vuto, funso kapena zochitika m'moyo zimene chikufunika chitsogozo. Kenako, fufuzani malemba kuti muwone ngati malamulo ananena mwachindunji, chitsanzo kapena mokhudzana ndi nyengo yanu.

Chitsogozo pa nkhani yokhudza ndi zinthu zambiri makamaka zokhudzana ndi zabwino kapena ndi zoyipa zinanenedwa moveka bwino m'mawu a Mulungu.

### **INDE**

Ngati yakho liri inde ndekuti vuto linayakhidwa moveka bwino m'malemba ndipo pangani chisakho pogwiritsa ntchito mavumbulutso amenewa. (Onani Column 1 On Model). Onetsetsani kuti chiganizo chani chikugwirizana ndi malemba a Mulungu.

### **AYI**

Ngati yankho liri Iyayi, pitirizani ndi ndondomeko za mgulu la no, pali zisankho ziwiri za mgulu limeneri la zinthu zimene zizinanenedwe mwa chindunji mu Baibulo. Mukuyenera kuwonetsetsa ngati chisankho chopangidwa chikukhudza chikhalidwe chopereka mafuso kapena zochitika pa miyoyo ya anthu.

#### **Machitidwe Opereka Mafunso**

Nchitidwe opereka mafuso ndi umene mawu a Mulungu sananene mwa chindunji ngati uli ololodwa kapena ayi. Zimatha kukhalazidsankho zokhudzana ndi zisangalao kapena zochitika za chikondwerelo, khalidwe, zakudga kapena zakumwa kapena mavalidwe.

Ngati chisankho chikukhudza zinthu zopereka mafuso dzufuseni nokha mafuso amene aperekedwa mu gawo la chiwiri la fanizo la mapangidwe a zisankho. Mukayankha mafuso amenewa pehereani, ndipo pangani chisankho potengela mayankho amene mwawapeza pa fanizolo.

#### **Zochitika M'moyo**

Zochitika m'moyo ndi chisankho chimene chimakhala ndi zotsatila zimene zimakhala ndi mphavu pa tsogolo lamunthu. Zina mwa zisankho zimenezi ndi zokhudzana ndi; ukwati, utumiki, ntchito, malo okhala, mpingo ndi zina zambiri. Pa zisakho izi gwiritsani ntchito mafuso a mu gawo lachitatu. POyamba peherani zokhudzani chisankho. Mufuseni ambuye kuti cholinga chke chidanilitsidwe m'moyo wani. Pephani zero kuti mupange chisankho chabwino ndipo pemphani anthu ena kuti akuthandizeni kupephera. Werengani mawu ndipo khazikitsani malonjezano olembedwa mu mawu a Mulungu.

Zindikirani mavumvulutso amulungu ngati akukutsogolerani. Pali njira zambiri zimene Mulungu amalankhulila ndi anthu po dziwitsa anthu kuti ziwathandize kupanga zisankho. Njira zina mwa izo ndi masophenya, uneneri, maloto, angelo, andi mawu.

Koma mavumbulutso amenewa si lamuloli munthu atha kusankha kuti agwiritse nthito kapena ayi. Ntchito imodzi ya Nzimu woyera ndi kutsogolera.

**(Yohane 16:13)**

Nthawi zambiri mzimu woyera atitsogolera munjira imeneyi. Ngati vumbulutso labwela Yamikani ambuye koma kumbukirani ichi palibe maloto, masophenya, unenelli kapena vumbulutso lina lililose lilmene limatsutsana ndi Mawu a Mulungu.

Njira ina imene imathandiza popanga zisankho ndi upangiri wa chikhristu. Upangiri wa nzeru wochokera kwa atsogolero a Chikhristu ndiwabwino.

**(Miyambo 11:14)**

**(Miyambo 12:15)**

Muyenera kuwonaso nyengo imene muli imene ikukupangani kuti mupange chisankho kenako onani njira zochokera Baibulo pa chitsogozo chani.

### **PEZANI MAYANKHO OSIYANASIYANA**

Mukatsatira chitsazo chopangira zisankho mupeza kuti pali mayankho ambiri pa yakho la vuto limene mulinalo. Onani mayankho osiyanasiyana andipo onetsetsani pogwiritsa ntchito zinthu izi;

Zowopsya Ngakhale kuti muli ndi chikhulupirilo mukuyenera kukhala ndi zeru komaso umunthu. Onani ubwino komaso kuyipa kwa zisankho zose. Open and closed doors of circumstances may affect your decision.

Zofunika: Kodi mufuna zinthu zina kuti muchite chisankho chimene mwasankha. Chisankho sichimakhala chabwino ngati palibe munthu amene akhoza kuchikwanilitsa. Palibe chisankho chimene chikhoza kukwanilitsidwa ngati simungakhulupirile Mulungu kuti apereka zofunika zake.

Zotsatira; Kodi ndi yankho liti limene libwera ndi zotsatira zochuluka pa ntchito yochepa? Palibe chifukwa chopangila zinthu movutika. Ngati pali njira yo pepuk ayochitira zinthu sankhani imeneyo pokhapokhapo ngati Mulungu akukutsongolerani choncho.

- **SANKHANI YANKHO LOPOSA ONSE**

Mutawonetsetsa mayankho onse, sankhani limene likuposa onse. Munapepha kuti Mulungu akutsogolerani ndiye khulupirilani kuti akukutsogolerani. Sankhani yakho labwino powonetsetsa zowoposa zake, zinthu zimene zifunike kuti mukwaniritse zofuna zanu, komaso zotsatira za chisankho chanu.

Tikunena kuti “thawi yina” chifukwa nthawi zina Mulungu Mulungu amatsogolera njira zosiyana ndi zimene anthu amayembekezera. Kumbukirani kuti njira za Mulungu si Njira za anthu ndipo nthawi zina mayankho ake awoneka osapatsa chikoka nkuwona kwa maso a wumunthu. Ndiye khalani odziwa za izi.

Chisankho chirichose chiri ndi kuwopsya kwake pokhapokha Mulungu atakuyankhulani pogwiritsa ntchito mavumbulutso kapena mawu ake. Musankhale amantha kupanga chisankho zisankho zambiri zoyipa zimantha kukonzedwa.

Kumbukirani kuti mzimu wa ambuye akukutsogolerani pa chisankho chanu;

**Mtima wa munthu ulingalira njira yace; Koma Yehova ayendetsa mapazi ace.**

**(Miyambo 16:9)**

Mukawona kuti mukusoweka ntendere pa nthawi imene mwapanga chisankho pitirizanibe kupephera pogwiritsa ntchito ndondomeko zimene ziri mu n’chitsazo chimene chiri mu chitsazo chakapangidwe ka zisankho. Ntendere wa muntima ndi njira imodzi mwa njira zambiri zimene mzimu amatsimikizira zisankho zoyenera. Musapange chisankho chomaliza pokhapokha mzimu wa ambuye atatsimikiza za chisankho chanu.

- **KUDZIWITSA ZA CHISANKHO**

Adziwitseni anthu za chisankho chimene mwa panga, fotokozerani bwinobwino musanayambe kupangapo kanthu.

- **KUCHITAPO KANTHU**

Mukapanga chisankho chitani monga mwa chisankhocho, simupindula chirichose podandawula ndi zolakwika za kale m’ malo mwake pakapita nthawi onaniso bwinobwino zisankho zanu.

- **KUWUNIKA CHISAKHO**

Unikani bwino bwino chisankho chimene munapanga. Kodi chinabweretsa yankho pa vuto? Kodi ndi chisakho chabwino? Kodi ndi mdalitso? Kodi mukuyenera kusintha? Zisankho zambiri zimantha kusinthidwa ngati kuli koyenera. Zisankho zambiri zimatha kukozedwanso. Mukhale omasika komaso okozeka kusintha motsogozedwa ndi nzimu woyera.

### **CHENJEZO**

Osapanga chisankho mutakwiya, kukhumudwa, komaso nthawi imene mwapanikizidwa.

Osapanga zisankho mwa change mukhale ndi nthawi yowunika bwinobwino. Zisankho zambiri

sizikuyenera kuchitidwa pompopompo. Ndi satana amene amakakamiza anthu kuti apange zinthu mwachangu. Mzimu wa a mbuye amatsogolera modekha. Osapanga zisankho mofulumira mukamatsatira ndondomeko;

**Yembekeza Yehova: Limbika, ndipo Iye adzalimbitsa mtima wako; Inde, yembekeza Yehova. Masalimo 27:14**

**Moyo wanga, ukhalire cete Mulungu yekha; Pakuti ciyembekezo canga cifuma kwa Iye Masalimo 62:5**

**Khala cete mwa Yehova, numlindirire Iye: Usabvutike mtima cifukwa ca iye wolemerera m'njira yace, Cifukwa ca munthu wakucita ciwembu. Masalimo 37:7**

**koma iwo amene alindira Yehova adzatenganso mphamvu; adzauluka pamwamba ndi mapiko monga ziombankhanga; adzathamanga kuma osalema; adzayenda koma osalefuka. Yesaya 40:31**



## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera osawonera:

---

---

2. Kodi njira yabwino yopangila zisankho monga mwa mawu a Mulungu ndi iti?

---

---

3. Lembani mwa chidule ndondomeko zisanu ndi ziwiri zopangila zisankho.

---

---

4. Kodi fanizo lopangila zisankho ndi liti?

---

---

5. Cholinga cha fanizoli ndi chani?

---

---

(Mayankho amafuso osewa ali kumapeto kwa buku lino)

## **KUPITILIZA KUPHUZIRA**

1. Chitsazo cha vuto ndi chisankho chake

### **VUTO**

Palibe aphunzitsi ophuzitsa ana Mau a Mulungu, anthu ochepa afuna kuthandiza. Nthawi zambiri amaphatikiza ma kalasi ndipo chiwerengero cha ana chikutsika.

### **ENA MWA MAYANKHO**

1. Kupepha anthu odzipereka
2. Phatikizani ma kalasi ambiri
3. Yambitsani maphuziro a aphuzitsi kuti muphuzitse aphuzitsi ambiri

### **KUWUNIKA MAYANKHO**

1. Kupepha anthu kupangitsa kuti anthu ambiri adzipereke kuyamba kuphuzitsa. Koma kodi anthuwa adzaphuzitsidwa moyenera?
2. Kuphatikiza ma kilasi kutha kuthandiza kuchepetsa vuto la amphuzitsi koma kodi ana akathandizidwa mwa padera mu kilasi lalikulu choncho?
3. Maphuziro athandiza a phuzitsi amene akufuna kulow m'malo mwa amene a nasiya.

### **KUSANKHA YANKHO LABWINO**

Yankho la chitatu ndilo labwino Maphuziro amphuzitsi athandiza pakukhula njira yokhazikika yobweretsa ndi kukozekeka a phuzitsi a tsopano. Mutha kugwiritsa nchito yakho loyamba (odzipereka) komaso (kuphatikiza ma kilasi) mpakana gulu loyamba la amphuzitsi la phuzitsidwa.

### **KUWUNIKA**

Ikatha miyezi itatu unikani bwino lomwe chisankho chanu. Kodi njira yophuzitsa aphuzitsi ikuthandiza kuthana ndi vuto losowa aphuzitsi?

1. Ganizani za chisankho chimene chimene mumayenera kupanga. Gwiritsani ntchito nondomeko imene mwaphuzira kuti mupeze chisankho.
2. Bayibulo ndi mbiri ya zisankho zimene anthu andi mayiko anapanga mogwirizana ndi chifunilo cha Mulungu. Kuti mudziwe zambiri zokhudzana ndi kupanga zisankho ndi chifuniro cha Mulungu pangani ma phuziro ndi “Harvesttime International Institute Course”.

3. Werengani zokhuzana ndi Mfumu Rehoboam amene anapeza malangizo nthawi imene amayenera kupanga chisankho. 1 Kings 12:1-19

## CHAPUTALA 9

### MIKANGANO KOMANSO MWAMBO

#### ZOLINGA:

Mukamaliza phuziroli muzikwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi lotsogolera osaonera
- Kupeza chifukwa chenicheni cha mikangano yonse.
- Kulemba mwachidule njira zopewera mikangano.
- Kulemba mwachidule ndondomeko zothetsera mikangano.
- Kuwona chifukw chani kusunga mwambo ndikofunika.
- Kulemba mwachidule njira za mawu a Mulungu zosungula mwambo.

#### VESI LOTSOGOLERA

**Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitso, citsutsano, cikonzero, cilangizo ca m'cilungamo: (2 Timoteyo 3:16-17)**

#### MAWU OYAMBA

Muchaputala 7 munaphuzira za ntchito ya atsogoleri. Ntchito ziwiri za atsogoleri ndiko ku sungitsa mwambo komaso kukhazikitsa bata. Mukamagwira ntchito komaso kutumikira anthu ntchito zimenezi ndizofunika. Kusungitsa mwambo ndi kuwalangiza amene alakwitsa.

Mikangano ikhudzana ndi ndewu komaso mikangano. Ntsogoleri wabwino ayenera kuwonetsa zoyenera kuchitika komaso kuthana ndi mafuto ochitika pakati pa anthu amene akuwatsogolera.

#### KUSIYANA MAGANIZO KOMA OSAKANGANA

Anthu atha kusiyana maganizo koma osakangana, koma mikangano nthawi zambiri imachokera ku maganizo osiyana. Sikusiyana magannizo kumene kumapweteka komaso kuwononga ena koma kulempha kukondana pamene tasiyana maganizo.

Paulo ndi Banaba anasiyanapo maganizo pa nkhani ya Maliko pa Machitidwe 15:36-41.

Kusiyana maganizo uku sikunafikre pa chidani komaso mangawa. Vuto linathetsedwa popanga gulu lachiwiri lolalikira. Gulu limeneli linathandizira kupititsa patsogolo ntchito yakulalikira uthenga wa Mulungu. Paulo ndi Banaba sanakwiye ndikusiya kulankhulana osalabadilanaso.

Palibeso amene anasiya chikhrisitu chifukwa cha kuwawidwa. Ose anapitirizabe kutumikira ambuye. Pamene anthu akumenyana sakulimbana ndi Satana. Mulungu afuna kuti anthu athane ndi mikangano komaso kusungitsa mwambo bwinobwino kuti ntchito mu ufumu wake ipitirile.

## NTCHITO YA MAWU AMULUNGU

Mawu a Mulungu ali ndi ntchito yofunika pothana ndi mikangano kapena kusungitsa mwambo.

**Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitsa, citsutsano, cikonzero, cilangizo ca m'cilungamo: (2 Timoteyo 3:16-17)**

Kusungitsa mwambo komaso kuthana ndi mikangano pogwiritsa ntchito mawu a Mulungu anthu amakozedwa pa ntchito ya Mulungu. Mawu a Mulungu ndi amphavu posungitsa mwambo kutsutsa andi kulangiza.

## MACHITIDWE A BAIBULO

Nthawi ina iliyose bungwe kapena ntchito ya Mulungu yayambitsidwa imadutsa m'miringo yosiyanasiyana ya makulidwe. Pali chitsazo cho milingo imeneyi. Werengani ma chaputala awa;

1. Machitidwe 1 Mulungu anasankha amuna ena
2. Machitidwe 2 Amunawa anaptsidwa utumiki
3. Machitidwe 3 Panali kuchulukana
4. Machitidwe 4 Gulu la anthu a chidwi linachuluka (Mpingo)
5. Machitidwe 5-6 Kusoweka mwambo komaso mikangano zinabuka

M'machitidwe 1-4 ntchito yayikulu inayambika, kenako Machitidwe 5:1-11, nkhani yakusoweka mwambo inabukanso. Petulo sanangoyisiya koma anachitapo kanthu. Mu Machitidwe 5:12-42, mikangano ya kunjira kwa mpingo inadzuka. Atumwi anatsutsidwa ndipo ananena molimba ntima

**Ndipo anayankha Petro ndi atumwi, nati, Tiyenera kumvera Mulungu koposa anthu. Ndipo masiku onse, m'Kacisi ndi m'nyumba, 2 sanaleka kuphunzitsa ndi kulalikira Kristu Yesu. (Machitidwe 5:29 ndi 42)**

Machitidwe 6:1 mikangano inabuka mu mpingo. Panali nkhangano chifukwa cha kugana zinthu zofunika kwa amayi a masiye. Ndipo atumwi anapeza mayankho pa vutoli. Akanatha khazika bata odandawula powawuza kuti mukanakhala awuzimu simukanadandawula.

Akanatha kunenaso kuti simukuyenera kuwukila utsogoleri umene yehova wawuyika. Gonjerani kapena siyani. M'malo mwake analali nawo machitidwe awutsogoleri. Anati, tanva kuti muli ndivuto. Tiyeni tiwone pamodzi, mothandizidwa ndi ambuye tipeza mayankho. (Onani Machitidwe 6:2-7)

Nthawi ina iliyose utumiki kapena ntchito ya ambuye yakhazikitsidwa imakumana ndi zinthu zofanana ndi zimenezi. Padzakhala Mavuto okhudzana ndi mwambo, komaso mikangano yochokera kunjira. Satana kufuna kuwononga utumiki.

Mukuyenera kukumbukiraso kuti amene akutsogozedwa ndi mzimu amakhalaso pa mikangano ndi anthu amene akutsogozedwa (pa nthawi imeneyo) ndi thupi (Onani mikangano inachitika ndi Yesu mu ziphuzitso zotsatila)

Mtsogoleri wabwino sathawa nyengo ngati zimenezo. Samatchula anthu opanda uzimu pobweretsa Mavuto kwa iye. Amathana mofulumira ndi zinthu zokhudzana ndi kusoweka mwambo komaso mikangano.

### **CHIFUKWA CHENICHENI CHOPANGILA MIKANGANO**

Baibulo limawonetsa zifukwa zenizeni zoyambitsa mikangano pakati pa okhulupirira, mpingo komasno mautumiki a Chikhristu.

**Koma mukakhala nako kaduka kowawa, ndi cotetana m'mtima mwanu, musadzitamandira, ndipo musamanama potsutsana naco coonadi. Nzeru iyi, sindiyo yotsika kumwamba, komatu iri ya padziko, ya cifuniro ca cibadwidwe, ya ziwanda. Pakuti pomwe pali kaduka ndi zotetana, pamenepo pali cisokonekero ndi cocita coipa ciri conse. (Yakobo 3:14-16)**

**Zicokera kuti nkhondo, zicokera kuti zolimbana mwa inu? Kodi sizicokera ku zikhumbitso zanu zocita nkhondo m'ziwalo zanu? (Yakobo 4:1)**  
**pakuti, pokhala pali nkhwidzi ndi ndeu pakati pa inu simuli athupi kodi, ndi kuyendayenda monga mwa munthu? (1 Akorinto 3:3)**

Mikangano imayamba chifukwa cha ukhanda mu uzimu, akhristu amene ali ndi zeru za umunthu olimbikitsidwa ndi Satana, thupi komanso kudzikonda.

### **KUPEWA ZIWAWA**

Njira zabwino zothetsera ndi kupewera zipolowe ziripo. Njira ziwiri zopewera zipolowe ndi izi;

1. Kudzutsa mtundu wa anthu akhwima muwuzimu (Yakobo 3: 14-16; 4:1; 1 Akorinto 3:3)
2. Kupanga anthu kukhala ozindikira. Chisokonezo komaso kusoweka kwa uthenga kumabweretsa Mavuto. Kukhala ndi njira zabwino zoperekera uthenga pakati pa anthu amene mukuwatumikira. Azitsogoleri abwino mu Bayibulo (Monga Moses, Nehemiah, Ezra, etc.) anali anthu odziwa kupereka uthenga.
3. Mukamachita ntchito yabwino ya Mulungu, Mavuto salephera. Pangani anthu kudziwa kuti mukuyembekezera mavuto kuti simudzidzimuka akayambika, ndipo kuti mukudziwa kuti mukwanitsa kupeza mayankho mwa mphamvu ya Mzimu wa Mulungu.

4. Ganizani za patsogolo. Pokonzekera bwinobwino mungapewe mavuto ambiri asanayambitse mikangano.
5. Pangani maubale ambiri. Nenani zabwino zokhudza anthu ena. Ndipo phuzitsani amene mukugwira nawo ntchito mu utumiki.
6. Yamikirani komanso thokozani onse amene mukugwira nawo ntchito mu utumiki
7. Mukalakwa vomerezani ndipo sinthani.
8. Zolinga komanso ndondomeko za utumiki wanu zikhale zomveka bwino. Mutha kuchepetsa mwayi wa mikangano ngati wina aliyese akakhala odziwa bwino zimene mukuchita komanso chifukwa chimene mukuchitira.
9. Ngati kuli kofunika kupanga malamulo, apangeni oveka bwino andipo afotokozereni bwino lomwe kwa athu onse.
10. Pezani nthawi yokhala ndi anthu amene mukugwira nawo ntchito kuti mudziwe mavuto akakhalapo. Mukapanda kukhala ndi nthawi mavuto ang'ono amatha kuyambitsa mikangano.
11. Yendetsani utumiki potsatira mfundo za m'Baibulo.

## KUTHANA NDI MIKANGANO

Ngati mavuto kapena mikangango yayambika, tsatirani ndondomeko izi:

1. Khalani pafupi kuti mupeze mayankho. Simungathane ndi vuto ngati mwatalikira.
2. Pephererani zero kuti muthane ndi vuto.
3. Pezani vuto lenileni, mikangano sivuto lenileni. Ndi chani chimene chayambitsa mikangano. Kutu mupeze vuto yambani kufunsa mafunso. Onetsetsani ndipo pitilizani kupepherera mavumbulutso. Vetserani mbali zose za vuto komaso kuchokera kwa anthu ose okhudzidwa. Musachite zinthu musanavetsetsa bwino. Onetsetsani kulingalira kulingalira zokhudzana ndi chiyambi chenicheni cha vuto (Yakobo 3:14-16; 4:1, 1 Akorinto 3:3).
4. Lolani athu okhudzidwa kupereka maganizo awo pothana ndi vuto. Mukhale ofuna kuva maganizo kuchokera kwa anthu onse. Pepherani pamodzi pa mayankho amene apezeka. Kusala kudya ndikovomerezekanso pa mikangano imene ndi yayikulu.
5. Ngati mikangano ikudzana ndi mavuto awo ngati anthu abweretseni pa modzi potsatila mfundo ya pa Mateyu 18:15-17.
6. Mukhale ndi maganizo abwino mukamayankha Mavuto. Mukhale okhululukirana komanso khalani ofunafuna kukozanso ubale. Khalani okonda. Musaopseze komanso musakwiye. Musalole anthu ku kuwana kapena kuyankhulana mawu olakwika. Pangani mochenjera. Kupanga mochenjera ndi kukhala ndi kuthekera kuthana ndi vuto mwa nzeru komanso mwa chikondi posalakwila anthu. Zimakhudzana ndi kukhala wa tcheru ndi anthu. Kukhala ovetsera, ndi kugwiritsa ntchito mawu kukozanso komanso kuchilitsa osati ku wagawa anthu komanso kukhumudwitsa. Nkhalani okonzeka kusintha. Modzikonda musakhale ndi mbali yanu. Mukhalenso ovetsera bwino ku njira zina zothanirana ndi mavuto.
7. Yambani mwanthana ndi vuto limodzi musanayambe lina. Musasokonezedwe pokambilana zinthu zina.
8. Mukavetsetsa bwino chimene chikuyambitsa mikangano musachedwe kuchitapo kanthu. Kumbukirana kuti yankho lipititse patsogolo ufumu wa Mulungu. Potsatila chitsanzo cha Paulo ndi Banaba thanani ndi mikangano pokhazikitsa magulu.



9. Fotokozerani chifukwa chimene mukutsatila njira imene mwasankha pothana ndi mavuto. Mwachitsazo pa Machitidwe 15 atsogoleri anafotokoza chifukwa chimene anasankhira njira yawo momveka bwino komanso polemba.
10. Yamikani ambuye chifukwa cha vuto komanso chifukwa chakuti mwaphuzirapo. Mukamayamika Ambuye chifukwa cha zonse zimapangitsa mphamevu ya Mulungu kugwira ntchito m'malo anu.

### **ZIFUKWA ZO SUNGUTSIRA MWAMBO**

Ndichikhalidwe chauchimo kuwukira ulamuliro. Ichi ndi chimene chinapangitsa uchimo wa Lucifala (Satana) komanso munthu (Adamu ndi Eve). Chifukwa cha chikhalidwe chimenechi chau chimo, nthawi zina mukuyenera kutsogolera nthawi zina amene sakufuna kutsogoleredwa. Mbusa komaso ntsogoleri wa chipembedzo ali ndi ulamuliro wosungitsa mwambo mu mpingo kapena utumiki chifukwa ali ndi udindo oyang'anaira moyo wauzimu wa anthu.

**Mverani atsogoleri anu, nimuwagonjere; pakuti alindirira moyo wanu, monga akuwerengera; kuti akacite ndi cimwemwe, osati mwacisoni: pakuti ici sicikupindulitsani inu. (Ahebri 13:17)**

Mtsogoleri ayenera kukhala okozeka kuchitapo kanthu pa mavuto okhudzana ndi kusungitsa mwambo akachitika. Kuvomera kuti ntchimo kapena kulephera kw moyo wa wuzimu kuti anthu asachitepo kanthu.

1. Kubwezeretsa munthu amene akukana mawu a Mulungu kapena amene wa pereka zifukwa zakulakwa kwake. (Agalatiya 6:1; Mateyu 6:14-15)
2. Kulangiza za uchimo (1 Akorinto 8:9)
3. Kuteteza umboni wa akhristu mu mpingo: (1 Timothy 3:7)
4. Kulimbikitsa otsatira kukhala mboni zokhulupirika ndiposo kuti asakhale osasamala: (1 Akorinto 5:6-7)

### **MFUNDO ZOSUNGITSIRA MWAMBO**

Zotsatirazi ndi ndondomeko zosungitsira mwambo;

1. Choyamba kumanani ndi mwalakwilana naye kuti mu lumikizane ngati anthu panokha ngati nkotheke: (Luka 17:3; Mateyu 18:15-17).

2. Ngati mbale amene walakwitsa sakuvera komaso kulapa pitaniso ndi mboni; Mateyu 18:15-17.
3. Ngati akukanabe kukuverani pita nayoni nkhaniyo kwa ku mpingo; (Mateyu 18-15-17)
4. Kusungitsa mwambo kukuyenera kuchitika ndi atsogoleri a mzimu woyenera. Onani Mateyu 7:1-5; Aroma 15:1-2; 2 Akorinto 2:6-8, komaso Galatiya 6:1-4. Okhulupirial okhwima muwuzimu akuyenera adziweruze okha kenako amene analakwitsa ndi mzimu wodzichepetsa, chikondi komanso kuthandizana.
5. Chilangizo chichitike ndi mtima wobwezeretsa wolakwa amene watengedwa ukapolo ndi satana. 2 Timoteo 2:24-26
6. Ngati kulangiza kwakanika, kusungitsa mwambo kungachitike pomuchotsa olakwa mu m'chiyanjano. Imodzi mwa Mphatso yabwino imene akhristu anapatsidwa ndi chiyanjano cha pa abale. Chimodzi mwa zilango zimene choopswa kwambiri ndi kukaniza muthu kuchiyanjano cha pa abale. Onani Mateyu 15; 15-17; 1 Akorinto 5; 2 Atesalonika 3:14; 2 Yohane 7-11; komanso 3 Yohane 9:11.
7. Mwayi upatsidwe kwa olakwa kuti ayankhepo. Mawonedwe ake azithu amakhudza kusungitsa mwambo komaso tsogolo la utumiki. Ngati akuwona zinthu molondola komaso walapa mtogoleri akhoza kumubwezeretsaso mutumiki. Ngati cholakwacho chiri chachikulu, olakwirayo ayenera kuyimitsidwda mpakana moyo ndi utumiki wake zitakozedwanso. Ngati ali owukira ndipo sakulapa, akuyenera kuchotsedwa pa wutsogoleri komaso mu mpingo.
8. Mavuto a chisisi komaso machimo osabisika akuyenera wonedwa mosiyana. Onani Mateyu 18:15-17; 1 Akolinto 5; Galatians 2:1-14; 1 Timothy 5:20. Nkhani yopezeka m'buku la Mateyu zikuwoneka kuti vuto linalipo pakati pa anthu awiri. Limayenera kuthetsedwa pothandizidwa ndi okhulupirila ndipo ngati wolakwa sanavera pomuyimitsa ku chiyanjanao. M'dime zina inali nkhani yokhudza gulu ndipo imayenera kukhudza gulu pothana nayo.
9. Sungitsani mwambo pokhapokhapo muli ndi mfundo zowona. Onani (Mateyu 18:15-18; 1 Akorinto 5:1, 9.)

### **MALAMULO OFUNIKA KUWAKUMBUKIRA**

Lamulo labwino lofunika kukumbukira mukamasungitsa mwambo ndi (Mateyu 7:12).

Mukuyenera kumadzifusa mafuso awa:

1. Kodi mawu a Mulungu akuti chani pa izi?
2. Kodi Yesu akanachita chani pa izi?
3. Kutakhala kuti mawundindo tasinthana ndi iyeyu ndipo ndiri mu nyengo imeneyi ndikanakonda kuti chichitike ndi chani kwa ine?

## MAFUSO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osonera.

---

---

2. Lembani ndira zopewera mikangano.

---

---

3. Lembani mwachidule ndondomeko zothetsera mkangano.

---

---

4. Lembani zifukwa zosungitsira mwambo mogwirizana ndi Baibulo.

---

---

5. Lembani mwachidule mfundo za M'baibulo zosungitsira mwambo zimene mwaphuzira.

---

---

6. Kodi chifukwa chenicheni cha mikangano ndi chani?

---

---

7. Chifukwa chani Mau a Mulungu ali ofunika posungitsa mwambo?

---

---

(Mayankho amafuso osewa ali kumapeto kwa bukuli)

## KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

Pali zifukwa zodziwikiratu za kusungitsa mwambo m'mabungwe a Chikristu komanso mu mpingo.

Mbale kapena mlongo.

- Khalidwe loyipa (machimo okhudzana ndi kugonana, kugonana, kuwonerela zithuzi zolawula, chiwerewere)
- Kusakhulupirika pa chuma cha mpingo, chuma chake ngati munthu, kapena nkhani ya malonda.
- Ndi osakhulupirika
- Sangagwire ntchito limodzi ndi anthu ena.
- Ali ndi makhalidwe oyipa akuwukira, kutsutsa komaso udani.
- Wachikunja, wokhazikika pa ntchito za thupi komaso wosakhwima muwuzimu.
- Kuwonetsa machitidwe kapena khalidwe lake.
- Sakukwaniritsa undindo wake ngati mtsogoleri.
- Sakhulupirila Mau a Mulungu.
- Amalakhula za ena komanso kupangitsa ziwawa.

Mungaganize zifukwa zina.

1. Nthawi zina atsogoleri amakhala pa mikangano ndi owatsatira chifukwa sakwanitsa kupirira pamene akutsutsidwa. Wotsutsa ndi munthu amene amena ngati sagwirizana ndi m'mene ukupangira zinthu. Kutsutsa mwachikondi kumathandiza. Zimathandiza kuti kozanso zithu zina. Kutsutsa kwina kumachitika mosoweka chilungamo. Maganizo ena am'mene mungachitile mukatsutsidwa ndi awa;
  - Mukhale anthu ovetsera bwino kuzimene otsutsa akunena.
  - Muthokozeni chifukwa chobweretsa nkhani kwa inu ndipo mumuwuze kuti mufufuza ndi kupemphera pa nkhani yonenedwayo.
  - Pepherani chifukwa cha kutsitsidwa ndipo pepherani kwa Mulungu kuti akuwonetseni ngati iri nkhanidi yofunika kuti ikozedwe.
  - Fufuzani; kodi munapanga chisankho cholakwika? Kodi mukupanga zolakwika?

Pezani mfundo zowona zimene muzigwiritse ntchito popanga zisankho.

Ngati mungapeze kuti kutsutsa kunachitika posoweka chilungamo, zisiyeni. Ngati ziri zowona sinthani.

1. Yesu anatsutsidwa kwambiri muwutumiki wake pa dziko lapasi. Werengani m'mene Yesu anachitira m'thawi imeneyi.
  - Ndi ophuzira ake pa nkhani ya maudindo: Marko 9:33-37
  - Ndi a falisi pa atachilitsa munthu tsiku la sabata: Mateyu 12:9-14
  - Ndi afalisi atatulutsa ziwanda: Mateyu 12:22-25
  - Ndi Afalisi komaso Asaduki amene amafuna kuti awonetsere mphavu yake popanga zodabwitsa: Mark 16:1-4
  - Ndi osinthitsa ndalama mu tchalitchi: Marko 11:15-18
  - Ndi bwalo lalikulu la Afalisi komaso atsogoleri a Chiroma chifukwa sanakane kuti simwana wa Mulungu: Marko 14:60-63; 15:15.
2. Ziripo zitsazo zambiri M'baibulo zowonetsa m'mene atsogoleri anachitirapo pankhani ya mikangano komaso kusungitsa mwambo. Ndipo anapambana m'machitidwe awo. Werengani ndime izi:
  - Mose: Eksodo 18:13-26
  - Mfumu Solomo:1 Mafumu 3:16-28
  - Nathani atsutsa Davide: 2 Samueli 12
  - Samueli astutsa Saulo: 1 Samueli 15
  - Nehemiya: Nehemiya 13: 23-25
  - Atsogoleri achipembedzo ku Yerusalemu: Machitidwe 15
  - Mulungu kusungitsa mwambo okhulupirira: Ahebeli 12:5-7
  - Mtumwi Paulo: Agalatiya 2:11.

## CHAPUTALA 10

### KUPHUZITSA ATSOGOLERI NDI OPHUNZIRA

#### ZOLINGA:

Mukamaliza phunziro muzikwanitsa kuchita izi:

1. Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera.
2. Kufotokoza chifukwa chophuzitsira atsogoleri komaso owatsatira.
3. Kufotokoza chifukwa chani kuphuzitsa ena ndi ntchito yofunika.
4. Kuona njira zisanu ndi imodzi zimene Yesu anagwiritsa ntchito posankha.
5. Kuona njira zisanu ndi zitatu zimene Yesu anagwiritsa nchtito pophuzitsa.
6. Kupereka chitsanzo cha ndondomeko yophuzitsira monga ma Baibulo.

#### VESI LOTSOGOLERA

**Wophunzira saposaphunzitsi wace; koma yense, m'mene atakonzedwa mtima, adzafanana ndi mphunzitsi wace. (Luka 6:40)**

#### MAU OYAMBA

Atsogoleri akuyenera kukhala ndi owatsatira. Mu mpingo wamba siwina aliyese amene akhoza kuphuzitsa atsogoleri komaso owatsatira. Koma tsogolo lampingo limadalira kwambiri iwo. Kuphuzita atsogoleri ndi owatsatira kukuyenera kuyamba akhristu akanalu achichepere kuwakozekeza kutengapo mbali mumpingo wa Mulungu. Maphuziro akuyenera kutsatana ndi chipulumutso posatengera zaka za munthu.

Mwaphuzira kuti kwa ena Mulungu anapereka Mphatso yapadera ya utsogoleri. Ena amabadwa ndi kuthekera kwa utsogoleri. Ena mwachilengedwe ndi otsogoleredwa. Wina aliyese anayitanidwa kukhala otsogolera komaso otsogoleredwa. Atsogoleri komaso otsatila ose amafuna Mulungu posatengera kuti ndi a luso lobadwa nalo kapena andi mpatso imene Mulungu anapereka. “Aliyese kuphuzitsa m’modzi kuti akaphuzitse wina” ndi yankho lamulungu pothana ndi vuto losowa atsogoleri.

**Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphuzitsa enanso. (2 Timoteo 2:2)**

Mu chaputala ichi muphuzira kukaphuzitsa atsogoleri ndi otsatila awo.

#### OTSATIRA

Wina aliyese amatsatira mzake. Paulo akudzitchula ekha otsatira Yesu ndipo akupempha Akorinto kuti amutsatire.

**Khalani onditsanza ine, monga inenso oditsanza Kristu. (1 Akolinto 11:1)**

Malangizo omwewo anapatsidwaso kwa Aifeso (Efeso 5:11), Afilipo (Afilipo 3:17), ndi Atesalonika (Atesalonika 6:1).

Mkristu aliyese akuyenera kuphuzitsidwa kukhala otsatira wabwino. Ambiri a ife sitifuna kukhala otsatira koma timafuna titakhala ongotsogolera. Koma ntsogoleri wabwino choyambirila amkhala mtsogoleri. Mtsogoleri amayenera kuyang'anira kwa wina wake apa zitanthauza kuti amatsogoleredwa. Timatsogolera bwino potsatira bwino.

Kukhala otsatira wabwino munthu ayenera kuvera atsogoleri ndi kugonjera kwa iwo kuti ntchito yawo ayigwire mokondwera:

**Mverani atsogoleri anu, nimuwagonjere; pakuti alindirira moyo wanu, monga akuwerengera; kuti akacite ndi cimwemwe, osati mwacisoni: pakuti ici sicikupindulitsani inu. (Ahebeli 13:17)**

Anthu atsatiye atsogoleri awo pokha pokhapo akutsatira Khristu. Atsogoleri akatalikirana ndi Mau a Mulungu musawatsatiye.

**ATSOGOLERI**

Wina aliyese sanayitanidwe kukhala mtsogoleri mu mpingo, koma munjira zosiyanasina wina aliyese amatsogolera nthawi zambiri. Mwa chitsazo munthu akhoza kukhala kuti sanayitanidwe kuti akhale mtsogoleri ku mpingo koma ndi ntsogoleri kunyumba kwake.

Okhulupirila akhoza kukhala opanda Mphatso ya utsogoleri koma atha kuthaniza ngati ntchito itapezeka ku chalitchi chawo. Chifukwa cha ichi aliyese akuyenera kuphuzitsidwa za utsogoleri mu mpingo.

**UDINGO WOFUNIKA**

Kuphuzitsa ena ndi udindo ofunika kwambiri chifukwa...

**Wophunzira saposi mphunzitsi wace; koma yense, m'mene atakonzedwa mtima, adzafanana ndi mphunzitsi wace. (Luka 6:40)**

Anthu ophuzitsidwa adzakhala ngati imu! Mukuyenera kupereka chitsazo pa makhalidwe anu ndi moyo wanu.

**Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansu pano. (Mateyu 28:19-20)**



Atsogoleri ndi anthu otsatira amaphuzitsidwa ndi cholinga chofikira kwa anthu amitundi yose, kuphuzitsa uthenda wabwino, kubatiza ndi kuwathandiza otembenuka mtima kuti akule moyo wawuzimu. Anthu akuyenera kuva mawu kuti atembenuke ntima, alape machimo awo ndi kubadwaso mwatsopano. Chiphunzitso ichi ndiye kulalikira.

**Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: (Mateyu 28:19)**

Okhulupilira amatchulidwaso kuti otembenuka ntima. Otembenuka ntima ndi munthu okhulupirira amene wabadwa mwatsopano ndipo walowa muufumu wa Mulungu. Koma otembenuka ntima ayenera kuphuzitsidwa kuti akhale ophunzira. Otembenuka ntima akuyenera kuphuzitsidwa m'zonse zimene Yesu anaphunzitsa.

**ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya panso pano. (Mateyu 28:20)**

Ndondomeko ya Mulungu ndi yakuti otembenuka ntima akhale ophuzira. Mawu akuti ophuzira atanthawuza kuti amene amaphuzira potsatira. Otembenuka ntima ndi otsatira amene wakhazikika pa mfundo za mayambidwe a chikhulupiriro cha Chikhristu ndipo alinako kuthekera kopeza kophuzitsaso ena. Akamapanga izi amakhala mtsogoleri. Izi zikamachitikachitika otsatira komanso atsogoleri amachuluka ndipo amathandizira kupititsa patsogolo ufumu wa Mulungu.

### **OTEMBENUKA MTIMA, KUKHALA OTSATIRA, KUTSOGOLERA**

Kodi anthu mumawotsogolera bwanji kochokera otembenuka ntima kukhala okhulupirira (Otsatira) komanso atsogoleri. Mukuyenera kuwaphunzitsa. Kukhala ndi otembenuka ntima ndi chinthu chapatali, koma pokhapokha ataphunzitsidwa ndi pamene adzapereka zipatso muzimu. Yesu anawonetsera izi pamene anasankha ophunzira ndi kuwaphunzitsa kuti akhale ophuzira. Anali ndi zaka zitatu ndi miyezi isanu ndi umodzi zautumiki zimene amayenera kugwira ntchito imene anapatsidwa. Anayenda malo owerengeka nthawi imene anali nayo anaphuzitsa anthu owerengeka. Kuti awonetsetse kuti ntchito yatha Yesu anayika patsogolo ntchito yophuzitsa omutsatira ndi atsogoleri. Anadziwa kuti amene awaphuzitse adzafikira anthu ambiri m'midzi ndi m'mizinda imene iye sakanakwanitsa.

### **MFUNDO ZOSANKHIRA**

Ndiwe munthu m'modzi amene uli ndi nthati koma sungaphuzitse aliyese. Izi zitanthawuza kuti ukuyenera kusankha amene udzaphuzitse. Ungasankhe bwani amene udzaphuzitse? Ukuyenera kugwiritsa ntchito maphuziro, thawi imene muthu wakhala ali muwutumiki, mayeso kapena pongosankhapo chabe.

Koma njira yabwino yogwiritsa ntchito posankha ndi imene Yesu anayigwiritsa ntchito posakha akuphuzira ake. Mbiri yakusakha kwake inapatsidwa pa Mateyu 5:1; 10:2-4; Marko 3:13-19; Luka 6:12-16; ndi Luka 10:1-16. Mfundo zimene Yesu anazitsatira zimeneso inu mukhoza kuzigwiritsa ntchito posakha oti muwaphuzitse.

### **DALIRANI MULUNGU**

Yesu anadalira Mulungu:

**Sindikhoza kucita kanthu kwa Ine ndekha; monga momwe ndimva ndiweruza; ndipo maweruzidwe anga ali olungama; cifukwa kuti sinditsata cifuniro canga, koma cifuniro ca Iye ondituma Ine. (Yohane 5:30)**

### **IPANGENI IKHALE NHANI YAPEMPHERO**

Luka 6:12-13 anena kuti Yesu anakhala usiku wose akupemphera asanasakhe akuphunzira ake. Pepherani kwa Mulungu kuti akupatseni nzeru yosankha amuna ndi akazi okhulupirika kuti muwaphunzitse.

### **CHITANIPO KANTHU**

Yesu anachitapo kanthu poyitana ophunzira. Anthu sangabwere kwa inu kuti akhale aphunzitsi kapena ophunzira. Mukuyenera kuchitapo kanthu kuti ndi kuwaitana.

### **MUYANG'ANE KUTHEKERA OSATI MAVUTO AWO:**

Yesu atasankha ophuzira, anayitana anthu wamba. Ena anali ophuzira ndipo ose anali ndi mavuto komaso zofoka. Zakhala zikunenedwa kuti ophuzira once 12 akanati afufuzidwe ndi mabungwe akufalitsa akanakanidwa.

Koma Yesu anayang'ana kuthekera osati mavuto. Sanasankhe amuna kapena akazi chifukwa cham'mene analiri koma chifukwa cha chimene adzakhale. Anayang'ana modutsa mavuto kufikira kukuthekera kwawo.

### **ZOFUNIKA ZIDZIWIKE**

Pamene Yesu anasankha ophunzira ananeneratu zimene zofunika. Ophunzira weniweni kapena mtsogoleri akuyenera kudzika.

**Cifukwa cace tsono, yense wa inu amene sakaniza zonse ali nazo, sakhoza kukhala wophunzira wanga. (Luka 14:33)**

Akuyenera kudzikana yekha poseza ntanda:

**Ndipo amene ali yense sasenza mtanda wace wa mwini yekha, ndi kudza pambuyo panga, sakhoza kukhala wophunzira wanga, (Luka 14:27)**

Akuyenera kunditsata Yesu:

**Pomwepo Yesu anati kwa ophunzira ace, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikane yekha, natenge mtanda wace, nanditsate Ine. (Mateyu 16:24)**

Ufumu wa Mulungu ukuyenera kuikidwa patsogolo:

**Cifukwa cace musadere nkhawa, ndi kuti, Tidzadya ciani? kapena, Tidzamwa ciani? kapena, Tidzabvala ciani? Koma muthange mwafuna Ufumu wace ndi cilungamo cace, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu. (Mateyu 6:31, 33)**

Mulungu analonjeza kupereka zofuna zonse ngati munthu ataika patsogolo ufumu wake.

Otsatira ayenera kukhala kapolo wa once:

**Kumkwanira wophunzira kuti akhale monga mphunzitsi wace, ndi kapolo monga mbuye. Ngati anamucha mwini banja Beelzebule, sadzaposi kodi kuwaterno apabanja ace? (Mateyu 10:25)**

Koma sizidzakhala choncho pakati panu. Aliyese adzakhala wankulu pakati panu akuyenera kukhala ntumiki wa once.

Ndipo aliyese amene akhala mfumu pakati panu ayenera kukhala kapolo;

**Sikudzakhala comweco kwa inu ai; koma amene ali yense akafuna kukhala warnkuru mwa inu, adzakhala mtumiki wanu; ndipo amene ali yense akafuna kukhala woyamba mwa inu, adzakhala kapolo wanu: monga Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa koma kutumikira, ndi kupereka moyo wace dipo la anthu ambiri. (Mateyu 20:26-28)**

### **SANKHANI AMENE ALI NDI ZOFUNIKA**

Paulo anawuza Timoteo kuti asankhe anthu okhulupirika ndipo awadalire ndi zinthu zimene anawaphuzitsa. Anthu okhulupirika amenewa amayenera kukhala nako kuthekera koti atha kuphuzitsa ena. Zinthu zofunika kwambiri ndi kukhulupirika komaso kukwanitsa kuphuzitsa ena. Ngati munthu ali osakhulupirika sangakwaniritse kupereka zipatso zauzimu. Ngati ali osakhulupirika koma sangaphunzitseso ena athaso kulephera.

Kukhulupirika kumakhudzana ndi kukula moyo wawuzimu. Paulo akulankhula za okhulupirila mene amayenera kuphuzitsa ena koma sanakule moyo wawo wawuzimu. Anthu awa sanakozeke kuti akhale ophuzira enieni. Ayenera aphunzitsidwebe za mayambidwe achikhulupiriro.

Sikuti anthu okhulupirika ndi anthu opanda zofoka. Ndi anthu amene akukula muchikhalidwe cha khristu m'moyo wawo. Ngakhale anthu okhulupirika ali ndi mavuto komaso zofoka zofunika kuzigonjetsa monga m'mene ophuzira oyamba analiri.

Dziko lapasi limatenga anthu amphatso ndikuwapatsa chikhalidwe. Amayima pa kudziwa zinthu. Mulungu anati sankhani okhulupirika, akhalidwe labwino ndipo iye adzapereka Mphatso komaso maluso osiyanasiyana awuzimu ndi kuthekera. Anthu okhulupirika alipo kuti amalizitse cholinga cha Mulungu. Yesu ataitana Simoni ndi Andrey, pompo anasiya Makoka awo. Mawu akuti pompo atanthawuza kupezeka.

Mukasankha amuna ndi akazi oti muwaphuzitse akuyenera kuti muziwaphuzitsa. Akuyenera kuti m'moyo wawo aike patsogolo kukhala ophuzira. Anthu okhulupirika amalimbikitsidwa ndi masophenya awuzimu. Yesu atapereka masophenya osodza amuna ndi akazi kwa Simoni ndi Andrey zinawalimbikitsa kusiya makoka awo.

Anthu okhulupirika amakhala ndi njala ya uzimu monga akuphuzira a Yesu. Mitima yawo inatetha pamene amagawana nawo malemba (Luka 24:32, 45). Anali ofuna ndi othunthumira kuphuzitsidwa. Anthu okhulupirika amdziwika ndi chikondi cha pa Ambuye komanso anthu. Lamulo loyamba komanso lachiwiri amayikapo mtima:

**ndipouzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse, ndi mphamvu yako yonse. Laciwiri ndi ili, Uzikonda mnzako monga udzikonda mwini. Palibe lamulo lina lakuposa awa. (Marko 12:30-31)**

## **MFUNDO ZOPHUZITSIRA**

Atasankha ophuzira, Yesu anawonetsa mfundo zisanu ndi zitatu zophunzitsira iwo:

### **1. UBALE**

Yesu ataitana ophuzira ake, anawaitana kuti akhale naye, ndimoyo wake wose anadzipereka kwa iwo. Anali ndi nthawi yokhala nawo pa nthawi imene amatumikira komaso kungakhala ngati abwezi ake. Simungagwiritse ntchito misonkhano ya atsogoleri kapena mapephero a tsiku la sabata okha kuti muphuzitse atsogoleri ndi ophuzira. Pakuyenera kukhala ubale ndi amene

mukufuna kuwaphuzitsa. Mukuyenera kugawana nawo moyo wanu. Mukuyenera kuwadziwa, mavuto awo, mulingo wa moyo wauzimu ndi zinthu zina.

## **2. CHIYERETSO**

Chiyeretso chinayambika kuchokera kubale umene anali nawo ndi Yesu. Yesu anaitana ophuzira kwa iye osati mpingo kapeana bungwe. Maitanidwe amenewa akwa Mulungu amafunika kuvera kwakukulu ku mawu ndi cholinga chake. (See John 4:34; 5:15:10; 17:4; ndi Luka 22:42)

## **3. MASOPHENYA**

Yesu analimbikitsa ophuzira ake powapatsa masophenya. Anawaitana kuti afuse zazikulu kusiyana ndi zinthu zikuluzikulu osati zokhudzana ndimoyo wa tsiku ndi tsiku. Anainidwa kuti akhale asodzi awanthu (Mateyu 4:19). Anawapata masophenya a kholola la dziko lose.

Anawalimbikitsa ndi mavumvulutso a ufumu wa Mulungu. (Mateyu 13)

Opanda masophenya anthu amawonongeka (Miyambo 29:18). Alibe chilimbikitso komaso chitsogozo. Mukamaphuzitsa awuzeni masomphenya kuti mulimbikitse cholinga. Cholinga ndi choti uthenga ufalikire pa dziko lose lapasi ndi uthenga wabwino. Osasokonezeka ndi chinthu china.

## **4. MALAMULO**

Nthawi yambiri ya moyo wake yesu anakhala akuphuzitsa uthenga wabwino. Malamulo ake amakhudzana ndi masophenya amene anawapatsa. Mukuyenera kuphuzitsa zimene iye anaphuzitsa ngati mufuna kutsatira chitsazo chake pophuzitsa atsogoleri. Izi ndi mbali imodzi ya zimene zinalamulidwa kuchitika lalikira kwa anthu onse (Mateyu 28:20).

Zimphuzitso za Yesu zikuyenera kuphuzitsidwa motsindika ndi zimene zinavumbulitsidwa pamene zinkagwiritsidwa ntchito mu mpingo woyamba. Izi zitanthawuza kuti ziphuzitso zikuyenera kuima pa Uthenga wa bwino ndi Makalata amene analembedwa mu nchipangano chatsopano. (Harvesttime Internatioal Institute curriculum imapereka maphuziro amenewa. Harvesttime imaperekaso maphuziro ngati “Luso la Kaphuzitsidwe” zimene zimaphuzitsa kaphuzitsidwe pogwiritsa ntchito njira za yestu khristu.

Mukamaphuzitsa zimene Yesu anaphuzitsa, mumaphuzitsa mavumbulutso onse a mawu a Mulungu chifukwa amaima pa chipangano chakale. Yesu anati:

**Ndipo anati kwa iwo, Awa ndi mauwo ndinalankhula nanu, paja ndinakhala ndi inu, kuti ziyenera kukwanitsidwa zonse zolembedwa za Ine m'cilamulo ca 6 Mose, ndi aneneri, ndi masalmo. ndipo anati kwa iwo, 8 Kotero kwalembedwa, kuti Kristu amve zowawa, nauke kwa akufa tsiku lacityatu; ndi kuti kulalikiidwe m'dzina lace kulapa ndi 9 kukhululukidwa kwa macimo kwa 10 mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu. (Luka 24: 44, 46, 47)**

## **5. KUONETSERA**

Yesu sanaphuzitse pogwiritsa ntchito mawu okha chabe. Anawonetsera zimene amaphuzitsa. Yesu anaphuzitsa machiritso ndipo anawonetsera pochiritsa odwala. Anaphuzitsa ulamuliro wa okhulupirira kwa satana ndipo anawonetsera potulutsa ziwanda. Anaphuzitsa za kukhudzika ndi osawuka ndipo anawonetsera opodyesta makamu.

**CIMENE cinaliko kuyambira paciyanbi, cimene tidacimva, cimene tidaciona m'maso mwathu, cimene tidacipenyenera, ndipo manja athu adacigwira ca Mau a moyo, (1 Yohane 1:1)**

Yesu anaphuzitsa powonetsa chitsazo. Anawonetsa zomene anaphuzitsa ndi makhalidwe ake komaso utumiki. Iye anati:

**Pakuti ndakupatsani inu citsanzo, kuti, monga Ine ndakucitirani inu, inunso mucite. (Yohane 13:15)**

Kuwonetsedwa kwa mphavu kumapangitsa anthu kuvetsera uthenga:

**Ndipo makamuwo ndi mtima umodzi anasamalira zonedwa ndi Filipino, pamene anamva, napenya zizindikilo zimene anazicita. (Machitidwe 8:6)**

Kuwonjezera kulalikirira zakuti uthenga wabwino ndi owona (Agalatiya 2:5) Paul analalikiraso kuti ndiwaphavu (Aroma 1:16). Analengeza komaso kuwonetsera uthenga wabwino (1 Corinthians 2:1, 4). (Harvest International Institute has a course entitled “Mfundo za utsogoleri” imene imanena za mutu umenewu.

## **6. MACHITACHITA**

Uthenga chabe siwokwanira, kuti ukhale opundula, uthenga umayenera kugwiritsidwa ntchito. Pamayenera kukhala nthawi yochitapo kanthu. Kuwonjezera kuvetsera ziphuzitso za Yesu komaso kuwona chiwonetsero cha mphavu yake, akuphuzira analiso amachititachita. Kuphuzitsa

chabe sikokwanira kuti maphuziro atheke. Kuphuzitsa kokha ziringati kuyesera kuphuzira kuthandiza munthu powerenga buku.

Akuphuzira akuyenera kukumana ndi zinthu zokhudzana ndi zimene iwo akuphuzira. Akuyenera kudziwadi kuti kulalikira uthenga, kupepherera odwala, kutulutsa ziwanda, ndi zina. Yesu anapereka mwayi umenewu kwa ophuzira ake. Werengani Marko 6:7-13 and Luka 9:-6. Yesu anatuma akuphuzira ake kuti akawone zimene anaphuzitsidwa. Amene munawaphuzitsa amayamba kuchita mawu osakhala akuva chabe.

## **7. KUYANG'ANIRA**

Akuphuzira atabwerera kuulendo wawo, Yesu anawunikira ntchito yawo (Luka 9:10). Yesu anawayang'anira nthawi yose imene anali akuphuzira. Sanasiyidwe okha nthawi imene anali kukumana ndi mavuto. Amawatsutsa, kutsutsa komaso ndi kulimbikitsa akuphuzira ake. Simungaganize kuti ntchito itheka chifukwa chakuti wa ntchito mwamuwonetsa machitidwe ake ndipo inu mulu ndichiyembekezo chimene chikulakulabe. Mukuyenera kuyang'anira akuphuzira akamakumana ndi Mavuto ndi zokhumudwitsa, mukuyenera kuwaphuzitsa zochita Mavuto akabwera.

Kuyang'anira kumatchulidwaso kuti “Kutsatira” Paulo anatsatira akuphuzira ake.

**Atakhala kumeneko nthawi, anacoka, napita pa dziko la Galatiya ndi Frugiya m'dziko m'dziko, nakhazikitsaakuphuzira onse. (Machitidwe 18:23)**

**nalimbikitsa mitima ya akuphuzira, nadandauliraiwo kuti akhalebe m'cikhulupiriro, ndi kuti tiyenera kulowa m'ufumu wa Mulungu ndi zisautso zambiri.**

**(Machitidwe 14:22)**

## **8. KULENGEZA:**

Pomalizira pa kukhala ophuzira Yesu analamulira iwo kuti akaphuzitseso ena. Anapatsidwa ntchito yakuti achulukane padziko lapasi.

### **CHITSAZO CHA AEFESO**

Werengani Machitidwe 19:1-20, chaputalachi chikufotokoza za utumiki wa Paulo mu mzinda otchedwa, Aefeso. Paulo atafika ku Aefeso anafufuza okhulupirira a kumeneko. Amuna ndi akazi amenewa anali atalandira kale uthenga wabwino ndipo anali omutsatira kaye Yesu (Machitidwe 19:1) koma amafunika maphuziro ena kuti atumikire bwino munzinda wawo.

Paulo anawaphuzitsa kudzera kuzimene amakumana nazo. Choyambirira chimene anapanga ndi kulola kuti akumane ndi zinthu zosiyanasiyana za uzimu zimene zinali ubatizo wa uzimu. (Machitidwe 19:2-8). Paulo anawaphuzitsa poonetsera. Anawona zodabwitsa zazikulu zikuchitika m'dzina la ambuye (Maachitidwe 19:11-12). Amene anali otsatira enieni a Yesu anawonekera ndipo analapa Machitidwe 19:13-17). Otembenuka anabwera kwa Yesu Khristu (Machitidwe 19:17-20).

Otsutsa Uthenga Wabwino atadzuka kuchokera pakati pa atsogoreli, Paulo anayambitsa malo ophuzitsira ku Aefeso:

**Koma pamene ena anaumitsa mtima ndi kusamvera, nanenera zoipa Njirayo pamaso pa anthu, anawacokera, napatutsa akuphunzira, nafotokozerana masiku onse m'sukulu ya Turano. (Machitidwe 19:9)**

Malo amene Paulo anakhazikitsa akupereka chitsazo cha maphuziro okwana zaka ziwiri awophuzira. Cholinga cha maphuzirowa kunali kuchulukitsa nambala ya ophuzira ofalitsa uthenga wabwino.

**Ndipo anacita comweco zaka ziwiri; kotero kuti onse akukhala m'Asiya anamva mau a Ambuye, Ayuda ndi Ahelene. (Machitidwe 19:10)**

Malo okhazikitsidwawo panalibe magawano chifukwa cha chikhalidwe. Ophuzira amatumikira pakati a Yuda komaso Amitundu (Mitundu ina imene sanali Yuda). Sukuluyi inalibe malire. Ophuzira samatumikira mum'zinda wawo okha wa Aifeso, anafikiraso dera loso la Asia. Chitsanzo cha Aefeso ndi chabwino kumbali ya maphuziro chifukwa maphuzirowo anaphunzitsa ena.

**Cotero mau a Ambuye anacuruka mwamphamvu nalakika. (Machitidwe 19:20)**

Sukulu ya kwa Aefeso inawaphuzitsa ndi kuwakozekeza ntchito ya utumiki. Cholinga kunali kufalitsa uthenga malo ose (Dera la Asia) komanso Ayuda ndi Amitundu. Otembenuka mtima atsopano anaphuzitsidwa mosadukizadukiza.

### **KUKHAZIKITSA MALO OPHUZITSIRA**

Malo ophunzitsira ndiwofunika monga m'mene zinaliri kwa Aefeso. Otembenuka mtima akamachuluka, ndikofunika kuti aphuzitsidwe ngati ophuzira, ndi atsogoleri amene akhale ndi udindo ofalitsa uthenga wabwino ku dziko lonse. Malo ophuzitsira sanalowa m'malo a mpingo. Okhulupirira anapitirizabe kukumana musunagoge, amene anali malo amodzi amene mpingo oyamba umakumana. Okhulupirira anapitilizabe kukumana m'ma tchalitchi a m'makomo awo.



Sukulu ya kwa Aifeso imapitiriza ntchito ya mpingo osati kulowa m'malo ake. Cholinga cha ndongosololi sikkuti ilowe m'malo mwa magulu amene akufalitsa uthenga wabwino.

Ngati muli osangalatsidwa kukhazikitsa malo ophuzitsira ofana ndi Aefeso, malangaizo popanga izi anaperekedwa mu m'maphuziro a Harvestime International Institute otchulidwa "Njira Zochulukitsira". Zimafotokoza kapezedwe ka malo, kuwona zofunika, kapezedwe ka ophunzira, kapezedwe kaphunzitsi komaso maphunziro, kufalitsa ndi kaphunzitsidwe.

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani mau a pantima.

---

---

2. Chifukwa chani kuphuzitsa ena ndi udindo ofunika?

---

---

3. Kodi cholinga chophezitsa atsogoleri ndi otsatira ndi chani?

---

---

4. Nenani ndondomeko zisanu ndi zinayi zosankhira muphuziro la Yesu ndi ophuzira ake.

---

---

5. Nenani ndondomeko zisanu ndu zitatu zophuzitsira m'phuziro la Yesu ndi ophuzira ake.

---

---

---

---

---

6. Tapatsidwa chitsazo chiti cha maphuziro m'chipangano chatsopano.

(Mayankho amafuso osewa apatsidwa kumapeto kwa bukhuli)

## KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

1. Ophuzira amakhala atsogoleri:

-Joshua, amene anali ophuzira wa Mose, anakhala ntsogoleri: Numeri 27:18; Detronomy 3:28.

-Elisa amene anali ophuzira wa Eliya, anakhala mtsogoleri: 2 Mafumu 2.

2. Yesu anaphuzitsa omutsatira omwe anakhala atsogoleri. Kawirikawiri Yesu anaitana kuti amutsatire. Mawu akuti “kutsatira” unditsanze, “bwera pambuyo panga” anagwiritsidwa ntchito makumi awiri. Ananenedwa ndi:

-Simoni ndi Adreya: Mateyu 4:19; Marko 1:17

-Yakobo ndi Yohane: Mateyu 4:21; Marko 1:20

-Mateyu: Mateyu 9:9; Marko 2:14; Luka 5:27

-Filipo; Yohane 1:43

-Petro: Yohane 21:19, 22

-Mwini chuma: Mateyu 19:21; Marko 10:21; Luka 18:22

-Ophuzira wina: Mateyu 8:22

-Mwamuna wina: Mateyu 16:24; Marko 8:34; Luka 9:23;

Yohane 12:26

3. Werengani za kuphuzitsa atsogoleri mthawi ya chipangano chakale (1 Samuel 19:18-20 ndi 2 Mafumu 2:1; 4:38; 6:1.

4. M’musimu muli mavuto asanu amene muyenera kuwagonjetsa mukamaphuzitsa okutsatirani ndi atsogoleri:

1. Kuwopa munthu.

2. Ulesi.

3. Kukana kusintha.

4. Kufuna kupanga zinthu zambiri nthawi imodzi.

5. Umbuli (Anthu akuyenera kuphuzitsidwa kuti akhoza kulalikira bwanji uthenga ndi kuchita ntchito ina yake mutumiki).

5 Maphunziro a ku Harvest International Institute atha kuthandiza pophuzitsa ophuzira ndi atsogoleri. Lembani lelo ndandanda wokeyana wa maphuzira amene amaparekedwa.

1. Milozo imene mungayigwiritse ntchito pophunzitsa ndi iyi:

**Khalani okozeka.**

Mphunzitsi wina aliyese amayenera kudziwa bwino zimene at aphuzitse, amayenera kukozeke popemphera. Akuyenera kukhala ndi malo okhazikika otengangako zipangizo kukozeke nthawi yamaphunziro.

Mphunzitsi aliyese akuyenera kukhala ndi cholinga pa phuziro lirirose. Ngati mukugwiritsa ntchito zipangizo zochokera ku Harvesttime Internatioanl Institute, zolinga zimaperekedwa poyamba pa chaputala.

Khalani otsimikizika kuti zipinda ziri bwino.

**Kusunga nthawi**

Yambani komaso malizani maphuziro m'thawi yake. (Pokhapokhapo Mzimu woyera akukutsogolerani)

**Pepherani:**

Yambani ndipo malizani ndi pephero.

Nenani mwachidule komaso mangirirani

Yambani maphunziro anu ponena mwachidule zimene munaphunzira. Malizani maphunziro anu pomangirira zimene mwaphunzira.

Gwiritsani ntchito njira zosiyanasiyana zophuzitsira:

Maphuziro a Harvest International Institute otchulidwa “Luso la Kaphuzitsidwe” limakuphuzitsani kuphuzitsa pogwiritsa ntchito njira za Yesu Khristu.

**Vetserani Mzimu Woyera:**

Kuvetsera Mzimu woyera ndikofunika kwambiri kusiyana ndi kutsatira zimene munakozeke.

**Wonetserani**

Wonetsani zimene zikuphuzitsidwa, chitsazo, ngati mukuphuzitsa za machiritso, pepherararani amene akudwala. Mukamaphuzitsa za ubatizo wa mzimu woyera, tsogolerani anthu kuti akumane nazo.

**Kozani Zochitika Zopereka Maphuziro:**

Perekani ntchito yoti ana amalize nthawi ya maphuziro. Perekani mwayi oyesera zimene iwakuphunzira ku tchalitchi kapena dera.

2. Awa ndi mafuso ena amene mukuyenera kuganizira:

-Kodi chitsazo chanu m'makhalidwe ndi chotsogolera ena kwa Mulungu? Tchulani njira ziwiri zimene munganene.

-Kodi ena ali ndi mwayi okhala nanu kuti awone chitsazo chanu? Kapena mumakhala patali ndi anthu? Tchulani njira zitatu za m'mene mumamasukira kwa anthu ena.

-Kodi mukukhulupirira kuti anthu akuyenera kutsatira inu ngati chitsanzo? Chifukwa chani ziri choncho nanga chifukwa chani ayi?

-Kodi simukutsatira mfundo za Mulungu pamene mukutsogolera? Mwanjira yanji? Nanga mungakonze motani?

-Mungatchule munthu amene mwamuphuzitsa kuti akuthandizeni?

## CHAPUTALA 11

### KUKUMANA NDI KULEPHERA

#### ZOLINGA

Mukamaliza chino muzikwanitsa kuchita izi:

1. Kulemba Vesi Lotsogolera.
2. Kupeza zifukwa zitatu zolepheretsa.
3. Kupeza atsogoleri a Baibulo amene angagonjetsa kulephera.
4. Kupeza atsogoleri a Baibulo amene analepherapo
5. Kupeza ndondomeko za M'baibulo zosintha kulephera kukhala chipambano.

#### VESI LOTSOGOLERA

**Potero udzadziwa kuti nzeru iri yotero m'moyo wako; Ngati waipeza padzakhala mphotho, Ndipo ciyembekezo cako sicidzalephereka. (Miyambo 24:16)**

#### MAU OYAMBA

Phuziro iri ndi limodzi mwa maphuziro ofunika kwambiri mubukuli “Biblical Management Principles” Chifukwa limathandiza kuthana ndi kulephera. Mulungu ali nd ndondomeko zamgwiro koma amagwiritsa ntchito anthu azinthu zofoka kukwaniritsa ndondomeko zake. Chifukwa chakuti sindinu angwiro mukuyenera kuvetsetsa zifukwa za kulephera ndikudziwa choyenera kuchita mukalephera.

Likamatha phuziroli muphuzira zoyambitsa kulephera. Muphuzira zitsazo za atsogoleri amene moyo wawo unathera mkulephera komaso amene anasanduliza kulephera kukhala chipambano. Mupatsidwaso mfundo za Baibulo zothana ndi kupanga kulephera kukhala chipambano.

#### CHIMAYAMBITSA KULEPHERA NDI CHANI?

Pali zifukwa zitatu zakulepheretsa;

##### ➤ KUWONONGEKA KWA UBALE

Atsogoleri ambiri amalephera chifukwa chosoweka ubale wabwino ndi Mulungu. Atha kukhala kuti asanayike maziko awo abwino awuzimu monga zinanenedwa pa Ahebeli 6:1-3. Akafuna kumanga ntchito ya Mulungu ndimaziko opanda mphavu imagwa.

Atsogoleri ena amatanganidwa ndi ntchito ya Mulungu kuyiwala mapemphero, kuwerenga mawu, kusala ndi kufunafuna chifuniro cha Mulungu. Ena amataya Chikondi chawo ndi

Mulungu. M' malo motsogoza Mulungu ndi ufumu wake chisamaliro cha chuma, kupanga ndalama, kukondweretsa anthu zimayamba kutenga malo muntima mwawo.

Mfumu Uziya ndi chitsazo cha mfumu imene inalephera chifukwa chosoweka ubale wabwino ndi Mulungu. Mfumu uziya sanayambe bwino. Anafuna ambuye ( 2 Mbiri 26:6-8). Anachita bwino pa nkhondo ya Aisraeli ndi adani awo (2 Mbiri 26:6-8). Koma mfumu Uziya atadziwika ndi kudzikweza anayamba kuchita mwa chinyengo, anali osakhulupirika kwa Mulungu, ndipo sanafuneso ambuye (2 Mbiri 26:16)

Kukhala mtsogoleri, uyenera kukhala ndi ubale wabwino ndi Mulungu. Atsogoleri ambiri amene analephera anazindikira kuti vuto linayambidwa ndi kulephereka kwa ubale wabwino nd Mulungu.

#### ➤ **KULEPHERA POCHITA**

“Kulephera pochita” zikutanthawuza kulephera kochitika chifukwa cha ntchitidwe wauchimo. Izi zikutanthawuza zochitika zoyipa, mawu, maonedwe, kapena zolinga. Machitidwe awa amabweretsa kulephera.

#### ➤ **KULEPHERA POSACHITA**

“Kulephera posachita” zitanthawuza kulephera kochitika chifukwa chakuti zinthu zina sizinachitike. Ukachimwa posachita zinthu umalephera kuchita zoyenera. Baibulo limati:

**Mkazi anayankha nati kwa iye, Ndiribe mwamuna. Yesu ananena naye, Wanena bwino, kuti mwamuna ndiribe; (Yohane 4:17)**

Machimo ochitika chifukwa chosachita ndi zinthu zimene mawu a Mulungu amati mukuyenera kuchita koma mumalephera kuchita. Yesu anadzudzula atsogoleri achipembedzo a nthawi yake ndipo anati;

**Tsoka inu, alembi ndi Afarisi, onyenga! cifukwa mupereka limodzi la magawo khumi la timbeu tonunkhira, ndi katsabola, ndi la citowe, nimusiya zolemera za cilamulo, ndizo kuweruza kolungama, ndi kucitira cifundo, ndi cikhulupiriro; koma zijazo munayenera kuzicita, osasiya izi zomwe. (Mateyu 23:23)**

#### **ATSOGOLERI AMENE ANAPAMBANA PA ZOLEPHERA ZAWO**

Baibulo liri ndi zitsazo za atsogoleri amene nthawi ina yake analephera ngati atsogoleri; Abraham: Ananama ponena kuti Sarah, nkazi wake pochita mantha kuti aphedwa ndipo nkazi wake anatengedwa. Komabe amadziwika kuti anali munthu wachikhulupiriro.

Mose: Mwakwiyo anamenya mwala ndipo madzi anatuluka m'malo molakhula ndi mwala m'mene Yesu ananenera. Komabe Baibulo limati sipanawukanso ntsogoleri wankulu ofanana ndi Mose.

Mfumu Davide: Pofuna kubisa tchimo Anapha munthu atachita chigololo ndi nkazi wake koma Baibulo limati inali mfumu ya mphavu "Munthu okonedwa ndi Mulungu".

Yona: Mulungu atamuitana kukalalikira ku Ninive anapita mbali ina, kenako anapita kulalikira ndipo chitsitsimutso chachikulu m'biri ya dziko chinachitika.

Joshua: Anali mtsogoleri wamphavu wa Asilikali amene anakhala mtsogoleri Mose atafa. Imodzi mwa ntchito imene anapatsidwa ndi kutsogolera ana a Israeli kukalandira dziko lamalonjezano. Koma nthawi ina yake Yoswa anakhumidwa pa Mulingo oti anafuna kukhalabe mbali ina ya nyanja ya Yolodani ku chipululu. Nthawi ina ananamizidwa ndi Agebonites. Komabe anapita ndi kulandira dziko la Malonjazo.

M'neneri Eliyah: Mfumukazi yoipa Yezebeli anatumiza nthenga kwa m'neneri Eliyah kumudziwitsa kuti amafuna kuti amuphe. Eliyah;

**Koma iye mwini analowa m'cipululu ulendo wa tsiku limodzi, nakakhala pansi patsinde pa mtengo watsanya, napempha kuti afe; nati, Kwafikira, cotsani tsopano moyo wanga, Yehova; popeza sindiri wokoma woposa makolo anga. (1 Mafumu 19:4)**

Apa panali munthu wankulu wa Mulungu amene anachiritsa odwala, anadzutsa akufa, anakhala ndi mphavu pa chilengedwe m'dzina la ambuye. Tsopano anabisala, ndi mantha ndipo anapempha kuti afe. Koma Eliyah anawonetsera mphavu ya Mulungu pa maso pa ntundu wose wa Israeli pa Phiri la Kalimeri.

Petulo: Munthu uyu anakana Yesu koma anakhala ntsogoleri wankulu mu mpingo wakale.

Ntumwi Paulo: Mtumwi Paulo analepheraposo. Analembapo kuti chifukwa cha zimene amakumana nazo ku Asia "Anazuzika modutsa mulingo" nafuna imfa. (2 Akorinto 1:8).

Anafotokoza nthawi zimene anavutika, kunzuzika, kupsinjika chifukwa cha Khristu. Ananena kuti anali ndi mantha komaso Mavuto (2 Akorinto 7:5:6). Koma mtumwi ananena kuti analalikira Uthenga Wabwino pakati pa amitundu, kudzutsa mipingo yambiri ndi atsogoleri padziko lonse lapansi.

**ATSOGOLERI AMENE ANALEPHERA CHIFUKWA CHA ZOFOOKA ZAWO**

Baibulo lili ndi zitsanzo za atsogoleri amene analephera chifukwa cha zofooka zawo.



Samison: Anali Oweruza wa ma Israeli ndipo anali wamphamvu zimene anapatsidwa ndi Mulungu. Anayamba kulanditsa Aisraeli kwa adani awo Afilisiti. Chifukwa cha mkazi wachikunja, Samson anatengedwa ukapolo ndipo anafa mu ukapolo.

Uzziah: Anakhala mfumu ali ndi zaka khumi, zisani ndi chimodzi. Amapambana pokhapokhapo akamapanga zoyenera pamaso pa Ambuye. Uziya anachimwa polowa munkachisi ndi kuchita ntchito imene ansembe amaloledwa kuchita. Mulungu anamukantha ndi khate ndipo anafa.

Saulo: Saulo anali mfumu ya Israeli, yolemekezedwa ndi anthu komaso amene mzimu wa Mulungu unalephereka. Chifukwa cha Kusavera, Saulo anakanidwa ndi Mulungu ndipo munthu wina anasankhidwa kuti amalize ntchito. Moyo wa Saulo unamalizika ndi kulephera, manyazi ndi kudzipha.

Eli: Anali wa nsembe wamphavu munyumba ya ambuye. Chifukwa cha kusavera, Eli ndi ana ache anafa mwa manyazi.

Yudasi: Yudasi anali ophuzira wa Yesu muwutumiki wake padziko lapasi. Anawonaso zodabwitsa zazikulu za Yesu ndi zimphuzitso zake. Anapereka Yesu ndipo kenako anadziza.

### **CHIMASIYANITSA NDI CHANI**

Ena mwa atsogoleri anachitaso bwino atalephera pamene ena sanasinthe. Moyo wawo unalephera. Chimene chinapangitsa kusiyana ndi chani?

Kuyankha fuso ili tiwone zambiri zokhudzana ndi atsogoleri awiri a dziko la Israeli amene ndi Davide ndi Sauli. Choyamba werengani nkhani yakulephera kwa Davide pa 2 Samuel 11-12 kenako werengani nkhani ya kulephera kwa Sauli pa 1 Samueli 15.

Nkuganiza kwathu, kulephera kwa Davide kunali kwakukuru kusiyana ndi Sauli. Sauli anangobweretsa zinthu kuchokera ku nkondo monga, ng'ombe, zimene Mulungu anamuletsa. Davide anachita chigololo ndi nkhazi wa mwini. Zitadziwika kuti ali ndi pakati, anapha mwamuna wake kuti abise tchimo lake. Sauli anakanidwa ndi Mulungu ngati mfumu pamene Davide anakhalabe mfumu natchulidwa "A man after God's heart".

Chifukwa chani ena amalephera pamene ena amapambana? Yankho ndi la mawu amodzi: kulapa. M'neneri Samueli atamutsutsa Sauli za tchimo lake, Sauli anati....

**Ndipo Sauli anati kwa Samueli, Ndinachimwa; pakuti ndinalumpha lamulo la Yehova, ndi mau anu omwe; cifukwa ndinaopa anthuwo, ndi kumvera mau ao. Cifukwa cace tsono, mukhululukire cimo langa, nimubwerere pamodzi ndi ine, kuti ndikalambire Yehova. Ndipo Samueli ananena ndi Sauli, Ine sindibwerera nanu;**

**pakuti munakaniza mau a Yehova, ndipo Yehova anakaniza inu, kuti simudzakhalanso mfumu ya Israyeli. Ndipo pakupotoloka Samueli kuti acoke, iye anagwira cilezi ca mwinjiro wace, ndipo cinang'ambika. Ndipo Samueli ananena naye, Yehova anang'amba ufumu wa Israyeli lero kuucotsa kwa inu, naupatsa kwa mnansi wanu wina wabwino woposa inu. Ndiponso Wamphamvu wa Israyeli sanama kapena kulapa; popeza iye sali munthu kuti akalapa. Pomwepo iye anati, Ndinacimwa, koma mundicitire ulemu tsopano pamaso pa akuru a anthu anga, ndi pamaso pa Israyeli, nimubwerere pamodzi ndi ine, kuti ndikalambire Yehova Mulungu wanu. (1 Samueli 15:24-30)**

Sauli atachimwa anavomera. Anapepesa chifukwa chakuti anagwidwa chokha. Kupepesa chifukwa cha tchimo sizokwanira. Kumva chisoni kuyenera kutsogolera ku kulapa.

**Ndipo Yehova anakutumani ulendo, kuti, Muka, nuononge konse konse Aamaleki akucita zoipawo, nuponyane nao kufikira utawatha. (1 Samueli 15:18)**

Ufumu unalandidwa ndi Sauli ndikupatsidwa kwa Davide.

M'neneri Natani atamutsutsa za tchimo, Davide anazindikira;

**Atero Yehova, Taona ndidzakuutsira zoipa, zobadwa m'nyumba yako ya iwe wekha; ndipo ndidzacotsa akazi ako pamaso pako ndi kuwapatsa mnansi wako, amene adzagona ndi akazi ako dzuwa liri denene. Ndipo Davide anati kwa Natani, Ndinacimwira Yehova. Natani nati kwa Davide, Ndiponso Yehova wacotsa chimo lanu, simudzafa. (2 Samueli 12:13)**

Sanakwiyire ena ngati Bethsheba. Modzichepetsa anavomera kulakwa kwake nalapa pamaso pa Mulungu. Pemphero la Davide lakulapa limapezeka pa Salimo 51. Werengani Salimo lonse.

Davide anazindikira tchimo lake ndipo anapempha chikhululukiro kwa Mulungu:

**Cifukwa ndazindikira macimo anga; Ndipo coipa canga ciri pamaso panga cikhali: Pa Inu, Inu nokha, ndinacimwa, Ndipo ndinacita coipaco pamaso panu: Kuti mukhale wolungama pakulankhula Inu, Mukhalenso woyera pa kuweruza kwanu. Mundilengere mtima woyera, Mulungu; Mukonze mzimu wokhazikika m'kati mwanga. (Salimo 51:3, 4,10)**

Davide atalephera analapa ndikusintha mayendedwe ake pamene Sauli sanatero. Anapatukadi pa chifuniro cha Mulungu ndipo moyo wake unakhala olephera, kugonja, ndi kudzipha.

## **MUKALEPHERA**

M'baibulo muli ndondomeko zimene mukatsatira kulephera kutha kusandulika chipambano. Tiphuzira ndondomeko zimenezi potsatira chitsazo cha Yona. Werengani machaputala 4 a Buku la Yona. Werenani buku la Yona (ma chaputala anayi) musanapitirire ndi phunziroli. Yona anatumidwa ndi ambuye kukalalikira kutembenuka mtima ku Ninive dziko lochimwa. M'malo momverá Mau a Mulungu anapita m'mbali ina. Yona anachita izi kuti akonze kulephera kwake. Izi ndi ndondomeko zoyenera pamene mwalephera:

### **KUWULULA**

Mukalephera wululani chimene chapangitsa. Khalani otsimikizika ntima kuti Mulungu ali ndi njira zambiri zokudziwitsani pamene mwalephera. Namondwe pa nyanja anawulula kuti Yona sanachite chifunuro cha Mulungu. Yona anavomereza kulakwa kwake atalandira vumbulutso iri (Yona 1:12). Pokhapokha mutazindikira tchimo mumakhalabe olephera:

**Wobisa macimo ace sadzaona mwai; Koma wakuwabvomereza, nawasiya adzacidwa cifundo. (Miyambo 28:13)**

**iyе sindiye kuunikaku, koma anatumidwa kukacita umboni wa kuunikaku. (1 Yohane 1:8)**

Musalole chifukwa chirichose kukulepheretsani kuvomereza kulephera kwanu. Izi ndi zina mwa izo;

- “Anthu ataya chikhulupiro mwa ine”
- “Ndikavomereza kulephera zitanthauza kuti ndikuvomereza kulakwa.”
- “Ndinalephera kale. Ndingosiya.”
- “Ndachedwa kale.”
- “Ndine chitsazo choipa, ndiye ndingosiya.”
- “Ndiri kutali ndi chifuniro cha Mulungu kuti zinthu zikozeke.”

Sizoyenera kuwulula kwa ena kulephera kwanu pokhapokha ngati zikukhudzaso moyo wa ena ndipo Mukuyenera kupempha chikhululukiro. Koma mukuyenera kuvomereza kulephera kwainu ndi Mulungu. Iyi ndi imodzi mwa mfundo yothandiza yopangira kulephera kukhala chipambano: Tchimo likuyenera kuwululidwa. Mukuyenera kulizindikira.

### **KULAPA**

Choyambitsa tchimo chikadziwika mukuyenera kulapa:

**Uku ndiko kuunika kweni kweni, kumene kuunikira anthu onse akulowa m'dziko lapansi. (Yohane 1:9)**

Pephero la kulapa la Yona limapezeka mu Yona Chaputala 2. Yona anazindikira tchimo pamaso pa Mulungu, analapa, ndikupempha chikhulukiro. Mukalephera, bwerani pamaso pa Mulungu mwa kulapa. Pemphani Mulungu akukhulukireni pa kulephera kwanu. Mukuyenera kudzikhulukiranso.

### **KUBWERERA**

Kudzera ku pemphero, malembo a Mulungu ndi chitsogozo cha Mzimu woyera Mulungu adzakuwonetsani pamene kulephera kwanu kunayambikira. Mukuyenera kufika pamenepo ndikusintha mayendedwe anu.

Nowa anazindikira kuti kulephera kwake kunayambika pamene amapita mbali ina osakhala ku Ninive. Anayenera kubwerera nasintha mayendedwe ake. Kulapa kwenikweni kumakhudzana ndi kusintha machitidwe azinthu. Mukafika porephera bwererani pamene munachimwa ndikusintha mayendedwe anu. Izi zimachitika po.....

### **BWEZERETSA**

Yona atazindikira kulephera kwake popita mbali yotsitsana ndi Mzina wa Ninive anabwerera. Anapita moyandikira Ninive. Anakoza kulephera kwake (Yona 3:3). Anachita chilichose kuti akoze zinthu zake. Izi ndiye kubwezeretsa.

Nthawi zina simungachite chirichose kukoza kupatula kungo lapa. Chitsazo cha Davide, tinakambirana kuti sanachite chirichose kupatual kulapa tchimo lokhudzana ndi Bethsheba. Izi zinali zitachitika kale. Chigololo chinali chitachitika kale ndipo mwamuna wake anali atafa kale. Panalibe chirichose akanacita kupatula kulapa.

Koma nthawi imene mutalephera mukhoza kukoza zinthu ndibwino kutero. Mutha kupepesa munthu wina. Mutha kubweza zimene munaba kapena kuvomereza kunanama. Izi ndi zitsazo za kubwezeretsa.

Mukuyeneraso kukhala ndi nthawi yodzibwezeretsa ndi kumangaso moyo wanu wa uzimu mutalephera. Mutha kusiya kaye ntchito za utumiki. Mukuyenera kukhala ndi nthawi ndi Mulungu.

Njira zina zobwezeretsa mpavu zauzimu ndi izi:

- Werengani mawu a Mulungu.
- Khalani ndi nthawi ya kusala kudya ndi kupemphera.

- Onani choyambitsa chenicheni cha kulephera kwawo (zoperekedwa m’phunziroli) mudzakhala nako kuthekera kopewa kulephera kutsogolo. Pemphani Mulungu awonetse ndi kukuthandizani kukoza vuto lina lililose m’oyo wanu.
- Unikani m’mene nkondo ya uzimu imakhalikira kukuthandizani kuti mudzapambana nthawi ina. Onani phunziro ku Harvest International Institute mutu wake (Ndondomeko za Uzimu). Likupezeka mu buku lotchedwa “Nkhondo ya Uzimu”.
- Pumulitsani thupi lanu. Munthu ali ndi magawo atatu monga thupi, mzimu ndi mtima. Thupi lanu likakhala lotopa satana atha kutengerapo mpata kuwononga moyo ndi mzimu wanu nakupangani kuti mulephere.

### **NJIRA YA KUPAMBANA**

Mukachita ndondomeko zosezi, mukuyenera kusiya kulephera kwau ndi kuyang’ana za chipambano. Yona anayiwala zakulephera. Ambuye anamuyankhula kachiwiri “Duka numuke ku Ninive” (Yona 3:1-2). Nthawi iyi anavera mwachangu. Ku Ninive Yona anabweretsa chitsitsimutso chachikulu m’biri ya Dziko. Mzinda onse unalapa. Potsatira ndondomeko izi, kuwonetsa, kulapa, kubwerera, kubwezeretsa ndi kusintha kulephera kukhala chipambano. Bible liri ndi nkhani zambiri za anthu ngani Yona. Anthu amene analephera koma anavomereza kulephera kwawo ndipo anapempha chikhululukiro kwa Mulungu. Atapanga izi, Mulungu sanalephere kuwakhulukira ndikupereka chitsogozo chabwino. Mulungu atha kupanga chimodzimodzi ndi inu sakuyang’ana zolephera zanu zakale. Akuyang’ana inu m’mene muliri lero. Akuyang’ana mwamuna kapena nkazi amene mukhoza kukhala mutayenda mokhulupirika ndi Iye.

### **KUPHUNZIRA KUCHOKERA KU ZOLAKWITSA**

Paulo analemba:

**Pakuti sitifuna abale, kuti mukhale osadziwa za cisautso cathu tinakomana naco m’Asiya, kuti tinathodwa kwakukuru, koposa m’phamvu yathu, kotero kuti tinada nkhwana ngakhale za moyo wathu; koma tokha tinakhala naco citsutso ca imfa mwa ife tokha, kuti tisalimbike pa ife tokha, koma pa Mulungu wakuukitsa akufa; amene anatilanditsa mu imfa ya ikuru yotere, nadzalanditsa; (2 Akorinto 1:8-10)**

Paulo anafotokoza kuti mavuto a (ku Asia) anamuphuzitsa zambiri. “Sitikuyenera kudzidzidalira ife eni koma Mulungu”. Iri ndi phuziro lalikulu loyenera kuphuzira ku zolakwitsa zathu.

Sungadalire iwe wekha, mphavu yako, kupambana kwako ngati mtsogoleri kumatsimikizidwa

mwa Yesu Khristu. Paulo amayang'ana modutsa dzikko lapasi ndikuwona ubwino wauzimu pa mavuto, mayesero komaso zolepheretsa:

**Cifukwa cace sitifoka; koma ungakhale umunthu wathu wakunja ubvunda, wa m'kati mwathu ukonzedwa kwatsopano tsiku ndi tsiku. Pakuti cisautso cathu copepuka ca kanthawi citicitira ife kulemera koposa kwakukuru ndi kosatha kwa ulemerero; popeza sitipenyenera zinthu zooneka, koma zinthu zosaoneka; pakuti zinthu zooneka ziri za nthawi, koma zinthu zosaoneka ziri zosatha. (2 Akorinto 4: 16-18)**

Paulo anaphuzira kuti ngakhale munthu wakunja akuwonongeka, munthu wankati amakozedwanso. M'malo mosiya, Paulo anaphuzira kuchokera kukulephera ndikufika pa kupambana. Pa 2 Akolingo 1:10 ananena kuti Mulungu:

“Anapulumsa” (Kale)  
“Amapulumutsa” (Tsopano)  
“Adzapulumutsa” (Mtsogolo)

...kumavuto, mayesero, masawutso, komaso kulephera. Anati tiri

Osautsika	KOMA OSAPSINJIKA
Osinkhasinkha	KOMA OSAKHALA KAKASI
Olondoleka	KOMA OSATAYIKA
Ogwetsedwa	KOMA OSAWONONGEKA

Ngankhale anasinkhasinkha, kusautsidwa, kulondoleka, ndi kugwetsedwa, Paulo m'masiku ake onse ananenabe kuti:

**Ndalimbana nako kulimbana kwabwino, ndatsiriza njirayo, ndasunga cikhulupiriro: (Timoteo 4:7)**

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera.

---

---

2. Perekani zitsazo zitatu za atsogoleri amene anagonjetsa mavuto awo.

---

---

---

3. Perekani zitsazo zitatu kuchokera Mbaivulo za anthu amene analephera.

---

---

---

4. Perekani ndondomeko zosinthira kulephera kukhala chipambano.

---

---

5. Ndizinthu ziti zimene zimabweretsa kulephera

R\_\_\_\_\_ R\_\_\_\_\_

R\_\_\_\_\_ R\_\_\_\_\_

6. Kodi zinthu zitatu zimene zimabweretsa kulephera ndi ziti?

---

---

---

(Mayankho a mafuso onsewa ali kumapeto kwa buku lino)

## KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

1. Yesu anayankhula za nyamata pa Luka 15:11-31 amene anasiya atate wake napita kudzikolo lachilendo. Werengani nkhanayi mozamala, makamaka mbali ya nkhanu imene ikunena zakubweraso kwa nyamatayi kunyumba ya atate ake. Muwona kuti pokoza kulephera kwake anatsatiraso mfundo zimene takambirana kale m'chaputalachi.
2. Werengani zitsazo zotsatirazi za atsogoleri m'baibulo amene analepherapo nthawi ina m'moyo wina. Ndi oti amene anakoza kulephera kwake? Zotsatira zake ndi ziti? Mukhoza kupereka zitsazo zina kundandawu kuchokera kukuwerenga mawu a Mulungu.

-Abrahamu	Genesisi 20-44
-Mose	Bukhu la Eksodo; Machitidwe 7:44
-Aroni:	Eksodo 32
-Balaam:	Numeli 22
-Uzziah:	2 Mbiri 26
-Samson:	Judges 13:16
-Davide:	2 Samueli 8:15
-Saulo:	1 Samueli 8:15
-Yona:	Buku la Yona
-Petulo:	Mateyu, Marko, Luka, Yohane, Machitidwe
-Yohane Marko:	Machitidwe 12: 12, 25: 15:39; 2 Tim. 4:11
-Demas:	2 Timoteo 4:9

3. M'phuziroli munaphuzira kuti pali zinthu zitatu zobweretsa kulephera zimene ndi izi;
  - Kulephera kwa ubale wabwino ndi Mulungu (maziko auzimu, kusoweka kwa pemphero, komanso kusawerenga Mau).
  - Kuchita tchimo (kusamvera Mau a Mulungu)
  - Kusachita zonena za Mulungu (Kusachita zimene zikuyenera kuchitika).

Uwu ndi m'ndandanda wa zotsatira za kulephera. Koma mungakhale ndi zotsatira zina zimene mungaziwonjeze pa m'ndandawu?

- Kukhumudwa
- Kutengera (kutengera utumiki wa ena)
- Kusoweka masomphenya



- Kusoweka kwa maphunziro
- Kusafuna kulipira dipo
- Kusakhulupirika
- Kusoweka zinthu zofunika kwambiri kwa iwo
- Kusoweka mwambo
- Chuma, kusagwiritsa ntchito bwino chuma, chikondi cha pa ndalama, Kumana
- Kudzikonda
- Nsanje
- Kulakwira otsatira
- Kusalumikizana bwino ndi otsatira
- Mantha apa anthu ndi kulemekeza anthu
- Kutchuka
- Kuchita zinthu modukizadukuza
- Kusachita kauniuni wa iwe mwini
- Kudziyerekeza ndi anthu ena
- Kusasunga mwambo
- Zokhumba
- Kusapereka ntchito kwa ena (kufuna kuchita chirichose)
- Kumva ndi kugonjera kwa anthu osati Mulungu; kutengeka ndi maganizo ambiri
- Kusakhulupirira
- Kusafikira pa zimene zimafunika kuti munthu akhale mtsogoleri wauzimu
- Kusoweka maitanidwe eni eni autsogoleri
- Kusoweka chidziwitso komanso kusagwiritsa bwino ntchito mfundo za nkondo ya wuzimu
- Kusoweka chidziwitso komanso kagwiritsidwe ntchito ka mfundo za M'baibulo zokhudzana ndi kupambana.
- Kulephera kumva mawu a Mulungu ndi kumva chifuniro chake ndipo izi zimapangitsa zisankho zolakwika.
- Kusoweka mphamvu zauzimu
- Kusakozerera bwino
- Kusagwiritsa ntchito bwino zinthu zimene Mulungu anapereka

- Kusabala zipatso zauzimu
  - Muzu wa nkwiyo
  - Ulesi
  - Chikondi cha padziko
  - Kusoweka kwa kudzodza
4. Kunyada ndi chifukwa chimodzi mwa zifukwa zambiri zobweretsa kulephera. Nchifukwa chimene chinapangitsa tchimo loyamba. Satana analankhula motsata kunyanda ndipo anati “Udzakhala ngati Mulungu” izi ndi zizindikiro za kunyada.
- Kuyang’ana kwambiri za kufunika kwako (Masalimo 101:5)
  - Kukhala ndi mayankho onse (Miyambo 3:7)
  - Kuyang’ana monyada (Miyambo 6; 17)
  - Kugwiritsa ntchito kwambiri mawu akuti “Ine” ndi “zanga”: Isaiah 14:14-16
  - Kuyang’ana kwambiri za mawonekedwe abwino a munthu: Isaiah 28: 1
  - Kukondwera ndi kulamulira anthu nthawi: Mateyu 20:26-27
  - Kukonda maundindo: Mateyu 23:6-11
  - Kudziyamikira wekha chifukwa cha ntchito yabwino imene yagwirika: Machitidwe 12:21-23
  - Kuchita zinthu ndi zolinga zoyipa: Aroma 8:6
  - Kulimbirana mpando m’mapwando kapena malo aulemu: Marko 12:38-39
  - Kuyangana kwambiri zokhudza nzeru zako: 1 Akorinto 3:20
  - Kukondwera kwambiri kukhala pakati pa anthu ofunika kwambiri: 1 Akorinto 4:6-7
  - Kudziyamikira: 2 Akolinto 10: 1:12-15
  - Kudziyamikira chifukwa cha ntchito yochitika ndi ena: 2 Akorinto 10:12-13
  - Kusakhudzika ndi zimene ena akudutsamo: Afilipi 2-4
  - Kukhala wotanganidwa ndi nthanu zachabe 1 Timoteo 6:4
  - Kudzitamandila chifukwa cha zimene wakhonza kuti achite: Yakobo 4:16
  - Kusagwiritsa ntchito upangiri ochokera kwa anthu ena auzimu: 1 Petro 56-7
  - Kukhala wodzidalira wekha osati Mulungu: Aefeso 5:21
  - Kudandawula m’ malo mopereka zopweteka zonse kwa Mulungu: 1 Petro: 1 Petro 5:15-16
5. Yesu anapemphera kuti anthu asalephere. Werengani Yohane 18:15 ndi 20

6. Kuchokera pa Mateyu 23, pangani m'ndandanda wa malamulo khumi a mtsogoleri wa Chikristu. Kulephera kwina kulikose kwa Afarisi kukhoza kubwezedwa ndi kutipatsa ndondomeko zabwinozi.
7. Buku la Miyambo liri ndi machenjezo ambiri okhudzana ndi zinthu zimene zimabweretsa kulephera. Werengani chaputala chimodzi tsiku lina lirilonse ndipo mukhoza kuwerenga buku lose mwezi umodzi. Onani zinthu zimene zikhoza kupangitsa kuti mulephere ndipo muzipewe (Muthanso kufuna kupanga izi m'mabuku ena)
8. Gawo loonjezera la maphuzirowa likufotokoza kuti tikhoza kuwerenga bwanji nkhani za atsogoleri amene ali M'baibulo. Werengani mtsogoleri amene analephera ndipo pangani m'ndandanda wa zinthu zimene zinamulepheretsa.
9. Mabuku a 1 ndi 2 Timoteo ndi Tito analembedwa kwa wachinyamata amene anali mtsogoleri muutumiki. Werengani mabukuwa mosamala ndikulemba m'ndandanda wa zinthu zimene mtumwi Paulo anawauza kuti apewe.

## CHAPUTALA 12

### MFUNDO ZOPAMBANIRA

#### ZOLINGA:

Mukamaliza phuziro muzikwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi yotsogolera osawonera.
- Kupereka tanthauzo la kupambana.
- Kufotokozera kuti tanthauzo la kupambana la M'baibulo limasiyana bwanji ndi tanthauzo la kudziko lapasi.
- Kulemba mwachidule ndondomeko za kupambanira.
- Kupanga kafukufuku wina wokhudzana ndi ndondomeko zina zakupambana.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Buku ili la cilamulo lisacoke pakamwa pako; koma ulingiriremo usana ndi usiku, kuti usamalire kucita monga mwa zonse zolembedwamo; popeza ukatero udzakometsa njira yako, nudzacita mwanzeru. (Joshua 1:8)**

#### MAU OYAMBA

Anthu amene anapambana amafunsidwafunsidwa, “kodi chinsisi chakupambana kwanu ndi chiani?” Amene ndi akudziko amatchula zinthu ngati maphuziro, undindo, chilakolako, luso, mphamvu, ndi ndalama. Mabuku ambiri alembedwa pa mutuwu koma mfundo zakupambana zinawonetsedwa M'baibulo. Phunziroli litiphunzitsa za ndondomeko za M'baibulo zakupambana. Pali kulingalira kuti munayala kale maziko achikhulupiriro opezeka pa Ahebri 6:1-3. Maziko auzimu ndiofunika kuti mugwiritse ntchito ndondomeko zakupambanira m'moyo wanu ndi muutumiki.

#### CHIPAMBANO NDI CHIANI?

Mu Ufumu wa Mulungu chipambano ndi “Kugwiritsa ntchito Mphatso komanso kuthekera mumpingo mogwirizananso ndi udindo umene unapatsidwa.” Ndinu opambana ngati mugwiritsa ntchito bwino zinthu zauzimu pa ntchito ya uzimu.

Mulingo wopambana wa Muufumu wa Mulungu usiyana ndi wakudziko la anthu. Dziko lapasi limawona kupambana powona kuchuluka kwa zinthu. Mulungu amawona uzimu. Mufumu wa Mulungu muli mulingo wina otanthauzira kupambana. Dziko lapasi liri ndi Mulingo wake. Mulingo wa Mulungu umatchulidwa kuti “kukhulupirika.”

Pali maziko ena akupambana. Maziko atanthauzo la kupambana la kudziko ndi limasinth komanso ndilosakhalitsa. Mufumu wa Mulungu, maziko akupambana sasintha ndipo ndi okhalitsa chifukwa amakhazikika pa chowonadi chowonetsedwa. Pali zolinga zosiyanasiyana zakupambana. Kudziko lapasi, anthu amalimbikitsidwa ndi kudzitamandira, chilakolako chodziwika ndi kufuna kuti zonse zikhale zawo. Okhulupirira amalimbikitsidwa chifukwa cha ulemerero wa Mulungu.

Mufumu wa Mulungu muli chitsanzo china chakupambana. Dziko limayang'ana anthu a chuma ndi mphamvu. Chitsanzo chathu ndi Ambuye Yesu. Pali cholinga china chakupambana monga, ndalama, mphamvu ndi udindo zimatsindikizidwa zolinga za anthu adziko lapasi. Cholinga cha Ufumu wa Mulungu ndi kufanana ndi Yesu Khristu.

Kupambana mufumu wa Mulungu kumatsindika kwambiri pa kupereka osati kulandira, kutumikira osati undido, kudzichepetsa osati kudzikuza, kufoka osati mphamvu. Dziko limawona kupambana monga zimene ukuchita. Mulungu amawona chimene uli. Kupambana kwa chikhalidwe kumatsindikizidwa kusiyana ndi kukwaniritsa zinthu.

Mufumu wa Mulungu kupambana sikumawerengedwa chifukwa cha chimene uli. Koma kumawerengedwa pofanizidwa ndi zimene utha kukhala. Kupambana sikumawerengedwa ndi zimene mukumuchitira Mulungu. Kumawerengedwa pofanizitsa ndi zimene mukanakhala mukuchita.

### **CHINSISI CHAKUPAMBANA**

Mulungu akufuna kuti inu mupambane mutumiki wanu. Afuna kuti inu mukwaniritse cholinga ndi ndondomeko zimene ali nazo pa inu. Zinsisi za uzimu zakupambana siziri zinsisi kwenikweni. Zinanenedwa momveka bwino m'Mau a Mulungu. Ziri zinsisi chabe chifukwa chakuti anthu amakana kufufuza ndi kuzipeza.

Sitingawone mfundo iriyose yakupambana m'mawu a Mulungu chifukwa ndi zambiri. Gawo la "Kudziwa Zambiri" mphuziroli limapereka ndondomeko zakudziwa mfundo zambiri za m'baibulo. Koma mfundo zina zofunika kwambiri zapatsidwa m'musimu.

### **KHALANI NDI MAWONEDWE ABWINO**

Kupamana kumayambira ndi munthu obisika wamuntima:

**Koma Yehova ananena ndi Samueli, Vsayang'ane nkhope yace, kapena kutalika kwa msinkhu wace, popeza Ine ndinamkana iye; pakuti Yehova saona monga aona**

**munthu; pakuti munthu ayang'ana cooneka ndi maso, koma Yehova ayang'ana muntima. (1 Samuel 16:7)**

Mawonedwe a mtima abwino ndizinthu ngati, chikondi, kudzichepetsa, kumvera, mzimu wotumikira, ndi chiyero choona.

### **DZIWANI GWERO LAKUPAMBANA**

Zimapangitsa kupambana sizimene umadziwa koma amene umadziwa. Ubale umakhazikika pa amene umadziwa osati zimene umadziwa. Moyo onse umakhazikika pa ubale. Amene umadziwa (Yesu) osati zimene umadziwa zidzakutengerani kumwamba.

Kudziwa Ambuye kumadzetsa chipambano:

**Atero Yehova, wanzeru asadzitamandire m'nzeru zace, wamphamvu asadzitamandire m'mphamvu yace, wacuma asadzitamandire m'cuma cace; koma wakudzitamandira adzitamandire adzikweze umo, kuti ali wakuzindikira, ndi kundidziwa Ine, kuti ndine Yehova wakucita zokoma mtima, ciweruziro, ndi cilungamo m'dziko lapansi, pakuti m'menemo ndikondwerera, ati. Yehova. (Jeremiah 9:23-24)**

**Ndipo akucitira coipa cipanganoco iye adzawaipisa, ndi kuwasyasyalika; koma anthu akudziwa Mulungu wao adzalimbika mtima, nadzacita mwamphamvu. Ndipo aphunzitsi a anthu adzalangiza ambiri, koma adzagwa ndi lupanga, ndi lawi lamoto, ndi undende, ndi kufunkhidwa masiku ambiri. (Daniel 11:32-33)**

### **FUNANI AMBUYE:**

Kufuna ambuye zitanthawuza kudikirira pa iye pomfusira nkupemphera, kuwerenga Mau cholinga chakuti umudziwe ndi kuchita chifuniro chake. Ubwino womfuna Ambuye unatsimikizika ndi Hezekiya, mfumu ya Chiyuda. Anafuna Mulungu ndipo ichi ndi chimene chinampambanitsa.

**Momwemo anacita Hezekiya mwa Yuda lonse nacita cokoma, ndi coyenera, ndi cokhulupirika, pamaso pa Yehova Mulungu wace. Ndipo m'nchito iri yonse anaiyamba m'utumiki wa nyumba ya Mulungu, ndi m'cilamulo, ndi m'mauzo, kufuna Mulungu wace, anacita ndi mtima wace wonse, nalemerera nayo. (2 Mbiri 31:20-21)**

Zamfumu Uziya zinanenedwaso:

**Ndipo iye anali munthu wakufuna Mulungu masiku a Zekariya, ndiye wozindikira masomphenya a Mulungu; ndipo masiku akufunira Yehova iye, Mulungu anamlemereza; (2 Mbiri 26:5)**

Ndizofunika kumfuna Ambuye chifukwa Mulungu anafuna kuwonetsa dongosolo ndi cholinga chake kwa atsogoleri (Onani Amosi 3:7)

#### **LINGALIRANI MAWU:**

Chipambano chinalonjezedwa kwa amene amalingalira mawu. Ambuye anamuwuzwa Yoswa:

**Buku ili la cilamulo lisacoke pakamwa pako; koma ulingiriremo usana ndi usiku, kuti usamalire kucita monga mwa zonse zolembedwamo; popeza ukatero udzakometsa njira yako, nudzacita mwanzeru. (Yoswa 1:8)**

“Kulingalira” kumatanthawuza kuganiza, kuima kwambiri, kukumbukira ndi kuwerenga mwa tsatanetsatane. Amene amalingalira akhulupirira kuti Mulungu analankhulana ndi munthu, Baibulo ndi mawu amene analankhula ndikuti mawu a Mulungu ndi owona.

#### **VERANI MAWU:**

Sikulingalira chabe kumene kumadzetsa chipambano komanso kumvera mawu....

**Buku ili la cilamulo lisacoke pakamwa pako; koma ulingiriremo usana ndi usiku, kuti usamalire kucita monga mwa zonse zolembedwamo; popeza ukatero udzakometsa njira yako, nudzacita mwanzeru. (Yoswa 1:8)**

Solomoni asanakhale mfumu ya Israeli, Davide anapereka upangiri uwu:

**Tsono, mwana wanga, Yehova akhale nawe; nulemerere, numange nyumba ya Yehova Mulungu wako monga ananena za iwe. Cokhaci, Yehova akupatse nzeru ndi luntha, nakulangize za Israyeli, kuti usunge cilamulo ca Yehova Mulungu wako, (1 Mbiri 22:11-12)**

Lamulo liri lonse Mau a Mulungu ndi lofunika. Kusunga malamulowa kudzakupangani kukhala opambana.

Pa inu nokha, simukuyenera kulingalira ndi kumvera Mau a Mulungu okha, mukuyenera kuwakwezanso pa malo ake aulamuliro kwa anthu amene mukuwatsogolera. Werengani m'mene Nehemiya anabwezeretsera mphamvu ya Mau a Mulungu pa Nehemiya 8:1-8. Kukonzanso kumene Nehemiya anapanga sikukanakhalitsa opanda ulamuliro wa Mauu a Mulungu. Utumiki wokhazikika pa ulamuliro wa Mau a Mulungu udzakhalitsa.

#### **KUTCHULIDWA ANA A MULUNGU:**

Ndikupezeka kwa Ambuye kumene kumapititsa patsogolo utumiki:

**Ndipo Yehova anali ndi Yosefe; ndipo iye anali wolemeralemera; nakhala m'nyumba ya mbuyace M-aigupto. Ndipo mbuyace anaona kuti Yehova anali ndi iye, ndi kuti Yehova anamlemereza m'dzanja lace zonse anazicita. (Genesisi 39:2-3)**

Mulungu atha kukhala nanu pokhapokhapo muli ndi ubale wabwino ndi iye, mukutumikiraso monga mwa maitanidwe anu ndi kukhala moyo wachiyero.

#### **KHALANI NDI KUDZOZA KWA MULUNGU:**

Chaputala 3 m'phunziro iri kunafotokozedwa za ubwino wa kudzoza kwa Mulungu. Mukuyenera kukhala ndi kudzoza kumeneku kuti mupambane muutumiki.

#### **KUMANANI NDI MAVUTO NDI ZISANKHO:**

Kukana kukumana ndi mavuto komaso zisankho kumabweretsa kulephera. Kumanani ndi mavuto pompopompo ndipo pangani zisankho mwanzeru kugwiritsa ntchito ndondomeko zimene munaphunzira.

#### **DZIWANI CHOLINGA CHANU:**

Mulungu ali ndi cholinga chenicheni ndi okhulupirira aliyese. Kudziwa cholinga chanu kumakhudzana ndi kukhala ndi masophenya auzimu, chidziwitso chachifukwa chokhala ndi moyo ndi chimene Mulungu anakuitanirani kuti muchite. (Mukhoza kuphunzira zambiri m'maphunziro a Harvestime International otchedwa “Kuyang'anira ndi Zolinga.”)

Munthu wa masophenya samakhala moyo wakale, kudandaula mu zolakwika kapena kuima pa kupambana kwake pa zinthu zina. Masomphenya komanso chidziwitso cha cholinga chimathandiza kuti munthu ayang'ane kwambiri za mtsogolo. Monga Paulo ananena:

**Abale, ine sindiwerengera ndekha kuti ndatha kucigwira: koma cinthu cimodzi ndicicita; poiwaladi zam'mbuyo, ndi kutambalitsira zam'tsogolo, (Afilipi 3:13)**

#### **KHALANI NDI DONGOSOLO**

Simungakwaniritse cholinga chanu pokhapokha mutakhala ndi dongosolo lopangira.

M'maphunziro a Harvest International Institute otchedwa “Kuyang'anira ndi Zolinga.” mukhoza kuphunzira mapangidwe a dongosolo.

#### **KUCHITA ZINTHU MONGA MWA DONGOSOLO LOPANGIDWA**

Kukhala ndi dongosolo labwino sikokwanira kuti mukwaniritse cholinga mutumiki wanu.

Mukuyenera kuchita zinthu monga mwadongosolo lanu. Mukuyenera kuchita zoyikika m'dongosolo lanu. Mukuyenera kulongosola, kupereka ntchito kwa ena komanso ndikuonetsetsa



kuti zikuyenda bwino. Chinthu chimodzi chodziwitsa utsogoleri wabwino wauzimu ndikuwonetsa kuti ukubweretsa chipambano ndi kuti zolinga komaso dongosolo la Mulungu zikukwaniritsidwa. Mukhoza kuphunzira mapangidwe a izi m'maphunziro a Harvestime International Institute otchedwa "Kuyang'anira ndi Zolinga."

#### **KHALANI MOYO WACHIYERO:**

Mudzakhala opambana mufumu wa Mulungu pokhapokhapo mutakhala moyo wa chiyo, kufikira zoyenera za atsogoleri okambidwa mu chaputala 4 cha maphunzirowa. Tchimo limanthawuza kulephera. Chiyo chitanthawuza chipambano.

**Wobisa macimo ace sadzaona mwai; Koma wakuwabvomereza, nawasiya adzacidwa cifundo. (Miyambo 28:13)**

#### **FUNANI NZERU KWA MULUNGU:**

Zeru za munthu sizokwanira kupanga zisankho ndi kutsogolera ena. Mukuyenera kukhala ndi nzeru kuchokera kwa Mulungu kuti mukhale mtsogoleri wabwino.

**Koma wina wa inu ikamsowa nzeru, apemphe kwa Mulungu, amene apatsa kwa onse modzala manja, niwosatonza; ndipo adzampatsa iye, (Yakobo 1:5)**

#### **YETSANI KUCHITA ZINTHU MWAPAMWAMBA:**

Musakhutitsidwe ndi zinthu zabwino chabe, yesetsani kuchita zinthu mwapambamba:

**kuti mukayese inu zinthu zosiyana; kuti mukakhale a mtima woona ndi wosalakwa, kufikira tsiku la Kristu; (Filipo 1:10)**

#### **CHITANI ZONSE KULEMERERO WA MULUNGU:**

**Ndipo ciri conse mukacicita m'mau kapena muncbito, citani zonse m'dzina la Ambuye Yesu, ndi kuyamika Mulungu Atate mwa iye. (Akolose 3:17)**

#### **YAMBANI MWATHANGA UFUMU:**

Mudzakhala opambana mufumu wa Mulungu ngati mudzatsogoza:

**Koma muthange mwafuna Ufumu wace ndi cilungamo cace, ndipo zonse zimenezo zidzaonjeredwa kwa inu. (Mateyu 6:33)**

Kulongosola zinthu kumapangitsa kuti zinthu zofunika ziyikidwe patsogolo. (Onani Machitidwe 6:1-7)

#### **TSATIRANI CHITSANZO:**

Mukamaphuzira phuziroli, Yesu ndiye chitsazo chachikulu cha mtsogoleri wauzimu. Yesu anati:

**Pakuti ndakupatsani inu citsanzo, kuti, monga Ine ndakucitirani inu, inunso mucite.  
(Yohane 13:15)**

Sibwino ngati mutadzifanizira ndi china chirichose osati chitsazo cha Khristu. Yakobo anafanizira Yosefe ndi abale ake ndipo anapangitsa zinthu zimene zimachitika chifukwa cha nsanje ndi kwiyo. Saulo anava kufanizidwa pakati pa iye ndi Davide ndipo anawonongedwa ndi mkwiyo. Kufananitsa ndikofunikira ngati kukukulitsa masomphenya anu ndikukupangani kuti mukwaniritse kuthekera kwanu. Koma zimene wina wakwaniritse simulingo wa moyo wanu. Kupambana kwanu sikumawerengedwa mogwirizana ndi zimene ena akwaniritse. Chifukwa cha ichi pempho la Petro lakuti “Ambuye nanga munthu uyu” linadzudzulidwa. “Kodi ziri chiyani ndi iwe?” Unditsate ine.” (Yohane 21:21-22)

### **CHISANKHO, KUSUNGA MWAMBO, CHITSOGOZO, KULIMBA NTIMA**

Chilungamo chikhoza kunenedwa mwachidule m’chiganizo chimodzi:

Tsatirani chitsanzo cha Yesu m’zisankho, kusunga mwambo, chitsogozo, ndi kulimba ntima.

Mtumwi Paulo anati:

**Kodi umudztwa kuti iwo akucita makani a Iwiro, athamangadi onse, koma nmodzi alandira mfupo? Moteru 2 thamangani, kuti mukalandire. Koma yense wakuyesetsana adzikaniza zonse. Ndipo iwowa atero kuti alandire korona wakubvunda; 3 koma ife wosabvunda. Cifukwa cace ine ndithamanga coteru, si nonga cosinkhasinkha. Ndilimbana coteru, si monga ngati kupanda nlengalenga; koma 4 ndipumpuatha thupi langa, ndipo ndiliyesa capolo; kuti, kapena ngakhale rdalalikira kwa ena, 5 ndingakhale votayika ndekha. (1 Akolinto 9:24-27)**

Paulo anapanga chisankho. Anafuna kupambana. Ankafuna kuwina mtundu wa moyo (ndime 24). Kutu achite izi, anazindikira kuti akuyenera kukhala osunga mwambo zimene zitanthawuza kukhala chitsazo m’zonse. (Ndime 25 ndi 27). Anali ndi chitsogozo. Sanathamange kapena kumenya opanda cholinga. Sanali okaika pa cholinga kapena dongosolo lake (Ndime 26). Analinso olimba ntima kuti atenge, kuti apambane (Ndime 24 ndi 25)

### **MTENGO WAKUPAMBANA**

Ndinu okonzeka kulipira mtengo wa kupambana? Dipo lake nali:

**iyere amene sanacidziwa, ndipo anazicita zoyenera mikwapulo, adzakwapulidwa pang'ono. Ndipo kwa munthu ali yense adampatsa zambiri, kwa iye adzafuna**

**zambiri; ndipo amene anamuikizira zambiri, adzamuza abwezere zoposa. (Luka 12:48)**

Mulungu amafuna zambiri kuchokera kwa inu mukamapambana. Uwu ndiye mtengo wakupambana.

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osawonera.

---

---

2. Lembani tanthauzo lakupambana.

---

---

3. Kodi kupambana monga mwadziko lapansi limasiyana bwanji ndi kupabana monga mwa Ufumu wa Mulungu?

---

---

---

4. Lembani mwachidule mfundo zakupambana zimene mwaphunzira.

---

---

---

---

(Mayankho amafuso osewa aperekedwa kumapeto kwa bukhu lino)

## KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

Phunziro iri laima pa mfundo za kupambanira. Pali mfundo zina zambiri zopambanira zimene zinalembedwa m'Mau a Mulungu. Gawo iri likuthandizani kupitiriza kuphunzira maphunziro ambiri.

1. M'chaka cha mawa, muwerenge Baibulo lonse. Sungani lamulo lirilose limene lapatsidwa. Kusunga malamulowa zitanthauza kupambana kwa utumiki wanu (Yoswa 1:8).
2. Kumapeto kwa phunziroli kukufotokoza kaphunziridwe ka moyo wa atsogoleri amene mbiri yawo inakambidwa M'baibulo. Phunzirani moyo wa atsogoleri amene anapambana. Onani zinthu zimene zinawapambanitsa ndipo zimphatikizireni izi m'moyo wanu.
3. Werengani bukhu la m'neneri limene likufotokoza za kupambana monga mwa dziko lapansi. Makamaka onani chaputala 2. Munthu amene kupambana kwake kumaina pa mulingo umenewu amakhala wa chabe komanso osakondwera. Werengani chimaliziro pa Mlaliki 12:13-14.
4. Mabuku a 1 ndi 2 Timoteo ndi Tito analembedwa kwa nyamata amene anali ndi udindo muutumiki. Werengani mabukuwa mosamala ndipo lembani m'ndandanda wa mfundo zakupambanira zimene mtumwi Paulo akugawana nafe.
5. Kumbukirani izi: Ziribwino kuyesera ndi kulephera kusiyana ndi kusapanga chirichose ndi kupambana. Simumalephera pokhapokhapo mutasiya.
6. Chuma ndichofunika kwambiri kuutumiki umene ukupambana. Mumafunika ndalama kuti mumalizitse ntchito ya Mulungu. Pali mfudno zina za kupambana pa chuma: Mulungu ndiye Gwero lanu: Genesis 22:14.  
Mulungu amafuna inu mutachita bwino ku gawo la chuma: Masalimo 35:27; 23:1 Marko 12:43.44; Aefeso 3:29; Agalatiya 3:13; Timoteyo 6:17; 3 Yonane 2.  
Mukaika Mulungu poyamba, adzakupatsani zofuna zanu: Mateyu 6:33

Kupambana pa chuma ndi mphoto:

-Kuika Mulungu patsogolo: Miyambo. 3:9-9-10; Mateyu 6:33

-Kukonda Mulungu: Miyambo 8:21

-Kumpatsa Mulungu ulemerero: Miyambo 13:21:15:6

-Kudzichepetsa. Miyambo 22:4

-Kukhala okozeka kupereka: Miyambo 22:9

-Kudalira Mulungu: Miyambo 28:25

-Kufesa moolowa manja: Miyambo 11:24-25; Luka 6:38; 2 Akolinto 9:6, 10

Mulungu amakupatsani mphavu yakupeza chuma: Deuteronomy 8:18-19

Chuma ndi zotsatira za kugwira ntchito molimbika:

Kugwira ntchito molimbika: Miyambo 10:4; 13:4

-Ntchito ya nzeru: Miyambo 10:5

-Ntchito yooni: Miyambo 13:11

-Ntchito yachete: Miyambo 14:23

Kupereka kumapanga kuti mupambane pa chuma. Mukuyenera kupereka:

-Choyamba kwa Ambuye: Malaki 3:1-2; Miyambo 3:9-10

-Mokondwera: 2 Akolinto 9:7

-Mofulumizika mtima: Eksodo 25:2; 1 Mbiri 29:7

-Mwaufulu: Ezra 2:68

-Monga mwakuthekera kwanu: Mateyu 5:42; Machitidwe 11:29; 2 Akorinto 8:12; Deuteronomo 16:17; Ezra 2:69

-Kulemerero wa Mulungu: Mateyu 6:3

-Modzichepetsa: Aroma 12:8

-Kwa osauka: Miyambo 3:27-28; 19:17; 21:13; 28:27

-Mosadziwonetsera; Mateyu 6:3

-Pafupipafupi: 1 Akonto 16:2

-Mofanana ndi momwe mumapezera: Genesisi 14:20; 28:22; Levitiko; 27:30; 2 Mbiri 31:5; Malaki 3:10

Kuti mupambane pa chuma mukuyenera kupewa izi;

-Chikondo cha pa ndalama: 1 Timoteo 6:10

-Kudalira Chuma: Masalimo 49:6; 1 Mbiri 29:14

-Ngondole: Aroma 13:8

-Ulesi: Miyambo 6:6-11; 24:30-34

-Kukonda zosangalatsa thupi: Miyambo 13:18; 21:17; 23: 2:21

- Kulota: Miyambo 13:4
  - Ziwawa: 1:10-19
  - Kusaona mtima: Yakobo 5:3-4; Miyambo 20:23; 13: 11; 22:16
  - Chinyengo: Miyambo 10:2
  - Katangale: Miyambo 14:27
  - Kusakhulupirika: Machitidwe 5:3-4; Miyambo 21:6
  - Njira zopezera chuma mwachangu; Miyambo 37:20
  - Kubwereka osabweza; Masalimo 37:21
  - : Miyambo 6:1 11:15; 22:26
  - Zizolowezi zolakwika: Miyambo 23:21
  - Kusagonjera kumene kumakhudza chipambano pa chuma: Miyambo 13:18
  - Kukonda ndalama: Miyambo 10:22; 1 Timoteo 6:10
  - Osapereka malipiro abwino: Yeremiya 22:13
  - Kufuna kudzikundikira zonse: Miyambo 28:22
  - Kukana malangizo a Mulungu: Miyambo 13:18
  - Kulandira zopereka zambiri cholinga chakuti mupindule: 1 Samuel 2:29
  - Kubisa chopereka: Miyambo 11:24
- Mudzakula m'moyo wanu wa uzimu pa mulingo wakukhulupirika m'maperekedwe:  
Luka 16:11

7. Buku la Miyambo liri ndi mfundo zamphamvu zakupambanira. Werengani chaputala chimodzi tsiku liri lonse ndipo mukhoza kuwerenga buku lonse kamodzi pa mwezi. Onani mfundo zakupambanira M'baibulo lanu ndipo lingilirani pa izo. Zigwiritseni ntchito m'moyo ndi utumiki wanu.
8. Izi ndi zina mwa zinthu zauzimu zoletsa munthu kuti asachite bwino pa chuma ndi kupambana:
 

-Deuteronome	-Masalimo 1:3; 73:12; 122:6
-Yoswa 1:8:9	-Miyambo 28:13
-2 Mbiri 31:21; 32:30	-Mlaliki 7:14; 11:6
-1 Mafumu 2:3	-Yesaya 54:17; 55:11
-Nehemiya 1:11; 2:20	-3 Yohane 2
9. Hezekiya anali ndi ndondomeko zinayi za kupambanira. Ana....

-Dalira Ambuye

-Kakamira iye (Ubale weniweni)

-Anamutsatira iye

-Anasunga malamulo ake.

Chifukwa cha izi anapambana mzonse zimene anapanga.



## CHAPUTALA 13

### KUWERENGA MALIPIRO

#### ZOLINGA:

Mukamaliza phunziro lino muyamba kukwanitsa kuchita izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osawonera.
- Kulemba mwachidule mpali zitatu za dipo lautsogoleri.
- Kupeza yesero lenileni la utsogoleri wabwino.

#### VESI LOTSOGOLERA:

**Pomwepo Yesu anati kwa ophunzira ace, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikane yekha, natenge mtanda wace, nanditsate Ine. (Mateyu 16:24)**

#### MAU OYAMBA

Mwaphuzira m'maphuzirowa kasamalidwe ka zinthu zauzimu kudzera mtsogoleri wabwino.

Mwaphuzira kuti mungakhale bwanji mdindo wabwino ndikutsogolera ngati kapolo kapena mbusa.

Munaphuzira ntchito ndi zomuyenerereza mtsogoleri, ubwino wa kudzoza ndi kapezedwe kamayankho a mavuto.

Funso limodzi lokha ndilimene latsala, “Kodi ndinu okonzeka kulipira dipo la kutumikira ngati mtsogoleri wauzimu?”

### KUWERENGERA MALIPIRO

Yesu anatsindika za ubwino owerengela malipiro zisakho zisanapangidwe. Anagwiritsa ntchito zitsazo ziwiri, cha munthu wakumanga nyumba ndi mfumu yopita kunkhondo.

**Ndipo m'mene iwo analikuyenda m'njira, munthu anati kwa iye, Ine ndidzakutsatani kumene kuli konse mukapitako. Ndipo Yesu anati kwa iye, Nkhandwe ziri nazo nkhwimba, ndi mbalame za kumwamba zisa, koma Mwana wa munthu alibe potsamira mutu. (Luka 9:57-58)**

Kudzera kuzitsazo zimenezi Yesu anafokokozerera zaubwino owerengera malipiro usanadzipeke mwauzimu. Kodi malipiro akutumikira ngati mtsogoleri wauzimu ndi ati?

### MBALI ZIWIRI ZA UTSOGOLERI

Werengani Luka 9:57-62 M'baibulo lanu. Nkhani imeneyi amuna atatu anamupeza Yesu popeza amafuna kukhala akuphonzira. Kwa amuna awiri onsewa, Yesu anawonetsera malipiro osiyanasiyana autsogoleri:

**KULINGALIRA ZA MALIPIRO:**

**Ndipo m'mene iwo analikuyenda m'njira, munthu anati kwa iye, Ine ndidzakutsatani kumene kuli konse mukapitako. Ndipo Yesu anati kwa iye, Nkhandwe ziri nazo nkhwimba, ndi mbalame za kumwamba zisa, koma Mwana wa munthu alibe potsamira mutu. (Luka 9:57-58) (Luka 9:57-58)**

Munthu oyamba amafuna kukala ophonzira chifukwa cha mphamvu yake. Samadikira kuti ayitanidwe ndi Yesu. Monga kukhala ophonzira, utsogoleri sichinthu chimene munthu amachita kuzipereka kwa Mulungu. Ndi kuitana kwa Mulungu kwa munthu. Ukayesera kutsogolera pogwiitsa ntchito mphamvu zanu, mulephera. Mukuyenera kuitanidwa ndikudzozedwa ndi Mulungu. Yesu anati kwa mwamuna “Unditsate ine, udzakumana ndi izi.” Malipiro autumiki ndi kutumikira komaso kudzipereka.

**Umo tizindikira cikondi, popeza Iyeyu anapereka moyo wace cifukwa ca ife; ndipo ife tiyener kupereka moyo wathu cifukwa ca abale. (1 Yohane 3;16)**

Malipiro autsogoleri akukhudzana ndi kukhala wekha. Paulo anati

**Ici ucidziwa, kuti onse a m'Asiya adabwerera kusiyana nane; a iwo ali Fugelo ndi Hermogene, (2 Timoteo 1:15)**

Atsogoleri amakanidwa ndi kutsutsidwa:

**Anadza kwa zace za iye yekha, ndipo ace a mwini yekha sanamlandira iye. (Yohane 1:11)**

Mtsogoleri amazuzidwaso. Werengani zinthu zovuta zimene Paulo anakumana zazo pa 2 Akorinto 11:23-27.

Mtsogoleri ali ndi ntchito yambiri:

**Popanda zakunjazo pali condisindikiza tsiku ndi tsiku, calabadiro ca Mipingo yonse. (2 Akorinto 11:28)**

Mtsogoleri akuyenera kusunga mwambo:

**koma 4 ndipumpuatha thupi langa, ndipo ndiliyesa capolo; kuti, kapena ngakhale rdalalikira kwa ena, 5 ndingakhale votayika ndekha. (1 Akorinto 9:27)**

Mtsogoleri ali ndi udindo waukulu kuyenda moyenera maitanidwe ake:

**Cifukwa cace popeza tiri nao utumiki umene, monga talandira cifundo, sitifoka; koma takaniza zobisfka za manyazi, osayendayenda mocenjerera, kapena kucita nao mau a Mulungu konyenga; koma ndi maonekedwe a coonadi tidzibvomeretsa tokha ku cikumbu mtima ca anthu onse pamaso pa Mulungu. (2 Akorinto 4:1-2)**  
**Ndikudandaulirani inu tsono, ine wandende mwa Ambuye, muyende koyenera maitanidwe amene munaitanidwa nao, (Aefeso 4:1)**

### **ZINTHU ZOYENERA KUYIKIDWA PATSOGOLO**

Munthu wachiwiri anayitanidwa ndi Yesu “Unditsate”. Monga mwaphuzirira, “Kutsatira” zitanthawuza kupita pambuyo pa amene akupita patsogolo, kutengera chitsazo. Zimakhudzana ndi kukhulupirira komaso kuvera.

Yesu atanitana akuphuzira ake khumi ndi awiri, anawawuza kuti amutsatire iye. Sananene bwinobwino njira yowoneka. Sanawapatse ndanda wa zochitika. Ophuzira anasiya moyo wake wakale Kumbuyo chifukwa cha maitanidwe okha basi. Zisanho, kusiyana, komaso kudzipereka zimene zidzafunika zimakhala zosadziwika.

Mtsogoleri ndi munthu amene amasiya moyo wachitetezo kutsatira moyo opanda chitetezo nkuwona kwa dziko lapasi. Kudzipereka si kwa zochitika zokha koma kwa munthu. Munthu ameneyu ndi A mbuye Yesu Khristu. M’nkhani ya Luka, yakho la munthu atainanidwa kuti unditsate linali lakuti “Choyamba uvutike kaye” Anafuna kutsatira Yesu, koma sanali patsogolo. Yesu sankanena kuti munthu akuyenera kusalabadira zofuna za makolo ake (onani Yohane19:25-27). Ndizokhudza zithu zofunika kwambiri zimene zinatsindikizidwa mkhaniyo. Mwamunayu anati akhafuna “kaika bambo ake” kaye. Mchipangano chakale munthu akati afuna “akaika bambo ake kaye” samathawuza kuti bambo ake amwalira. Zimatanthawuza kuti adikirebe kufikira bambo ake atafa kuti alandire cholowa chimene chimakhala chake. Ndiye pameme muthuyu atapereka chifukwa chimenecho amaika patsogolo tsogolo lacholowa chake asanaianidwe ndi Ambuye Yesu Khristu. Mthawi yofunika kwambiri yesu akaitana munthu kuti amutsate kuti akhale mtsogoleri, china chiri chonse sichikuyenera kuikidwa pamwamba pa maitanidwe.

Ndime zina Yesu anafotokoza momveka bwino ubwino oyika zinthu zoyenera patsogolo.

**Pomwepo Yesu anati kwa ophunzira ace, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikane yekha, natenge mtanda wace, nanditsate Ine. (Mateyu 16:24)**

Kudzikana wekha kukuyenera kuchitika munthu asanasenze ntanda. Munthu wakale ndi munthu wauchimo akuyenera kukanidwa (Aroma 7:8) Munthu wakale akakanidwa ntanda ukuyenera kukhala patsogolo. Mtanda ndi chizindikira cha kudzipereka, kuwawa, kukanidwa, kunyozedwa, ndi kuvuika zimene zimapezeka potumikira Mulungu. Mtanda ukutanthawuza maitanidwe akufa chifukwa cha Uthenga Wabwino.

Kusenza mtanda sizitanthawuza mavuto amoyo. Izi ndi zawina aliyese. Ndi kuvutika, mayesero, kukhumudwa ndi kupwetekedwa zimene timakumana nazo chifukwa tikukhala mdziko lauchimo. Okhulupirira akuyeneraso kukumana ndi mavuto amoyo uno. Amadwala, ngozi, moto ndi zowopsa za chilengedwe chifukwa chakuti akukhala mziko limene linawonongedaw ndi tchimo. Koma mavuto awa sikusenza mtanda. Kusenza ntanda kumachitika modzipereka, osati zokumana nazo chifukwa cha mavuto amoyo uno. Ndi kusankha motipirira kukana zilakolako za thupi ndi cholinga chochita chifuniro cha Mulungu.

Yesu anati, “Aliyense amene sangadzikane yekha nasenza mtanda wanga sangakhale ophunzira wanga. Kusenza ntanda sikokondweretsa kwa munthu wachilengedwe zimakhudzana kudzikana wekha. Zimayenera kuchitika modzipereka chifukwa cha Khristu.

Kuti usenze mtanda ukuyenera kukhala opanda chirichonse cha dziko lapasi. Ngati ntima wanu wakhazikiza pa ndalama ndi katundu, manja anu ali odzaza kwambiri kuti asenze ntanda. Ngati nthawi yanu ikumatha ndi chikondwerero ndi zinthu zimene zimakondweretsa thupi, manja anu ali odzaza ndi zinthu kuti asenze mtanda. Mutadzikaniza nokha ndi kusenza mtanda chotsatira ndi kutsatira. Mukuyenera kusiya moyo wakale ndi maubale akale auchimo.

Simungakhale mtsogoleri ngati mukungodikira kuti uchitike. Mukuyenera kutenga kanthu: Dzikanizeni nokha, senzani ntanda, ndikutsatira. Mateyu akanakhalabe pa tebulo lamtsonkho ndi Petro pamakoka ake. Onsewa akanamapanga malonda awo mokhulupirika ndipo adamasangala ndizokumana nazo zauzimu. Koma ngati amafuna kukhala atsogoleri Awuzimu, amayenera kusiya zinthu zakale ndi kukumana ndi zatsopano. Mateyu anasiya tebulo la msonkho ndi Petro anasiya Makoka.

Izi sizikutanthauza kuti wina aliyense akuyenera kusiya ntchito, ndi nyumba yake ndikukhala mtsogoleri. Zikutanthawuza kuti pakhala kusintha kwakhalidwe. Nthawi zina zimatanthaunso kusiya ntchito, nyumba, ndi okonedwa chifukwa cha Uthenga Wabwino. Mukuyenera kutsatira kulikonse kumene Yesu akukutsogolerani.

Kutsogoza zinthu zoyenera kutanthauza kuti mukuyenera kusiya zonse chifukwa cha maitanidwe.

**Cifukwa cace tsono, yense wa inu amene sakaniza zonse ali nazo, sakhoza kukhala wophunzira wanga. (Luka 14:33)**

Mukuyenera kutsogoza kutumikira ena:

**Sikudzakhala comweco kwa inu ai; koma amene ali yense akafuna kukhala warnkuru mwa inu, adzakhala mtumiki wanu; (Mateyu 20:26-28)**

Ufumu wa Mulungu ukuyenera kuikidwa patsogolo:

**Ndipo monga mufuna inu kuti anthu adzakucitirani inu, muwacitire iwo motero inu momwe. (Mateyu 6:31, 33)**

**ZOLINGA ZAZIKULU:** (Luka 9:61, 33)

Munthu wachitatu pa Luka 9:61-62 anafuna kumutsatira koma ankafuna kuchita izi potsatira mfundo zake. Kutsanzika apabanja ake chinali chinthu cha chizolowezi kuchita, koma Yesu anamuitana. Cholinga chake chenicheni m'moyo chinali chani? Amafuna kukhaladi mtsogoleri kapena kutsatira dongosolo lamoyo wake? Zolinga za munthuyu zinali zisanakhazikike, amasungira, amagawanika pakati pa moyo wakale ndi watsopano umene Yesu anamuitanira. Cholinga chake chachikulu m'moyo sichinali maitanidwe a Mulungu. Kudzipereka kwanu kuutumiki kukuyenera kukhala kokwanira. Chikuyera kukhala cholinga chanu chachikulu m'moyo.

**MAYESERO ENI ENI AUTSOGOLERI WA UZIMU**

Mayesero autumiki ndi amene amachitika pamene simuli ndi okutsatirani. Kodi mumakhalabe okhulupirika kuzimene mwawaphuzitsa? Kodi amaphuzitsa zimene amphuzira? Kodi akhoza kupitiliza kukhwima m'moyo wauzimu opanda kupezeka kwanu. Ngati zirichoncho mwapambana mayesu awutsogoleri wauzimu.

**VUTO LOMALIZA**

Muzikumbukira udindo wanu waukulu ngati mtsogoleri:

**Wophunzira saposaphunzitsi wace; koma yense, m'mene atakonzedwa mtima, adzafanana ndi mphunzitsi wace. (Luka 6:40)**

Osakhumudwa andi mavuto a okutsatirani. Yesu anakumana ndi mavuto. Nthawi ina, Petro, Yakobo ndi Yohane anawonetsa mtima wokwiya pamene anafuna kuti ayitane moto kuchokera kumwamba kuwononga midzi ya Asamaliya osamvera (Luka 9: 55). Petro anakana Ambuye

katatu (Luka 22:54, 62) Onse atatu anali atagona m'munda wa Getsemane pamene anauzidwa kuti apemphere (Luka 22:45-46).

Yesu amayenera kupatula nthawi ndi utumiki pa ophunzira ochepawa. Anatsimikidwa kuti anali anthu okhulupirika, posatengera zofoka ndi zolephera zawo. Kudzera mwa iwo Uthenga Wabwino unafalikira kumadera onse adziko lapansi. Ngati muli okonzeka kulipira dipo la utumiki ndizotheka kuti inunso mutha kudzutsa atumiki okhulupirika.

Ndinamva kuitana “bwera unditsate” zinali choncho.

Chikondwerero chadziko chinachepa.

Mtima wanga unamutsatabe.

Ndinaima ndikumutsa zinali choncho.

## MAFUNSO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani ndime yotsogolera pantima.

---

---

---

2. Kodi mbali zitatu za dipo la utsogoleri lolembedwa m' mphunziroli ndi chiani?

---

---

---

3. Kodi mayeso eni eni autsogoleri wauzimu ndi chiani?

---

---

(Mayankho amafunso onsewa apatsidwa kumapeto kwa bukhu lino)

## **KUDZIWA ZAMBIRI**

1. Werengani ndime zotsatirazo ndipo onani malipiro amene aliyense wa awa pa undindowake ngati mtsogoleri:  
Yosefe: Genesisi 37-50  
Mosesi: Buku la Eksodo  
Hoseya: Buku la Hoseya  
Ezekiel: Ezekieli 3  
Mtumwi Paulo: Machitidwe 9:28
2. Tsopano popeza mwamaliza kusanthula za kuyendetsa zinthu tikuganiza kuti muyambe kuphunzira maphunziro a Harvestime International Institute a “Kauniuni wa Zochitika Pakati pa Anthu” ndi “Kuyang’anira mwa Zolinga.”  
Maphunziro awa aonjezera chidziwitso chanu cha utsogoleri, kukonzekera, ndi kuika zinthu m’ malo komanso ofunika kuti mukhale ndi utumiki wamphamvu.



## ZOONJEZERA ZAPADERA

Gawo lino loonjezera likupatsani inu mwayi wakuti muphunzire zambiri zokhuza utsogoleri woyendetsa bwino zinthu pophunzira za miyoyo ya anthu ena owerengeka a m’Baibulo.

Kusanthula miyoyo ya anthu a m’Baibulo nkothandiza chifukwa mumaphunzira zambiri za kulephera kapena kupambana kwawo. Baibulo limati,

**Koma izi zinacitika kwa iwowa monga zoticenjeza, ndipo zinalembedwa kuticenjeza ife, amene matsirizidwe a nthawi ya panso pano adafika pa ife. (1 Akorinto 10:11)**

Nkhani za anthu akale zinalembedwa m’Baibulo zinalembedwa kuti ife tikapindule nazo. Momwe miyoyo yawo inayendera zimatipatsa maphunziro ambiri a utsogoleri. Mukamawerenga za kulephera kwao ngati atsogoleri, mutha kuphunzirapo zinthu zina zomwe zofunika kupewa. Poona za kupambana kwao ngati atsogoleri, mutha kuphunzira zabwino zambiri za momwe mungakhaliye mtsogoleri wamphamvu.

Pamene musanthula moyo wa munthu m’Baibulo tsatirani zinthu zinayi izi:

### **GAWO 1: SANKHANI MUNTHU WOTI MUSANTHULE**

Mutha kusankha munthu amene wakusangalatsani. Mungathe kugwiritsa ntchito m’ndandanda wa anthu amene ali mu Ahebri 11, Agalatiya 3:7, kapena Luka 4:27. Mutha kusanthula munthu m’bukhu limene mukuwerenga panopa.

Kumbukirani kuti mtsogoleri wamphamvu kwambiri mwa onse ndi Yesu Khristu. Yambani mwasanthula kaye moyo wake popeza kuti Iyeyo ndi chitsanzo chabwino cha utsogoleri wapambana.

Mukasankha munthu wakuti musanthule, musasokonekere ndi maina. Mwachitsanzo, m’Baibulo mu a Zakariya okwana 330, a Natani 20, a Yonatani 15, a Yudasi 8, a Mariya 7, a Yakobo 5 ndipo a Yohane 5. Onesetsani kuti mavesi onse omwe mukugwiritsa ntchito akukamba za munthu m’modzi yemweyo osati wina koma wa dzina lomwelo.

Anthu enaso ali ndi maina oposa limodzi. Mwachitsanzo, dzina la Yakobo linasinthika kukhala Israel komanso Abram anakhala Abrahamu. Mu Chipangano Chatsopano, Saulo anasinthika kukhala Paulo.

### **GAWO 2: PEZANI NKHANI ZONSE ZA MUNTHUYO**

Werengani zonse zomwe Baibulo likukamba za munthu ameneyo. Ngati muli ndi mabuku ena oti atha kukuthandizani koma ngati mulibe mugwiritse ntchito ndime zochitira umboni kuti mupeze nkhani zonse. Lembani ndime zonse zochitira umboni pa nkhani ya munthuyo ndipo werengani kapena kusanthula iriyonse payokha payokha.

### **GAWO 3: UNIKANI NKHANI ZOMWE MWAPEZA**

Zomwe mukuyenera kupeza posanthula nkhani ya munthu ziri m'musimu. Mwina Baibulo silikhala ndi china chirichonse cha zomwe talembazi komabe yesesa kupeza zomwe Baibulo liri nazo zokhuza munthu yemwe mukusanthulayo. Onani zinthu izi pamene mukusanthula moyo wa munthu m'Baibulo:

1. Dzina ndi tanthauzo lake lomwe.
2. Achibale a munthuyo: makolo kapena azigogo ake, abale ndi alongo ake.
3. Kubadwa: malo obadwira, kufunika kwa kubadwa kwake, zochitika zachilendo pa kabadwidwe kake.
4. Umwana wake ndi momwe anakulira.
5. Chilengedwe cha malo obadwira: Kodi nkhani ya munthuyu inachitikira kudera lanji?
6. Abwenzi ndi ogwira nawo ntchito, maubwenzi apadera.
7. Ntchito ya munthu: kodi amagwira ntchito yanji munthuyu? Kodi thandizo la ndalama amalipeza motani?
8. Kafotokozeredwe ka maonekedwe ake akuthupi.
9. Makhalidwe osilirika kapena utsogoleri omwe munthuyi akuonetsa kuti anali nawo.
10. Makhalidwe osasilirika kapena utsogoleri woipa wa munthuyu.
11. Zochitika zofunikira:
  - a. Kukumana ndi Mulungu koyamba.
  - b. Kutembenuka mtima
  - c. Maitanidwe
12. Nthawi yofunikira kwambiri pa moyo wa munthuyu.
13. Momwe anambanira ngati mtsogoleri. Kodi chinapangitsa kuti apambane ndi chiyani?
14. Momwe analepherera ngati mtsogoleri. Kodi chinapangitsa kuti alephere ngati mtsogoleri ndi chiyani?
15. Imfa: Kodi anafera kuti? Anafa motani? Zochitika zachilendo.

### **GAWO 4: GWIRITSANI NTCHITO ZOMWE MWAPHUNZIRA.**

Gwiritsani ntchito zinthu zomwe mwaphunzira mwa munthuyu m'moyo wanu:

1. Kodi ndi makhalidwe okoma ati omwe anali nawo ngati utsogoleri? Pemphani Mulungu kuti akuthandizeni kukhala ndi makhalidwe otero ngati mtsogoleri.
2. Kodi ndi makhalidwe oipa ati omwe anali nawo ngati mtsogoleri. Kodi mukuona ena mwa makhalidwe amenewa m'moyo wanu? Pemphani Mulungu kuti akuthandizeni kuwagonjetsa.
3. Kodi munthuyu anapambana mu njira yanji ngati mtsogoleri. Kodi mungagwiritse ntchito mfundo zimene iyeyu anagwiritsa ntchito kuti nanunso mupambane?
4. Kodi munthuyu analephera mu njira yanji? Kodi mabvuto amenewa inunso muli nawo? Kodi mungatani kuti musinthe?

5. Lemphani mfundo imodzi yomwe mwaphunzira kuchokera kwa munthu ameneyu. Mwachitsanzo, m'moyo wa Solomoni mutha kulemba kuti, “Kulekerera mu zinthu zauzimu kumagwetsa munthu.”

## **CHITSANZO: KUSANTHULA MOYO WA MUNTHU WA M'BAIBULO**

### **GAWO 1: KUSANKHA MUNTHU WOTI TISANTHULE**

Mfumu Sauli

### **GAWO 2: KUPEZA NKHANI ZONSE ZA MUNTHUYO**

Nkhani ya Mfumu Sauli imapezeka mu 1 Samuel 19 mpaka 31. Nkhani zonse zichokera mu machapatula amenewa.

### **GAWO 3: KUUNIKA NKHANIZO**

1. Dzina ndi tanthauzo: Sauli kuthanthauza kuti, “Wopemphedwa kwa Mulungu.” 1 Samuel 9:2
2. Achibale: (1 Samuel 9:1; 14:49-50)
3. Kubadwa: Baibulo silitipatsira malo ndi zomwe zinachitika pobadwa.
4. Umwana wake: amadyetsa abulu a bamboo ake.
5. Dera: Yuda
6. Abwenzi ndi anthu ena odziwana nawo: (1 Samuel 10:27; 14:50. Davide anakhala wogwira ntchito ndi Sauli. Poyamba amagwirizana kenako anamuchitira nsanje ndipo ubwenzi wawo unasokonokera (1 Samuel 18:69). Pamene Sauli anangoyamba kumene ufumu anali ndi gulu la ankhondo omwe “anakhudza mtima wa Mulungu” pamene anayamba kuonjezera amuna a zitho popanda chitsogozo cha Mulungu, mavuto ake anayamba (1 Samuel 10:26; 13:2; 14:52.
7. Ntchito ya Sauli: Mfumu yoyamba ya Israel
8. Kafotokozeredwe ka maonekedwe ake: Anali wantali kuposa aliyense komanso wokongola (1 Samuel 9:2; 10:23)
9. Makhalidwe abwino autsogoleri:
  - a. Amakhudzika ndi banja lake (9:5)
  - b. Wokoma mtima (9:2; 10:24)
  - c. Analola kusinthika ndi mzimu (10:6; 11:6)
  - d. Anakana kubwezera (chaputala 11)
  - e. Anatsogolera anthu (chaputala 11)
  - f. Munthu wakhama (chaputala 11)
  - g. Anali womvera poyamba (9:27)
  - h. Pafupi ndi Mulungu (10:26; 11:7)
  - i. Wolimba mtima (10:6)
  - j. Poyamba anali wodzichepetsa (9:21)
10. Makhalidwe oyipa pa utsogoleri
  - a. Anachita zooneka zoyenera m'malo momvera Mulungu: (13:8-13)

- b. Sanamvere ndipo ananama, naloza chala anthu ena: (chaputala 15)
  - c. Anakwiyitsa anthu a Mulungu: (15:35)
  - d. Amakhuzidwa kwambiri ndi zokamba za anthu osati Mulungu (15:30)
  - e. Anafuna kukhala pafupi ndi amuna ankhondo osati omwe anali ndi mitima yokhuzidwa ndi Mulungu. (10:26; 14:52)
  - f. Wamantha: (17:11)
  - g. Anachita zinthu moona ndi maso (17:33)
  - h. Anadalira zida za kuthupi (17:38)
  - i. Wansanje (18:6-9)
  - j. Mzimu woyipa: (18:10)
  - k. Mzimu wofuna kubwezera (18:11)
  - l. Anafuna kupha munthu wa Mulungu: (18:20-30)
11. Zochitika zofunikira:
- a. Kukumana ndi Mulungu koyamba: 1 Samuel 9:15-27)
  - b. Conversion: 10:9
  - c. Kuitanidwa ku maitanidwe: 10:1
12. Nthawi yofunika kuyidziwa: Pamene sanamvere Mulungu ndipo ufumu unachotsedwa kwa iye. (chaputala 13)
13. Imfa: Sauli anafera m’manja mwake momwe. Ana ake awiri, wonyamula zida wake, pamodzi ndi amuna onse anafa tsiku limodzi ku Phiri la Giboa pa nkhondo ndi Afilisti (chaputala 31)

#### **GAWO 4: KUGWIRITSA NTCHITO ZOMWE MWAPHUNZIRA**

Makhalidwe okoma autsoholeri omwe Sauli anali nawo ndipo ndikuyenera kukhala nawo m’oyo wanga:

Pamene Mzimu wa Mulungu ubwera pa munthu, munthuyo sakhalanso chimodzimodzi. Amasinthika nakhala munthu “watsopano.” (10:6) Ndikuyenera kufunafuna kudzodza kotereku.

Makhalidwe oyipa pa utsogoleri omwe Sauli anali nawo ndipo ndikuyenera kuwapewa m’oyo wanga:

Mulungu amafuna atsogoleri a pantima pake: (13:14). Ngakhale Sauli sanachite bwino pa gawo limeneli, ndikufuna nditakhala mtsogoleri wa pantima pa Mulungu.

Kusamvera: Kuchita zinthu zooneka zoyenera komanso zachidule koma ziri zosemphana ndi chifuniro cha Mulungu.

Kuloza anthu ena chala pa uchimo wake.

Kulabadira kwambiri zomwe za anthu akuganiza pa ine osati zomwe Mulungu akuganiza pa ine.

Ndingachite bwino kwambiri nditaunika makhalidwe onse a Sauli ndi kusanthula mtima wanga nthawi ndi nthawi kuti ndisakhale ngati iyeyo.

Maitanidwe a Mulungu pa Sauli anali oti atsogolere ngati wamkulu wa nkondo wa Israel: (10:1). Koma anthu anampanga iye kukhala mfumu (12:12-15; 10:24). Mulungu ndi amene amayenera kukhala mfumu ya Israel. Ndikuyenera kusamala ndi matamandidwe a anthu kuti ndisachoke m'dongosolo la Mulungu pa moyo wanga ndi kundipanga kukhala chimene Mulungu sakufuna kuti ndikhale.

Ngakhale Mulungu anali naye Sauli poyamba, koma mapeto ake anamulanda ufumu. Ndi bwino kwambiri kuzindikira kuti ngakhale Sauli anali atachimwa komanso anali atankhula mwa mneneri za kutha kwa ufumu wake, kudzodza kwa Mulungu kunali kudakali pa iye (14:47). Maitanidwe ndi mphatso za Mulungu sizilapika. Sauli ankamvabe liu la Mulungu (15:1) ndipo anampembedza (15:31) koma anali ndi tchimo losapa nataya ufumu wake. Davide anazindikira za kuopsa kokhudza munthu amene Mulungu anamdzodza kukhala mtsogoleri. Ndikuyenera kutengerapo phunziro.

Phunziro lalikuru kuchokera m'moyo wa Sauli: Zotsatira za kusamvera Mulungu. Ndipo phunziroli liri mu ndime yakuti, “Kumvera kuposa nsembe yopsereza ndi nyama za mafuta” (15:22). Davide analankhula nati, “Amphamvu agweranji?” (2 Samuel 1:19).

Gwiritsani ntchito ndondomeko yomweyi posanthula za moyo wa munthu.

## MAYANKHO A MAFUNSO ODZIYESA NOKHA

### CHAPUTALA 1:

1. Mauwa ali okhulupirika, ngati munthu akhumba udindo wa woyang'anira, aifuna nchito yabwino. 1 Timoteyo 3:1
2. Mau ena a “kuyendetsa zinthu” ndi kukhala “mdindo.” Adindo kapena oyang'anira amayang'anira zomwe anthu ena awaikiza. Ndipo ndi ndondomeko yokwaniritsira madongosolo a Mulungu ndi zolinga zake kudzera mwa anthu, zipangizo, ndipo chuma cha uzimu. Kuchita bwino kumaoneka pamene zolinga ndi madongosolo a Mulungu akwaniritsidwa.
3. Chumachi ndi Uthenga Wabwino, ndalama, zipangizo za mu utumiki, mphatso zauzimu, komanso okhulupirira ena.
4. Kukhulupirika
5. Yesu Khristu
6. Yerekezani ndemanga yanu ndi yomwe yaperekedwa mu Chaputala 1.
7. Yerekezani yankho lanu ndi ndemanga ya mu Chaputala 1.

### CHAPUTALA 2.

1. Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; (Aefeso 4:11)
2. 2, 1, 3, 5, 6, 7
3. a. Akulu a mpingo  
b. Atumiki  
c. Oyang'anira

### CHAPUTALA 3

1. Koma munakweza nyanga yanga ngati ya njati; Anandidzoza mafuta atsopano. (Masalimo 92:10)
2. “Kudzodza” ndiko kupatula kapena kuyeretsa chinthu mwa kupaka mafuta.
3. Mafuta ndi chizindikiro cha Mzimu Woyera. Ndipo pamene munthu wadzodzedwa ndi mafuta ndi chizindikiro cha Mzimu Woyera kubwera pa iye kukagwira ntchito ina yake.
4. Kudzodza kwa wakhate – maubale; kwa wansembe – chihero; kwa mtsogoleri – ulamuliro ndi mphamvu.
5. Mulungu ndiye gwero la kudzodza kwa utumiki.
6. Kudzodza kumakupanga kukhazikika pa malo omwe Mulungu wakuikani, kukupatsani kuthekera kokwaniritsa dongosolo la Mulungu, kukupatsani nzeru pa utsogoleri, kuphwanya magoli a iwo omwe mukuwatumikira.
7. Mulungu akamadzodza munthu sayang'ana maphunziro, nzeru, maluso, kapena kudziwa. Amayang'ana mtima.
8. Mphamvu za mdima zimafuna kukutchingani kuti musayende mkudzodza popeza zimadziwa kuti kudzodza kumakwaniritsa zolinga za Mulungu.
9. Pakuyendabe m'magawo atatu a kudzodza omwe aperekedwa m'phunziro lino.

## **CHAPUTALA 4**

1. Pakuti ife ndife cipango cace, olengedwa mwa Kristu Yesu, kucita nchito zabwino, zimene Mulungu anazipangiratu, kuti tikayende m'menemo. (Aefeso 2:10)
2. Zoyenereza si maluso obadwa nawo. Koma makhalidwe ake a munthu molingana ndi momwe Mau a Mulungu akufotokozera kuti mtsogoleri akhale nawo. Amaonekera kudzera m'moyo wa Umulungu.
3. Chipatso cha ulaliki ndiko kukhala mboni yamphamvu ya Uthenga Wabwino.
4. Onani mndandanda wa makhalidwe ofanana ndi Khristu omwe aperekedwa mu Chaputala 4.
5. 9, 7, 8, 5, 6, 2, 4, 3, 1.
6. Ndimezo ndi 1 Timoteyo 3 ndi Tito 1
7. Akhale obadwanso mwatsopano, obatizidwa ndi Mzimu Woyera, okhala ndi maitanidwe a paderadera ochokera kwa Mulungu kuti akhale mtsogoleri, ndi kukhala okhwima muuzimu.

## **CHAPUTALA 5.**

1. Mukhale nao mtima m'kati mwanu umene unalinso mwa Kristu Yesu, ameneyo, pokhala nao maonekedwe a Mulungu, sanaciyesa colanda kukhala wofana ndi Mulungu, koma anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe akapolo, nakhala m'mafanizidwe a anthu; (Afilipi 2:5-7)
2. Utsogoleri wotumikira
3. Yesu Khristu
4. Mphamvu ya utsogoleri wotumikira ndiyakuti imamchepetsa munthu kufika pa mlingo wakuti Mulungu atha kumugwiritsa ntchito bwino ntchito. Izi zinaonekera m'moyo wa Yesu Khristu.
5. Atsogoleri a dziko amakhala ndi ulamuliro pa owatsatira ndipo amakhala monga mabwana awo.
6. Timatumikira Thupi la Khristu komanso dziko lotayika ndi lakufa. Komano utumiki wathu ndi wa kwa Ambuye.
7. Yerekezani kufotokozera kwanu ndi kukambirana kwa mu Chaputala 5.

## **CHAPUTALA 6.**

1. (1 Petro 5:23)
2. Yesu Khristu
3. Okhulupirira onse mwa Khristu ali gawo limodzi la gulu la nkhusa.
4. Yerekezani yankho lanu ndi zokambirana za mu Chaputala 6.
5. Yerekezani yankho lani ndi zokambirana za mu Chaputala 6.

## **CHAPUTALA 7**

1. Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi enaaneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; kuti akonzere oyera mtima: ku nchito ya utumiki, kumangirira thupi la Kristu; (Aefeso 4:11-12)

2. Kukonzekeretsa okhulupirira ku ntchito ya utumiki.
3. Kukonzekeretsedwa kwa okhulupirira ndiko kusula ophunzira kukachita ntchito ya utumiki. Izi ndi monga kuphunzitsa, kulalikira, kuonetsera, kusula ndi kukusa.
4. Zotsatira za kukonzekeretsa okhulupirira ku utumiki nazi:
  - a. Ntchito ya utumiki imachitika: Aefeso 4:12
  - b. Thupi la Khristu (mpingo) limalimbikitsidwa (kumangalirika) Aefeso 4:12
  - c. Anthu amakula muuzimu: Aefeso 4:13-15
  - d. Umodzi umakhalapo: Aefeso 4:13
  - e. Anthu amaumbika mchikhalidwe cha Khristu: Aefeso 4:13
  - f. Anthu amazama ndi kukhazikika m'choonadi: Aefeso 4:15-16
  - g. Thupi la Khristu limagwira bwino ntchito: Aefeso 4:16
5. Yerekezani yankho lanu ndi zokambirana za mu Chaputala 7.

## CHAPUTALA 8

1. Mtima wa munthu ulingalira njira yace; Koma Yehova ayendetsa mapazi ace. (Miyambo 16:9)
2. Njira ya m'Baibulo si yamavoti kapena kukweza manja. Mulungu amaika atsogoleri mu mpingo kuti akapange ziganizo.
3. Yerekezani yankho lanu mlozo womwe waperekedwa mu Chaputala 8.
4. Njira ya chitsanzo yopangira ziganizo ndi chitsanzo choyenera kutsatira pamene mupanga ziganizo.
5. Ndipo chithunzithuzichi ndi chitsanzo chabwino choyenera kutsatira.

## CHAPUTALA 9

1. Ndipo pobvomerezeka, cinsinsi ca kucitira Mulungu ulemu ncacikuru: iye amene anaonekera m'thupi, anayesedwa wolungama mumzimu, anapenyeka ndi angelo, analalikidwa mwa amitundu, wokhulupiridwa m'dziko lapansi, wolandiridwa m'ulemerero. (1 Timoteyo 3:16-17)
2. Yerekezani ndemanga yanu ndi yomwe yaperekedwa mu Chaputala 9
3. Yerekezani ndemanga yanu ndi yomwe yaperekedwa mu Chaputala 9
4. Yerekezani mndandanda wa zifukwa zanu ndi womwe zaperekedwa mu Chaputala 9
5. Yerekezani ndemanga yanu ndi yomwe yaperekedwa mu Chaputala 9.
6. Chifukwa cha Akhristu osakhwima muuzimu, otsogozedwa ndi Satana, thupi, ndi kudzikuzi.
7. Tikasungitsa mwambo komanso kuthana ndi mikangano pogwiritsa ntchito Mau a Mulungu, anthu amakonzekeretsedwa ku ntchito ya utumiki. Mau a Mulungu ndi a mphamvu kusungitsa mwambo, kudzudzula, komanso kuwongolera.

## CHAPUTALA 10

1. Wophunzira saposi mphunzitsi wace; koma yense, m'mene atakonzedwa mtima, adzafanana ndi mphunzitsi wace. (Luka 6:40)



2. Kusula ena ndi udindo wofunikira kwambiri chifukwa amene umawaphunzitsa amadzasanduka iwe mwini.
3. Timaphunzitsa atsogoleri ndi otsatira ndi cholinga chopita ku maiko onse kukafalitsa Uthenga Wabwino, kuwabatiza, ndi kuwatsogolera ku kukula muuzimu kudzera nkuphunzitsanso kwa ena.
4.
  - a. Kudalira pa Mulungu.
  - b. Chipangeni kukhala nkhani ya pemphero
  - c. Muchitepo kanthu
  - d. Onani mwayi womwe ulipo osati mavuto
  - e. Auzeni anthu momveka bwino za dipo lomwe liripo
  - f. Sankhani iwo amene ali ndi zowayenereza zofunikira.
5.
  - a. Kukhala pamodzi.
  - b. Kupereka malangizo
  - c. Kuonetsera
  - d. Kupatula
  - e. Kutenga nawo mbali
  - f. Masomphenya
  - g. Kuyang'anira
  - h. Kugawira ntchito
6. Njira ya kwa Aefeso

## **CHAPUTALA 11**

1. Pakuti wolungama amagwa kasanu ndi kawiri, nanyamukanso; Koma oipa akhumudwa pomfikira tsoka. (Miyambo 24:16)
2. Kuti mupeze mndandanda wa iwo amene anasanduliza kulephera kukhala chipambano onani zokambirana za mu Chaputala 11.
3. Kuti mupeze mndandanda wa iwo amene miyoyo yawo inathera nkulephera onani kukambirana komwe kunachitika mu Chaputala 11.
4.
  - a. Kubvumbulutsa
  - b. Kulapa
  - c. Kubwerera
  - d. Kubwezeretsedwa
5. Kulephera kwa maubwenzi komanso chifukwa cha tchimo lochita ndi losachita

## **CHAPUTALA 12.**

1. Buku ili la cilamulo lisacoke pakamwa pako; koma ulingiriremo usana ndi usiku, kuti usamalire kucita monga mwa zonse zolembedwamo; popeza ukatero udzakometsa njira yako, nudzacita mwanzeru. (Yoswa 1:8)
2. Mu Ufumu wa Mulungu, kupambana kumabwera pamene munthu watha kugwiritsa bwino ntchito mphatso ndi kuthekera konse kumene Mulungu anampatsa. Ngati mukugwiritsa bwino ntchito zinthu zauzimu ndiye kuti ndinu opambana mu utsogoleri.
3. Yerekezani kufotokozerani kwanu ndi kukambirana kwa mu Chaputala 12.
4. Yerekezani ndemanga yanu ndi kukambirana komwe kulipo mu Chaputala 12.

## **CHAPUTALA 13**

1. Pomwepo Yesu anati kwa ophunzira ace, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikane yekha, natenge mtanda wace, nanditsate Ine. (Mateyu 16:24)
2. Magawo atatu ofunikira a dipo la utsogoleri amadziwika kuti dipo, kudziwa zinthu zofunikira, ndi zolinga zabwino
3. Utsogoleri wanu umaonekera pamene inuyo palibe. Kodi anthu akukhulupirika kuchita zomwe mwawaphunzitsa? Kodi akuphunzitsa amnzawo zomwe aphunzirazo? Kodi atha kupirira kukula muuzimu ngakhale inuyo palibe.